


M'BADWO WA MPINGO

WA LAODIKAYA

 Tsopano, iye sanamalize konse izo. Ine ndinati, “Ine ndinachedwa pa ukwati wanga...Ndinabadwa mochedwerapo pang’ono, ndinachedwerapo pang’ono pa ukwati wanga, ngati ine ndingadzakhoze kungochedwa pa maliro anga!” Apo ndi pamene ine ndikufuna kwenikweni kuti ndidzachedwepo, ndidzachedwe kwenikweni.

² Ayi, anali mafoni kunyumba, ine ndimalephera kuti ndichokeko, nkomwe. Ndiyeno mkazi wanga ndi iwo atanyamuka mofulumira, ine ndinali basi ndi zinthu zochuluka kwambiri. Ndiyeno anthu mmalo osiyanasiyana, akupemphera, ndipo basi tsopano akulowa mkati; ndipo vumbulutso la Ambuye linabwera kwa m’bale; mlongo wayima kumbuyo uko, akudwala; inu mukudziwa zimene ine ndikutanthauza, ndizo basi pita, pita, pita, pita. Ndipo ine sindinathe ngakhale kugwirana chanza ndi ena mwa amzanga kuno ochokera ku Georgia ndi malo osiyanasiyana konse kozungulira, uko ku Canada. Ine ndikungomverera moyipa kwambiri kuti sindinathe kukugwirani chanza.

³ Ndipo, ndisanayiwale, Fred ali kuti usikuuno, Fred Sothmann? Fred, iwe ukukumbukira nthawi ija imene iwe unandiyimbira foni kuchokera ku Canada, unali kubwera kuno, ndipo ine ndinakuwuzwa iwe kuti usabwere pa galimoto? Iwe unabwera, mulimonse; anali ndi ngozi, monga...anaphwanya galimoto yake, ngati kuti ikanamupha mkazi wake, banja, anathyola mphuno yake, ndipo anakawagoneka onsewo mu chipatala.

⁴ Kanthawi kapitako pamene ine ndimachoka, masana womwewo, M’bale Ben apa anali atayima kunja uko, anabwera molunjika kwa ine. Ndipo Rosella anabwera kumeneko, iye anati, “Ine ndikupita kwathu.”

Ine ndinati, “Rosella!”

Iye anati, “Chavuta ndi chiyani, M’bale Branham?”

Ine ndinati, “Ine ndikumverera mwachilendo kwenikweni za izo.” Mukuwona?

Anati, “Chichitika chirichonse?”

Ine ndinati, “Ine sindikudziwa. Izo zikuwoneka kwa ine, Chinachake chandichenjeza ine.”

⁵ Iye anandiimbira ine maminiti angapo apitawo, iye anachita ngozi. Ndipo chotero, palibe amene anavulala, koma ilo

linali dzanja la Ambuye. Ndipo iye amatsetsereka (Ndi konse kwachisanu Kumpoto.) ndipo iye anaterereka pa Indianapolis, ndipo anayamba kutsetsereka chopingasa msewu mwaliwiro kwambiri mbali *iyi*. Ndipo iye anafuula mokweza, “O Ambuye, ndithandizeni ine!” Galimotoyo inapotokeza mmbuyo mbali *iyi* kenanso, inabwereranso ndipo inakalowa mbali yake yolondola, ndikuyamba kumapita bwinobwino. Iye anapita pamwamba pa msewu, iye anati, “Mai, mai, ndine wothokoza bwanji kuti ndituluke mu zimenezo, chifukwa magalimoto ena akubwera mkanjira komweko, akungowuluka.” Chotero iye anangowoloka msewu, ndipo kenako iye anakayima pamenepo kumapita kuti. . . Ine ndikukhulupirira, chinachake, iye anayima kuti akapeze kapu yake ya khofi kapena chinachake. Ndipo basi iye asanatuluke mgalimoto imeneyo, galimoto ina inadzamuwomba iye kumbuyo kwake, ina pomwepo kumbuyo kwake, ina pomwepo kumbuyo kwake, ndipo pamenepo onse iwo anadzawunjikana. Koma anati iye anamenyetseka pang’ono, koma osati moyipa, koma iye amafuna kumuthokoza Ambuye, ndi kuyimba ndi kuwuuza mpingo kuti umuthokoze Ambuye kuti iye sanavulale kapena chirichonse, ndipo anapempha mpingo kuti upitirize kupemphera kuti iye akafike kunyumba. Mwawona, iye ndi dalaivala watsopano, iye wangopeza kumene laisensi yake. Chotero, ndine wothokoza kwambiri.

⁶ Koma nthawizonse zimathandiza kutenga machenjezo amenewo a Ambuye. Anati, “Chabwino,” iye anati, “Ine ndikhoza kuphonya ntchito ya tsiku limodzi.” Ntchito ya tsiku limodzi ndi chiyani? Mtengo wake ndi woposa kukonzanso kumbuyo kwa galimotoyo, mwawona. Chotero ndi zopambana ku—kukupangitsani inu. . . kukhala ndi Ambuye. Kodi si kulondola uko? Ngati Iye atiuza ife chirichonse, ife kulibwino tikhale ndi Icho. Chifukwa Iye nthawizonse amakhala wolondola. Sichoncho Iye? Nthawizonse wolondola!

⁷ Tsopano, oh, *iyi* ndi yotero. . . yakhala sabata yodabwitsa chotero. Ine basi sindikudziwa momwe ine ndingadzifotokozere ndekha kwa Mulungu ndi kwa inu anthu chifukwa cha sabata yabwino *iyi*. Awa akhala ena a masiku eyiti osangalala kwambiri omwe ine ndinayamba ndalalikirapo mmoyo wanga. Izo ndi zoon. Ine nda—ine ndaphunzira zochuluka kwambiri za Ambuye ndi chifundo Chake chokoma, ndi zonse zomwe Iye wachita kwa ife, ndi kuwona Mzimu Wake ukugwiranso ntchito mu mpingo. Ndipo ndine wokondwa kwambiri kuziwona mphatso zikuyambiranso kugwira ntchito mu mpingo. Mukuwona?

⁸ Tsopano, ukangokhalapo, pamene iwe wachoka, izo zimangowoneka ngati kuti wina alowamo kwenikweni, adzango—adzangoyipitsa iwo, inu mukudziwa, iwo angoyamba kuchita chirichonse. Ndipo pamene inu simulemekeza mphatso zimenezo, Mulungu sadzakulemekezani inu. Mukuwona? Uko

nkulondola. Inu mukuyenera kuzipanga izo kukhala zolondola. Ndipo, momwe ife timazifunira izo ndi basi pamene izo ziri mu dongosolo, mmene iwo akuyankhulira ndi malirime. Osati kumangobwereza Lemba, koma kunena chinachake chimene chikukonzekera kuti chichitike. Ndipo ngati inu mungokhalabe olemekeza kwenikweni ndi zimenezo, izo zidzayamba. . . Ngati aliyense achoka mu dongosolo mu mpingo, Mzimu Woyera udzaziyankhula izo momveka ndi kuwauza iwo yemwe iye ali. Ndipo pameneno, iwo adza—iwo adzamverera kudzudzulidwa ndipo adzapita ku guwa. Ndi chimene mphatsozo zinadzera.

⁹ Ndipo kumuwona m'busa wathu pano, M'bale Neville, iye anali wamanyazi, mnyamata wamtundu wachikale. Ndipo ine ndikukuuzani inu, iye anali. . . iye ankawoneka ngati iye sadzazigwiritsitsa izo pamene izo zidzafika pa Pentekoste. Koma kumuwona iye akuyimirira ndi kutanthauzira malirime ndi kumanenera, ine ndikukuuzani inu, iye wachokera kutali. Kulondola. Tiyeni tiziwapempherera abusa athu.

¹⁰ Ndipo, mukuona, mphatso zimayamba kubwera mu tchalitchi. Ndipo m'bale wina wamng'ono, wodzichepetsa pano, iye ali pano, iye ndi. . . akuyenera kukhala pano penapake. Ine ndikuganiza iye ali, iye nthawizonse amakhala alipo. Iye ndi munthu wodzichepetsa kwambiri, anali mmodzi wa matrastii pano pa tchalitchi, M'bale Higginbotham, munthu wofunika, munthu waumulungu. Ndipo kuwona kuti iye walandira mphatso yolankhula mmalirime, ndani akanaganizira kuti M'bale Higginbotham akanachita konse zimenezo? Wamanyazi, munthu wamng'ono wachikale, sankafuna kuti azidziwika, ndi kulikonse, amakhala kumbuyo. Koma, mwawona, Mulungu akhoza kumutenga munthu wonga ameneyo ndi kumugwiritsa iye ntchito, mwawona, chifukwa iye sakufuna kuti achite zimenezo, kuyamba ndi kuyamba. Ngati iye akanafuna kuti azichita zimenezo, iye akanakhoza kukhala wodzikuza. Koma pokhapokha ngati iye akutulukira kumene iye sakufuna kuchita izo, mwinamwake Mulungu akhoza kumugwiritsa iye ntchito monga choncho.

¹¹ Junie ali pano, ali. . . oh, iye ali kuseri kwa chipilalachi kuchokera kwa ine.

¹² Ine ndinena izi, ine ndamvapo anthu ambiri akuyankhula mmalirime. Ndipo ine ndikuganiza izo zonse zimachokera kwa Mulungu, chifukwa iwe sungakhoze kupanga phokoso popanda ilo kutanthawuza chinachake kwa winawake, kwina wake. Inu mukudziwa, Baibulo limati, "Sipamakhala phokoso lopanda kufunikira," kutanthauza kuti sipamakhala phokoso popanda ilo kutanthauza chinachake. Inu simungathe kupamanga mtundu uliwonse wa kuyankhula pokhapokha izo zikutanthauza chinachake. Ine nthawi zambiri ndinkadabwa kuti zingatheke bwanji mpaka ine nditadzapita ku Africa ndi kukamva maphokoso onse awo, ndipo ine ndinadzapeza

pamenepo kuti linali liwu la winawake. Nthawizina limakhala liwu laungelo, ndi zina zotero.

¹³ Koma Junie Jackson, wamanyazi, wachikale, wamantha pang'ono, mlaliki wakumidzi kunja uko wa mpingo wa Methodist, uko kumusi—kumusi mkati kuzungulira Elizabeth, Indiana, kumbuyo komwe mu nkhalango zammbuyo. Wachete, samanena kalikonse, wokhala ngati wachikale, amawoneka ngati iye... Ine ndimawona nthawizina, ine ndikufuna ndidzamtenga iye, kudzamugwira chanza iye, ndikuti, “Tanena chinachake, Junie, wawona, ingosiya kukhala pamenepo ndikumandiyang'ana ine monga choncho.”

¹⁴ Ife timatha kukhala pansu pa chitsa mu nkhalango, ndipo iye amatha kukhala pamenepo ndi kuti, “Chabwino, ... ine ndikuganiza ... izo ziri bwino.”

¹⁵ Ine ndimatha kunena, “Oh, Junie, ine—ine ndikumverera ngati 'ndilole ine ndinene izo mmalo mwako,' inu mwawona. Ndiwe—ndiwe wochedwa kwambiri kwa ine, mwawona.” Ndipo Mulungu anampatsa iye a—a—mphatso yolankhula mmalirime; ine sindinamvepo chinenero china chomveka bwino mmoyo wanga wonse. Mukuwona?

¹⁶ Kumuwona Iye mu tchalitchi. Kumuwona mkazi wamng'ono uyo akuyankhula mmawa uno osati nkumudziwa mkazi winayo? Ndipo mmodziyo wosamudziwa winayo, ndipo uyu, kamvekedwe ka liwu limene linayankhulidwa; ndipo pamene ilo linatanthauziridwa, mu kamvekedwe komweko, malemba aliwu, zizindikiro; chimodzimodzi basi, kubwereranso. Ndipo uthengawo unali wangwiro, kwa mpingo. Mukuwona momwe izo zikukhalira? Tsopano, ife tiyenera kumuthokoza Mulungu. Tsopano, musati mutulutse chidale chanu kunja. Ngati inu mutero, inu mudziphwetsa nokha, ndipo mdierekezi adzakugwirani inu. Mungokhala odzichepetsa; ndikuti, “O Ambuye, ndibiseni ine mmbuyo, musadzandilole ine kuti ndidzadzuke nthawi isanakwane.”

¹⁷ Iye sadzakulolani inu kuti mudzachoke mu dongosolo. Ngati inu mutero, nthawiyina, izo sizidzakhala—izo sizidzakhala ndi ntchito. Ngati inu mutero, bwanji, abusa pano adza—adzakuuzani inu. Mwawona, mpha—mphatso siziri zoti zikhalepo pamene inu muli... pamene ife tikulalikira. Kawirikawiri, ngati mphatso zidzayamba kugwira bwino ntchito mu mpingo, ife tizidzakulolani inu kuti muzikumana nthawi yayitali msonkhano wina usanayambike; kulola Ambuye kuti agwire nanu ntchito pamenepo, inu mukuwona, chifukwa ndiye pagawo ili izo sizidasokoneza izo konse. Tsopano, pamene ife tiri mwa osonkhana, nthawizina inu mumayenera kukhala chete pang'ono. Koma ngati Mulungu ali ndi uthenga, kwinakwake kapena kwina Iye adzawubweretsa iwo, mwaona, basi kungomusiya Iye yekha, koma muzichita izo molingana ndi

kuphunzitsa kwa Baibulo. Ndipo M'bale Neville mwinamwake akhala akuphunzitsa pa zinthu zimenezo, zimene ife tidzayesere kuti tizizichita. Ine ndiyesetsa kuthandizana naye limodzi momwe ife tingathere, tonse awiri pamodzi, kuti tizibweretse izo ndi kukuwonetsani inu momwe izo zingagwiritsidwire ntchito.

¹⁸ Inu mukumverera bwino, m'bale wanga waku Poland? Izo nzabwino. Oh, momwe Ambuye anamudalitsira iye! Zaka eyiti zapitazo, ndinamuza iye kuti chinachake chikanati chichitike. Iye anali yense wosokonezeka, weniweni wautatu wosamalitsa. Ndipo Ambuye ananena, tsiku lina, "Pali munthu amene akubwera, iye ali ndi tsitsi lakuda ndi maso abulauni, wojintcha. Usati umubweze iye, Ine ndikumutumiza iye kwa iwe." Ine ndinatenga Lemba basi pomwepo pamene iye anasokonezekapo, ndinaikapo pamenepo kachidutswa ka pepala ndipo ndinakasiya pamenepo. Patapita kanthawi apa iye anabwera.

Mkazi wanga anati, "Kuli bambo kunja uko kuti akuwoneni inu."

Ine ndinati, "Ndi ameneyo, mubweretse iye muno."

¹⁹ Ndipo iye—iye anandiuza ine zomwe zinanenedwa kwa iye...pansi pa kudzoza kwa Mzimu Woyera. Momwe iye nthawizonse ankakhulupirira ndi kugwiritsitsa ku Uthenga, ndi zina zotero, pakati pa anthu ake; komabe akutsutsidwa, iye anakhalabe molondola ndi Iwo. Anati, nthawi ina kalelo, mu msonkhano, kuti ine ndinayankhula ndi iye ndipo ndinatchula dzina lake. Ndipo momwe ine ndinatchulira dzina limenero, ine sindikudziwa. Iye anati ine ndinachita ku—kulitchula ilo mzilembo, kapena chinachake kapena chimzake, mu msonkhano. Anati iye anali atanyamula mwana pa nkono wake yemwe anali ndi zotuluka pankhope pake, ndipo anati mwana wamng'onoyo anayeretsedwa kwathunthu, kwathunthu basi. Ndi momwe Ambuye...

²⁰ Ndipo ine ndinati, "Chabwino, chinthu chimene inu mukuchisowa tsopano ndi kupita kumusi ku tchalitchi ndi kukabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu."

²¹ Ine ndinakumana naye iye kanthawi kapitako pamwamba pa phiri, chifukwa iye anabwera pansu, anabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu. Tsopano iye yense ndi wokhutitsidwa, akumverera bwino, akubwerera kwawo. Ine ndikuyembekeza iye adzanditanthauzira ine ku Poland limodzi la masiku amenewa, ndi Germany, ndi mkati, kubwerera ku malo amenewo uko. Ambuye akudalitseni inu, m'bale wanga.

²² Zinthu zambiri zopambana zomwe Ambuye wathu amachita! Kungowona Chake—chifundo Chake, momwe chiriri kuchokera kummawa, kumadzulo, kumpoto, ndi kummwera,

Iye akuwatsogolera ana Ake okonedwa; kubwera pamodzi, kukokera kunja, kugwedezera pansi. Zambiri zoti zinedwe!

²³ Tsopano, musati muiwale, Lamlungu likubwerali usiku, Ambuye wathu akalola, Lamlungu likubwerali usiku, ife tidzakhala ndi...Lamlungu likubwerali mmawa, kani, msonkhano wamachiritso. Chifukwa chimene ine ndikunenera zimenezo pa izo, mwinamwake ndiye ngati alipo ochuluka kwambiri kwa Lamlungu mmawa ine ndidzakhala ndi Lamlungu usiku kuti ndidzabwererenso mmbuyo, inu mukuwona. Koma ngati ine ndingakhoze kudzawatengera onsewo kunja Lamlungu mmawa, chabwino, zabwino.

²⁴ Lachitatu usiku ndi msonkhano wa mapemphero wapakati pa sabata. Tsopano, kwa anthu inu omwe muli pano kuzungulira kwathu kuno, inu abwenzi mudzasonkhane muno, mudzakhale ndi msonkhano wa mapemphero. Musati mudzawuphonye iwo, mudzakhale nawo iwo, mukuwona. Ndipo mudzapemphere, mudzafunefune kukhala pafupi ndi Mulungu. Musadzalole kutentheka kudzakhale pakati panu. Muzisunga...Ziripo zenizeni zochuluka mwakuti simungavomereze zabodza, mwawona, musati—musati mudzikhala mbali yolakwika. Mudzikhala molondola.

²⁵ Ine ndinamva “Ameni” wodziwika bwino ndiye amene ine ndakhala ndikumumva kwa zaka, M’bale Russell Creech. Iwo anandiuza ine kuti Patty ndi amene anayankhula mmalirime kumbuyo uko usiku wina. Patty, iwe uli kuti? Iwe uli pano, wokonedwa? Eya, mai, ine sindikanamudziwa nkomwe iye ngati ndikanamuwona iye. Koma ine ndikukhulupirira ine ndinamugwira mwana ameneyo mmanja mwanga ndipo ndinamupereka iye kwa Ambuye, pomwe pano. “Ndipo ndi mtsikana,” Meda anati, “mtsikanana wamng’ono, wokongola, wausinkhu wammatini,” ndi mphamvu ya Mzimu Woyera pa iye, akuyankhula mu...Russell, iwe ndiwe munthu wolemera. Inde, ndiwe.

²⁶ Kodi Mlongo Creech ali kuti? Ine sindinamuwone iye. Kodi iye ali pano? Kumbuyo uko. Oh, Mlongo Creech, momwe ine ndiliri wothokoza kuti Mulungu wakupatsani inu mwana wonga ameneyo, bwanji, inu simukuzindikira momwe—momwe ndikuthokozera. Pa usinkhu umene atsikana a usinkhu wa mmatini amanyogodola ndi kumaseka ndi kumapitirira, inu mukudziwa, ndi mulu wa zamkutu kwa anyamata awa, kametedwe kawo ka abakha ndi chirichonse, ndipo monga choncho; ndipo mwana wamng’ono uyu pano ndi mphamvu ya Mzimu Woyera, akuyankhula mu malirime muno. Oh, mai!

²⁷ Hmm! Ndi amuna angati usikuuno, alaliki Achipentekoste, omwe angapereke moyo wawo wonse ngati atamuwona mwana wawo wamkazi wa usinkhu wammatini, amene ali kunja ku phwando la gwedemula, akuchita zimenezo.

28 Basi—muzingolemekeza zimenezo, m'bale. Ine ndikudziwa zimene inu mukuchita kumeneko ku Interstate, ine ndinachitanso chinthu chomwecho, ndinagwirapo ntchito masiku ambiri ovuta, koma, m'bale...kuti uwalere ana amenewo. Koma kumbukirani, Mulungu ndi wokhulupirika, Iye amapereka mphotho. Inde, ndithudi! “Ine ndidzabweza.”

29 Mulungu akudalitse iwe, Patty. Wokonedwa, ine—ine sindikanakudziwa iwe ngati ine ndikanakuwona iwe, ine ndikuganiza, koma usati udzasiye konse njira yowongoka imeneyo, wokonedwa. Usadzalole konse mdierekezi kuyika chirichonse—chirichonse mwa iwe, ngati apulo yabwino yagolide, chifukwa iyo idzakhala ndimu, mwawona. Chitaye chinthucho ndipo uchisiye icho monga choncho. Maso ako angokhala pomwepo pa Khristu, pa Mtanda pomwepo. Ndipo zipitirira kumasuntha, pakuti oralo layandikira. Mukuwona?

30 Zinthu zambiri zolimbikitsa zomwe ine ndikanakhoza kunena, madalitso a Mulungu. Ine sindinathe kuwayendera ambiri, ndipo sabata yonseyi ine sindinapempherere anthu opitirira fifite, ine ndikuganiza, ndi zolowa ndi zotuluka, ndi zadzidzidzi ndi zomwe zalowa, ndi zina zotero, koma ine ndakhala ndiri wotanganidwa kuphunzira. Koma tsopano, Lamlungu likubwerali, ife tidzakhala tikupempherera anthu, ndi kuwapempha Ambuye kuti abwere ndi kudzatipatsa ife mphamvu yayikulu, ndi kudzadziwonetsera Yekha kwa ife Lamlungu likubewerali mmawa, Ambuye akalola.

31 Oh, ine ndikungodana nazo kuti ndiyambe pa m'badwo wa mpingo uwu chifukwa ine ndikudziwa ndiwo wotsiriza wa iyo. Ndipo tsopano, mu izi, zikhala ku—kumalizitsa kwa Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo. Kodi inu mwasangalala nayo iyo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Tsopano, kumbukirani, ine ndikunena izi kumapeto monga ine ndinachitira pachiyambi, pakhoza kukhala zinthu zambiri, pakhoza kukhala zinthu zambiri zomwe inu simunagwirizane nane molimba, koma musati muziike izo monditsutsa ine, mwawona, mungondikonda ine, mulimonse, chifukwa izo sizingapange kusiyana kulikonse zomwe inu mungachite kapena zomwe inu munganene, ine ndingaganize chimodzimodzi za inu; ngati pali chirichonse, mochuluka, mwawona, ngati ziripo, ine ndikhiza kumaganiza zochuluka za inu. Koma ine ndimakukondani inu, Mulungu akudziwa zimenezo, palibe munthu yemwe angakhoze kutchula Dzina la Yesu Khristu koma yemwe ine ndingamukonde iye. Mukuwona?

32 Ndipo ine sindikufuna kuwawidwa mtima kulikonse kapena kusayanjanitsika, ngakhale ife tikhoza kusagwirizana kwenikweni. Ngati ife tikanakhala kuti tinali pa tebulo ndipo wina akudya mtundu umodzi wa mkate, ndi wina, ndi umzake, izo zikanakhala basi monga momwe ziliri apa, mwawona. Pamene izo zifika ku kuyanjana wina ndi mzake,

ife timakondana wina ndi mzake. Ndipo ngati ife sitimachita zimenezo, ndiye ife tiyenera kuti tizichita zimenezo. Ndipo ngati. . . ife sitidzapita patsogolo paliponse ndi Mulungu mpaka ife titachita zimenezo.

³³ Basi musati muiwale, musati muiwale kuti mphatso yayikulu kwambiri ya mphatso zonse ndi chikondi. “Ngakhale ine ndingayankhule ndi malirime a anthu ndi a angelo, kupereka thupi langa kuti liwotchedwe ngati nsembe, kumvetsetsa chidziwitso chonse, ndi zina zotero, ine sindine kanthu. Chotero. . . Koma pamene icho chimene chiri changwirocho, chomwe chiri chikondi. . .” Ngati mphatso zonse zauzimu sizinawumbidwe pamodzi ndi chikondi, izo zizingagwire. Dongo lina lirilonse lidzasweka, “Koma chikondi chidzapitirira kwanthawizonse.” Mwawona, ameneyo ndi Akorinto Woyamba 13.

³⁴ Tsopano, usikuuno, tikulowa m’badwo wa mpingo waukulu uwu. Oh, mai! Tsopano, ife tikhoza kukhala pafupifupi kotala itakwana (usikuuno) naini. Ndipo tsopano ine ndithudi ndikupepesa kuti ife tiribe malo okwanira, koma. . . oti timukhazike aliyense, okhalapo aliyense, kani, koma ife basi tiribe iwo, ndipo mwinamwake tsiku lina ife tidzatero.

³⁵ Koma tsopano ine ndikufuna kuti ndikupempheni inu kuti mundichitire ine kukonderedwa. Inu mwawona mayimidwe anga ndipo inu mukudziwa zomwe zidzanditengere ine tsiku lina, inu mukuwona, ndipo oralo liri pafupi kwambiri. Mukuona? Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muchite izi, nthawizonse muzindipempherera ine. Ndipo kumbukirani, ine ndakhala woonamtima momwe ine ndikudziwira kukhala woonamtima, mwawona. Ndipo ine ndikuzindikira kuti ine sindirinso mwana konse, ndine wa usinkhu wa zaka fifite-wani zakubadwa. Ndipo ine—ine pamene wanga. . . Ine sindingakhoze kupita mpaka Mulungu atadzandiitana ine. Ndipo ndidzapita momwe Iye akufunira kuti ine ndidzapitire, ndipo izo zidzakhala chomwecho. Mukuwona? Koma ine ndiyenera kukhala woonamtima ndi kunena Choonadi, posatengera. Chotero ine ndimadziwa ndiwo mayendedwe osungulumwa nthawizina, koma bola ngati Iye ali ndi iwe, kodi izo zimapanga kusiyana kwanji? Mukuwona?

³⁶ Tsopano, ife tisanati tilowe mu m’badwo wa mpingo wawukulu uwu, ine ndikudabwa ngati ife tingakhoze kuyimirira tsopano kwa pemphero, mphindi yokha kenanso. Zimenezo zimakhala ngati zakuwongolani inu ndi kumverera bwinoko. Pa msonkhano wotseka, alipo. . . Ndi angati pano angafune kuti akumbukiridwe pamaso pa Mulungu? Ingokwezerani mmwamba manja anu kwa Mulungu, “Ndikumbukireni ine, O Ambuye, kumapeto kwa m’badwo. Pamene moyo udzatha wonse, mudzandikumbukire ine.”

³⁷ Atate Athu Akumwamba, ife tiribe malirime okwanira kuti tifotokoze kuyamikira kwathu chifukwa cha Kukhalapo kwa Mulungu wamoyo kumene kwakhala pakati pathu sabata yathayi, pa zinthu zimene ife taphunzira za Inu, momwe Inu mwadziwululira Nokha kwa ife kudutsa mu nthawi yonse, ndi momwe Inu mwawapangira Mawu Anu kukhala omveka bwino kwambiri kwa ife. Momwe ife tayembekezera pa Inu, ndi momwe ife ta—tayerera kufotokozerera chikondi chathu, ndipo talephera kuti tichite izo, Ambuye, chifukwa malirime achivundi sakanakhoza kuchita izo. Kuti s... pakuti ngakhale kutipulumutsa ife, ndipo Inu...chifukwa ngakhale kutipatsa ife njala ya Inu. Pakuti munalembedwa mu Mawu, "Odala ali iwo akumva njala," (kungokhala ndi njala, ndi mdalitso) "njala ndi ludzu la chilungamo." Ndiye Inu munapanga chobwereza chachikulu chimenecho, "Pakuti iwo adzakhutitsidwa!" Tsopano, ife tikukhulupirira zimenezo, Ambuye. Mutikhululukire ife zolephera zathu.

³⁸ Ndipo pamene ife tikulowa muno usikuuno pa...ku m'badwo wampingo wotsiriza uwu, umene uli Laodikaya, ife titatha kuwawona Malemba ndi mbiriyakale ikugunda nthawi iliyonse molondola ndendende. Chotero, Atate, ife tikudziwa choyankhula chochokera mu uneneri Wanu waukulu apa, wa m'badwo wotsiriza uno, iwo udzakhala monga mibadwo ina isanu ndi umodzi yakhalira. Atate, ine ndikupemphera kuti Inu mulole Mzimu Woyera ubwere kwa ife usikuuno, tsopano, ndipo mutidalitse ife pamene ife tikuyembekezera mopitirirabe pa Inu. Mu Dzina la Yesu. Amen. Khalani pansu.

³⁹ Ngati Ambuye alola, bukhulo li...mofulumira momwe ife tingathere. M'bale Leo akuzichotsa izo pa tepi ya maginito, kuti zizipita ku...kupitirira ku kulembedwa mwachidule, zikachoka pamenepo zipita kukalembedwa, kenako kupita mu bukhu.

⁴⁰ Ndipo ndisanayiwale, Rosella akhala ndi bukhu lake posachedwapa, *Chidakhwa Chipulumutsidwa*. Nonse a inu mukukumbukira nkhani yake, momwe kuti Mzimu Woyera unamuyitanira iye mu msonkhano. Ndipo iye anali... atalepheredwa ndi mabungwe foro aakulu kwambiri a zoledzeretsa, ndipo anakanidwa kuzipatala zomwe zinali mu Chicago. Ndipo Ambuye Yesu, mu nthawi ya mphindi imodzi, anamuchotsera izo zonse kwa iye. Iye akumangopita kuchokera ku ndende kupita ku malo enawo, kumawauza anthu momwe Mulungu amapulumsira, kuyankhula kwa zidakhwa ndi ena otero. Iye wakhala ali...ndi umboni wake, anapindulira anthu ambiri kwa Khristu.

⁴¹ Tsopano, m'badwo wa mpingo woyamba, kodi inu mungandiuze ine kuti iwo unali chiyani? Efeso. Wachiwiri? Smurna. Wachitatu? Pergamo. Wachinayi? Tiyatira. Wachisanu? Sarde. Wachisanu ndi chimodzi? Filadelfia. Wachisanu ndi chiwiri? Laodikaya.

⁴² Woyamba unali pakati pa A.D. 55 ndi 170, Efeso. Smurna, 170 mpaka 312. Pergamo, 312 mpaka 606. Tiyatira, 606 mpaka '520. Sarde, '520 mpaka 1750. Filadelfia, 1750 mpaka sikisi... '06; tsopano, iwo unayambika m'badwo wa Laodikaya, unalowana, ndipo usiku watha ife tinalowa mu kulowana kwapang'ono. Tsopano, ife tiri usikuuno, tikutenga mapeto a Laodikaya.

⁴³ Ife tikukhulupirira kuti mpingo wa Laodikaya unayamba mu A.D. 1906. Ine ndikupenekera... Tsopano, kumbukirani, "kupenekera," makamaka inu mukumvetsera pa tepi. Ine sindikuti izo zidzakhala choncho, koma kupenekera kuti iwo udzatha podzafika 1977, kuti mpingowo udzapita kwathunthu mu chinyengo ndipo iwo udzachotsedwa mkamwa mwa Mulungu. Ndipo Kudza Kwachiwiri, kapena Mkwatulo wa Khristu, ukhoza kudzabwera nthawi iliyonse. Tsopano, ine ndikhoza kuziphonya izo ndi chaka, ine ndikhoza kuziphonya izo ndi zaka twente, ine ndikhoza kuziphonya izo zaka handiredi. Ine sindikudziwa ndi pati... Koma ine ndikugopenekera kuti malingana ndi masomphenya omwe Iye anandiwonetsa ine, ndi kutengera nthawi, momwe iyo ikuyendera, ine ndikuti iyo idzakhala nthawi ina pakati pa '33 ndi '77. Mo—modziwikiratu, fuko lalikulu ili lidzayamba nkhondo yomwe idzaphulitse ilo mu zidutswa, mwawona. Tsopano izo zayandikira kwambiri, ziri pafupi kowopsya. Ndipo ine ndikhoza kukhala ndikulakwitsa, ine ndikupenekera. Aliyense akumvetsa? Nenani, "Ameni," ngati inu mukutero. [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Mukuona?

⁴⁴ Koma Ambuye anandiwonetsa ine masomphenya a mkazi wamphamvu kwambiri, mu '33, 1933, ziri pa pepala. Za momwe kuti "Roosevelt akanati adzapangitse... iye anathandizira kupangitsa dziko kuti lipite ku nkhondo." Momwe kuti "Mussolini akanati adzapange kuwukira kwake koyamba ku Ethiopia ndipo iye akanati adzalilande ilo, koma iye akanati adzafike ku mapeto ochititsa manyazi." Ndi momwe kuti "Kenako kachitidwe katatu: Nazism, Fascism, ndi Communism, zonse zikanadzathera kukhala Chikomisini." Ndipo ndi angati muno akukumbukira ine ndikungokusungani, kukupangitsani inu kuti mungoima, ndi kubwereza izo, ine ndinkakuuzani inu, "Yang'anani Russia! Yang'anani Russia, mfumu ya Kumpoto! Yang'anani Russia, mfumu ya Kumpoto! Yang'anani Russia, mfumu ya Kumpoto!"? Ndi angati anandimvapo ine ndikungoti, ingobayibitsani ilo, mobwereza? Amkhalakale, inu mukuwona, mmbuyo mu gawo loyambirira la mpingo. Ingoimirirani pamenepo ndipo mubaibitse mobwerezabwereza, "Yang'anani Russia, mfumu ya Kumpoto! Mwawona, zomwe iye akanati adzachite, chifukwa kachitidwe konse ako kadzaunjikana mpaka ku Russia."

⁴⁵ Ndiyeno ine ndinanena, kuti "Fuko lino pamapeto pake lidzapita ku nkhondo ndi Germany. Ndipo Germany

adzamangidwa mmakoma a konkire.” Ndipo umenewo unali Mzere wa Magnot, zaka leveni iwo usanayambe nkomwe kumangidwa, zaka leveni zisanachitike. Ndipo ine ndinati, “Achimereka adzamenyedwa mowopsya pamzere umenewo.” Ena mwa abale awa pano anali pa mzere umenewo, M'bale Roy Roberson ndi iwo; afunzeni iwo zimene zinachitika. Iwo ndithudi anatero. Chabwino. “Koma potsiriza,” ine ndinati, “ife tidzagonjetsa ndipo tidzakhala mmodzi mwa opambana mu nkhondoyo pakati pa ife ndi Germany.”

⁴⁶ Tsopano, ine ndinati, “Ndiye pambuyo pake, kuti sayansi ikanadzapita patsogolo kwenikweni.” Iwo anatero, iwo anapanga bomba la atomiki ndi chirichonse. Ine ndinati, “Pa kutukuka kwawo, iwo akanati adzapange a . . . magalimoto mopitirira akanati adzayambe kumawoneka ngati dzira.” Ndipo inu mukukumbukira chigalimoto chachikulu chakale mu 1933, kumbuyo kwakukuluko kumatsika pansu munga chonchi, teyala lapadera kumbuyo kwake? Tayang'anani momwe izo ziliri tsopano, mwawona: kubulungira, mwawona, ngati dzira. Ndipo ine ndinati, “Potsiriza iwo adzapanga galimoto yomwe iwo sakuyenera kudzakhala ndi chiwongolero mkati mwake. Ine ndinawona banja likupita mmusi . . . Amawutcha iwo, 'msewu,' ali mgalimoto yagalasi pamwamba, misewu yayikulu yowoneka bwino ndi galimoto yabwino. Ndipo iwo anali atakhala, akuyang'anana wina ndi mzake, ndipo galimotoyoni inali kudziyendetsa yokha, ikumangopita moyungulira mokhotakhota ndi chirichonse.” Ndipo iwo ali nayo galimotoyoni pakali pano, iyo yapangidwa kale. Iwo ali nayo galimotoyoni. Ndipo ine ndinati ndiye, “Oh, momwe sayansi idzapitire patsogolo tsiku limenero!”

⁴⁷ Ine ndinati, “Kenako ine ndinawona . . . Iwo adzawalola azimayi ndipo akuwalola azimayi kuti azivota. Ndipo mwa kuvota, iwo adzasankha munthu wolakwika ena mwa masiku awa.” Ndipo inu munatero pa zisankho zapitazi. Anali mavoti a azimayi omwe anamusankha Kennedy. Ife tikudziwa zimenezo, mwawona, pakati pa makina opera ndi zinthu zochita kukonzedwa, zomwe FBI yaziyalutsa. Ndipo aliyense akanakhoza bwanji . . . Chifukwa chiyani iwo sakuchitapo kanthu za izo? Chifukwa chiyani chinachake sichikunenedwa? Hah! Kuwopa kuti wina akhoza kutaya ntchito yake. Inu mukuwona, ndi mulu chabe wa ndale, wovunda mpaka mkati. Ndizo zonse. Ndithudi!

⁴⁸ Palibepo ayi—palibe ayi . . . palibe ayi, ndikhululukireni ine. Mulibemo chipulumutso mu fuko lino, mulibemo chipulumutso mu fuko lililonse. Chipulumutso chiri mwa Yesu Khristu ndipo Iye yekha! Uh-huh! Uko nkulondola. Tsopano, ndine wothokoza chifukwa cha America. Ine ndingakonde ndizikhala kuno kusiyana ndi malo aliwonse mdziko lapansi, chifukwa . . . kuna kwa Canada. Canada ndi United States ndi mapasa,

ife tikudziwa zimenezo, mayiko oyandikana, malo odabwitsa, koma ine—ine ndikukhulupirira ine ndingakonde nditamakhala kuno kuposa kulikonse komwe ine ndikukudziwa, chifukwa ndi kwathu. Ndine wokondwa kuti ndine waku America, ndipo ndikuthokoza chifukwa cha zimenezo. Koma ine ndikukuuzani inu, iye ndithudi akusowa chitsitsimutso chomutsutsa, iye ndithudi akutero. Ndipo iye sachipeza icho! Ayi, bwana. Iye sadzaukanso kachiwiri! Ayi, bwana. Iye wapita! Inu mukukumbukira, pafupifupi zaka faifi zapitazo mu Chicago, izo ziri pa tepi. Iwe uli nayo iyo, Gene. Ine ndinati, “Iwo mwina avomereza Iwo chaka chino, kapena iwo apitirira kumagwa pansu.” Ndipo iwo achita zimenezo, mwawona, ndipo iwo adzachita izo mpaka pamapeto pake iye adzakumanizana nawo mathero ake.

⁴⁹ Koma padzakhala mkazi wamphamvu! Tsopano, kumbukirani! Izi ziri pa tepi, nazonso. Mkazi wamphamvu, mkazi wamkulu, iye mwina adzakhala Purezidenti, kapena iye adzakhala mkazi woyimira mpingo wa Katolika (zomwe ine ndikuganiza kuti ziri) adzatenga ulamuliro kuno tsiku lina ndipo iye adzalamulira dziko lino. Fuko lino ndi fuko la mkazi. Mbendera inapangidwa ndi mkazi, ndi nambala sartini. Iye anayambitsa, nyenyezi sartini, mizere sartini, zigawo sartini. Chirichonse ndi sartini, sartini, sartini, mpaka mmusi. Nyenyezi sartini pa dola yake ya siliva tsopano. Chirichonse ndi sartini. Ndi nambala sartini, ndipo akupezeka mu mutu wa 13 wa Chivumbulutso. Kwathunthu sartini! Chirichonse ndi “mkazi, mkazi, mkazi, mkazi,” mpaka kutsika pansu. Ndipo iye anatenga maofesi onse. Iye watenga Hollywood. Iye watenga mafuko. Iye watenga maofesi. Iye watenga chirichonse chimene chiripo; mafulu ofanana ndi mwamuna, kuvota ndi mwamuna, kutukwana ngati mwamuna, kumwa ngati mwamuna, china chirichonse. Ndipo nyambo chabe ya mpingo wa Katolika, ya kupembedza mkazi! Iwo akumupembedza kale mkazi, mulimonse.

⁵⁰ Iye ndi wopambana... Mkazi wachiwerewere ndi nyambo yopambana yomwe satana anayamba wakhalapo nayo. Iye ndi woyipa kuposa zipinda zomwera mowa zonse zomwe zinayamba zakhalapo. Iye akhoza kutumiza miyoyo yambiri ku gehena kuposa zipinda zonse zomweramo mowa mdziko. Uko nkulondola.

⁵¹ “Mkazi wabwino ndi ngale mu korona wamwamuna,” anatero munthu wanzeru kwambiri padziko lapansi. Mwamuna akuyenera kulemekeza mkazi wabwino, mwawona. “Koma woyipa ndi madzi mmagazi ake,” ndipo magazi ake ndi moyo wake. Amuna inu omwe muli ndi akazi abwino, inu simukudziwa momwe mukuyenera kumamuthokozera Mulungu chifukwa cha mkazi wabwino! Pakuti ngati Mulungu akanakhoza kumupatsa munthu chirichonse chabwinoko ngati

chomuthandizira, Iye akanakhoza kuchita icho. Koma mkazi ndi wothandizira wopambana kwambiri yemwe Mulungu angamupatse mwamuna. Koma pamene iwo atembenuka . . .

⁵² Iye anali iyeyo m'munda wa Edene amene Satana anamusankha ngati chida chake. Iye sanatenge mwamuna, iye anamtenga mkazi. Nchifukwa chiyani iye sanapite kwa Adamu kuti akamupatse iye zilakolako? Iye anabwera kwa mkaziyo ndipo anamupatsa iye, mwawona, chifukwa ameneyo anali yemwe iye anamusankha. Mulungu anatenga mwamuna, ndipo Satana anatenga mkazi.

⁵³ Ndipo muyang'ane mpaka mmusi momwe, ndipo pamapeto . . . Pamene Babulo anakhazikitsidwa pachiyambi, *Mababulo Awiri* a Hislop, mkazi! Pamene izo zinafika mpaka mmusi mu m'badwo; tsopano zikutsirizitsa m'badwo wa Amitundu. Babulo anayamba monga choncho, ndipo akuthera ndi kupembedza mkazi (Maria) mu mpingo. Ndi tsiku lotani limene ife tikukhalamo!

⁵⁴ Tsopano, *Laodikaya*, m'ba—m'badwo wa Laodikaya, mawuwo amatanthauza “wofunda.” Ndi wolemera ndi katundu, ndipo amaganiza kuti iye sakusowa kanthu. Koma Baibulo limanena kuti iye ndi “wopanda pake, wakhungu, womvetsa chisoni, ndi wamaliseche.” Ndi chikhalidwe chotani!

⁵⁵ Mphoto kwa iwo amene agonjetsa m'badwo uno wa mpingo, ndi “kudzakhala pampano wachifumu ndi Ambuye.”

⁵⁶ Tsopano, nyenyezi, kapena mngelo, kapena wamthenga wa m'badwo wa mpingo uwu, sakudziwika.

⁵⁷ Tsopano, wamthenga wa m'badwo wa mpingo woyamba, anali ndani ameneyo? Paulo, Efeso. Smurna? Ireniasi. Pergamo? Marteni Woyera. Tiyatira? Columba. Sarde? Luther. Filadelfia? Wesley. Ndipo mu . . . Laodikaya uwu, ife sitikumudziwa panobe, ndipo mwinamwake sitimudziwa mpaka iwo wonse utadzatha.

⁵⁸ Koma ine ndikungofuna kuti ndipereke zobwereza zanga za zomwe mngelo uyu adzakhale, chomwe ife tikuchiyembekezera. Kodi izo zingakhale zabwino? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Pokhala kuti ife tiri ndi nthawi yochepa, ine ndinangolembe chobwereza chaching'ono apa cha zomwe ine ndimagana.

⁵⁹ Mngelo wa mpingo wa Laodikaya uwu, kuti adzamalizitse iwo. Tsopano, iye adzakhala kumapeto kwa m'badwo, monga ena onsewo, monga Baibulo. Iye adzakhala kumapeto kwa m'badwo. Osati koyambirira kwake, kumapeto kwake, chifukwa mngelo nthawizonse amabwera kudzadzudzula . . . iwo pa zomwe iwo achita. “Kwa—kwa mngelo wa mpingo wa Laodikaya lemba zinthu izi.”

⁶⁰ Mwawona, “Kwa mngelo wa mpingo wa Smurna lemba zinthu izi.” Mwawona, iliyonse ndi ya kwa mngelo kumapeto

kwa m'badwo. Paulo, kumapeto kwa m'badwo. Ndi kumatsika monsemo, kumapeto kwa m'badwo. Kulowana, kumapeto kwa m'badwo. Kumapeto kwa m'badwo, ndi zomwe zimapangitsa iyo kulowana. Mukuwona, “Kwa mngelo,” kuyankhula zomwe zinali. Uwu ukulowana apa, “Kwa mngelo,” kumapeto kwa m'badwo umenewo. Mwawona, kuyambira pomwe apa, unapanga kulowana monga makwerero kupita mmwamba, Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo.

⁶¹ Tsopano, mngelo uyu yemwe akubwera mu tsiku lino, ine ndikufuna kuti. . . Ine ndiri ndi chinachake cholembedwa apa, ine ndikungofuna kuti ndichiwerege icho. Koma iye adzadziwika gawo lotsiriza la m'badwo. Ndipo chifukwa ife tiri pafupi kwambiri ku izo—pafupi kwambiri ndi m'badwo wa Kuwala umenewo, kuti mwinamwake iye ali padziko lapansi tsopano. Mwawona, simukumudziwa iye. Iye adzakhala mne—mneneri wamphamvu yemwe ati adzakanidwe ndi dziko la mpingo, pakuti iwo adzapitirirabe mmachimo awo ndipo potsiriza adzalavulidwa mkamwa mwa Mulungu, kutuluka mkamwa mwa Kukhalapo kwa Mulungu.

⁶² Ine ndikukhulupirira iye adzakhala wina wonga Eliya. Ine ndipereka zifukwa zanga. Tsopano tiyeni tingotembenezira apa mu Bukhu la Malaki, mphindi chabe, ine ndikupatsani inu chifukwa chimene ine ndikuganiza kuti adzakhala wodzozedwa ndi Mzimu wa Eliya. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muvale chanu—chisoti chanu cha chisomo tsopano. Malaki, mutu wa 4. Tsopano, mvetserani pamene ine ndikuwerenga, ndi inu mu Baibulo lanu. Tsopano, talingalirani mwacheru kwenikweni tsopano kwa maminiti angapo otsatirawa, tsopano, ife tisanapite mu m'badwo wa mpingowu.

Pakuti, tawonani, tsiku likudza, limene lidzatenha ngati ng'anjo; ndi onse onyada, eya, . . . onse ochita zoyipa adzakhala ziputu: ndi tsiku lomwe likudza lomwe liti lidzawatenthe iwo, atero YEHOVA wa makamu, ndipo silidzawasiyira iwo muzu kapena nthambi.

⁶³ Kodi Iye akunena chiyani? Iye akuyankhula ku tsiku lomwe likubwera. Kodi inu mungavomereze pa zimenezo? Ku tsiku la kudza kwa Ambuye.

Koma kwa inu . . .

⁶⁴ Tsopano taonani, tsopano Iye akuyankhulanso kwa Israeli. Tsopano, kodi Iye anati chiyani? “Pakuti, taonani tsiku likudza (kutsogolo uko) lomwe lidzatenha.”

Koma kwa inu amene mumawopa dzina langa . . . Dzuwa la chilungamo lidzatulukira ndi machiritso mmapiko mwake; ndipo inu mudzatulukira, ndi kukula ngati ana a ng'ombe onenepa.

Ndipo inu mudzapondereza oyipa; pakuti iwo adzakhala maphulusa pansi pa zidendene za mapazi anu mu-...mu tsiku lomwe Ine ndidzachita ichi, atero YEHOVA wa makamu. (Osati...Tsiku lomwe Iye adzawotche dziko lapansi, ife tidzaponda pa maphulusa awo. Ndizo Zakachikwi, ndithudi, mwawona.)

Kumbukirani...chilamulo cha Mose mtumiki wanga, chimene Ine ndinamulamulira...iye mu Horebu kwa Aisraeli onse, pamodzi ndi malamulo ndi chiweruzo.

Taonani, Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri kusanafike kudza...ndipo tsiku lalikulu ndi lowopsya la AMBUYE:

Ndipo iye adzatembenuzira mitima ya atate kwa ana, ndi mitima ya ana kwa atate, kuti ine ndingadze ndi kukantha dziko lapansi ndi themberero.

Kumalizika kwa Chipangano Chakale.

⁶⁵ Tsopano, Yesu anati...Mateyu 17:10, poyankhula za izi. Ayuda onse ali kuyembekezera Eliya wakudzayo. Tsopano, taonani zimene Yesu ananena za izo, Mateyu 17:10. Ife tiyambira pa ndime ya 9, Mateyu 17:9:

Ndipo pamene iwo anatsika pansi kuchoka pa phiripo, Yesu anawalamulira iwo, nanena, Musakawuze munthu aliyense ma...Musakanene masomphenyawo kwa munthu aliyense, (Mwawona, "Musati mukanene izi. Inu mukudziwa zimenezo, koma muzisunge izo kwa inueni.")...Musauze munthu masomphenyawo, kufikira Mwana wa munthu atawuka...kuchoka kwa akufa. Musati mukanene zimenezo.

Ndipo ophunzira ake anamufunsa iye, anati, Nanga bwanji ananena alembi kuti Eliya akuyenera kubwera kaye poyamba? Nchifukwa chiyani ayenera Eliya kudzabwera poyamba asanadze Khristu uyu, Dzuwa la chilungamo? Nchifukwa chiyani iwo ananena izi? Apa, Inu muli kale apa, ndipo alembi ananena kuti—kuti Eliya akanadzabwera kaye poyamba.

Tsopano, taonani:

Ndipo Yesu anayankha ndipo anati kwa iwo, Eliya ndithudi adzabwera, ayenera adzabwere poyamba, ndi kudzabwezeretsa zinthu zonse.

Koma Ine ndinena kwa inu, Kuti Eliya anabwera kale, ndipo inu simunamudziwe iye, (Mwawona, Iye sananene kuti iye anali ndani, mwawona.) koma mwamuchitira iye zimene inu munazifuna. Momwemonso Mwana wa munthu adzazunzidwa ndi iwo.

Ndipo ophunzira anamvetsa kuti iye amayankhula kwa iwo za Yohane M'batizi. (Tsopano—tsopano, Yohane M'batizi anali Eliya amene anali nkudza.)

66 Tsopano taonani, ine ndikubwerera ku Malaki mutu wa 4, kenanso. Tsopano kumbukirani, Iye ananena apa kuti “Lisanadze lalikulu ndi lolemekezeka, Tsiku lowopsya la Ambuye, Ine ndidzakutumizirani inu Eliya mneneri.” Ndime ya 5:

Koma Ine ndidzatumiza kwa inu...mneneri...Ine ndidzatumiza kwa inu Eliya mneneri lisanadze lalikulu ndi tsiku lowopsya la... [Osonkhana akuti, “AMBUYE.”—Mkonzi].

67 Kodi ife tikupeza chiyani “mu Tsiku la Ambuye”? Kumapeto kwa m'badwo! Ndi pamene dziko liti lidzawotchedwe. Inu mukukumbukira momwe ife tinamutengera Iye atavala wigi yoyera, inu mukudziwa, ndi—ndi chifuwa Chake, ndipo atadzimanga nazo pachidale. Inu mukukumbukira zimenezo? Ndipo ife tinatsimikizira mwa Baibulo, ilo silinali tsiku la *sabata* ngakhale *Lamlungu*, ilo linali Tsiku la Ambuye. Ndi kulondola uko? Ndipo ndiro tsiku limene Iye adzabwere ngati Woweruza, “Ndipo adzakantha dziko lapansi ndi themberero.” Ndi kulondola uko?

Ndipo Ine ndidzatumiza kwa inu Eliya mneneri lisanadze tsiku lalikulu ndi lowopsya la AMBUYE:

68 Tsopano, taonani kubwera kwapawiri kwa Eliya. Tsopano, ngati inu mungazindikire, Lemba lirilonse limakhala ndi matanthauzo apawiri, “Koma Izo zimabisika pamaso pa anzeru ndi aluntha, ndi kuwululidwa kwa makanda omwe angaphunzire.” Kodi inu simukukhulupirira zimenezo? Tsopano, gwirani Malaki 4 pamenezo.

69 Ndipo tsopano tiyeni tibwerere ku Mateyu 2 miniti yokha, kungodutsa tsambalo, Mateyu 2. Ine ndikukhulupirira ine ndimayenera kuti ndimatanthauza Luka 2 mmalo mwa Mateyu 2. Ine ndazilemba izo apa, koma ine ndimafulumira mphindi zochepa chabe zapitazo, ndipo Mzimu Woyera unali mchipinda pa ine ndipo ine ndimangokhala ndi nthawi yopambana. Chotero ine ndimatanthauza...2, tiyeni tiwone ngati izi zingakhale zimenezo. Tsopano, ndiloleni ine ndiwerenge apa miniti yokha. Mateyu 2? Pamenezo si pamene ine ndikupafuna, ndi choncho? Tsopano, miniti yokha, ine ndipapeza pamenezo basi... Ndiloleni ine ndikhale ndi kanthawi pang'ono apa chifukwa ine ndikufuna kuti inu mukhale otsimikiza kuti mwaziwona izo, kuti Lemba liri ndi tanthauzo la pawiri kwa Ilo. *Kulambira kwa Anna; Kubwerera ku Nazareti; Pasaka; Utumiki wa Yohane.* Tsopano, ndiloleni ine ndiwone ngati ine ndingakhale kuti ndimatanthauza Luka, ine ndimawerenga penapake ndipo... Ine—ine ndikutanthauza Marko mmalo mwa Luka, ayenera kuti

anali Marko. Koma ine ndikufuna kuti inu mutenge Lemba ili kuchitira kuti—kuti inu mudziwe kuti iyo ndi ntchito ya Ambuye, kuti Iye amachita izi mwanjira iyi. Tsopano, ine ndikuwuzani inu pamene ine ndikupafuna, pamene, “Kuchokera mu Igupto Ine ndinaitana mwana Wanga.” Winawake amene ali ndi zowerenga za m'malire yemwe angapeze izo mofulumira kwenikweni kapena kupapeza pamenepo? “Kuchokera mu Igupto Ine ndamuitana mwana Wanga, Ine ndamuitana mwana Wanga.” Tsopano, mphindi chabe.

⁷⁰ [M'bale akuti, “Luka 1:17.”—Mkonzi]. Luka 1:17. Zikomo inu, m'bale. Ndiko kulondola, Luka 1. Marko...Luka 1:17, m'malo mwa 2. Ine ndikufuna kupeza ya 14, ndi pamene... Ndi pamenepo, m'bale. Ndiko kulondola ndendende, Luka 1:17. Chabwino. Tsopano, tsopano inu mukhoza kulemba zimenezo. Tsopano, chomwe icho chiri, ndi kuchokera mu madalitso a Ambuye, kuti izo zinadalitsidwa.

Ndipo iwe udzakhala nacho chimwemwe ndi chisangalalo; ndipo ambiri adzakondwera pa kubadwa kwake.

Pakuti iye adzakhala wamkulu pamaso pa Ambuye, ndipo sadzamwa konse vinyo kapena chakumwa cha ukali;

⁷¹ Munthu uyu amene akubwera adzaphunzitsidwa kuchokera pakubadwa kwake kuti asadzamwe kapena kukhala ndi kanthu kochita ndi tchimo monga choncho. Inu mukumvetsa izo?

...ndipo iye adzadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ngakhale kuchokera mmimba mwa amayi ake.

Ndipo ana ambiri a Israeli iye adzawatembenezira kwa Ambuye Mulungu wawo.

Ndipo iye adzapita patsogolo pa iye mu mzimu, ndi mu mphamvu ya Eliya, kuti akatembenezire mitima ya atate kwa ana, ndipo osamvera ku nzeru za olungama; ndi kuwakonzekeretsa anthu okonzekera Ambuye.

⁷² Tsopano, tsopano ife tikuzindikira kuti iye anali ataloseredwa, ndipo Yohane anali munthu ameneyo! Ndi kulondola uko? Yohane anali Eliya, wa tsiku limenero, yemwe anali kubwera.

⁷³ Tsopano, ife tikudziwanso kuti Lemba nthawizina limatanthauza zinthu ziwiri. Ilo limanena chinthu chimodzi, monga uko mu Mateyu pamene Ilo linati, “Kuchokera mu Igupto Ine ndinaitana mwana Wanga.” Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti ndi zomwe ine ndimazisaka, “Kuchokera mu Igupto ine ndinaitana mwana Wanga.” Ndiyeno ngati inu mungatsatire icho “mwana wamwamuna” cholozera chimenecho, Iye anali...sanatero...Icho chinabwerera kwa Hoseya, zomwe sizimatanthauza Yesu, Mwana Wake; uyo anali—anali Israeli,

mwana Wake, “Kuchokera mu Igupto Iye anaitana Israeli.” Koma iwo anali ndi matanthauzo apawiri ndi kumvetsetsa kwakukulu kwa izo pamene izo zimatanthauza ndi kulankhula za—kubwera kwa Yesu, amene anali wamkulu kuposa—kuposa Israeli, pamene Iye anaitana Israeli atuluke. Chabwino.

⁷⁴ Tsopano, ife tikupezanso kuti izo zakhala...mu kudza Kwake koyamba sipanali pa Tsiku la Ambuye. Ndi kulondola uko? Tsopano, kubwerera ku Malaki, tiyeni tiwongole ichi poyamba, “Kubwera pa Tsiku la Ambuye.” Tsopano, taonani kubwera Kwake kwa pawiri, kubwera Kwake kumodzi ndi kwachiwiri Kwake. Kodi inu mwakonzeka ndi kuganiza kwanu kwauzimuko? Ndime ya 6 tsopano, “Iye adzatero...”

...Iye adzatumiza...Eliya...lisanadze...tsiku lalikulu ndi lowopsya la AMBUYE: (Ndi kulondola uko?)

⁷⁵ Tsopano, ife tikuzindikira kuti ameneyo sanali Yohane, chifukwa ilo silinali Tsiku lowopsya la Ambuye (linali ilo?), ndipo Iye...komanso Iye sanalitenthe dziko lapansi. Chotero ziyenera kuti zinkatanthawuza kuwonetseratu, kapena—kapena kubweranso kwina kwamtsogolo kwa Yohane... kapena kwa—kwa Eliya. Ndi kulondola uko? Chifukwa Iye anati, “Ndidzatumiza Eliya, ndipo Ine ndidzatatentha dziko lonse lapansi, ndipo Ine ndidzangoliyeretsa ilo, ndipo inu mudzayenda pa maphulusa awo.” Ndizo Zakachikwi, ife tikudziwa zimenezo. Bomba la atomiki likadzaphulitsa izo mzidutswa, ndiyeno padzakhala...dziko lapansi lidzawongoka. Ndipo padzakhala Tsiku lalikulu pano padziko lapansi, ndipo Mpingo udzalamulira ndi Yesu padziko lapansi kwa zaka chikwi. Ndi kulondola uko? “Koma lisanadze Tsiku lalikulu ndi lowopsya la Ambuye, pamene ilo liti lidzaphulitsidwe, Ine ndidzatumiza kwa inu Eliya mneneri.” Ndi kulondola uko? Chotero izo sizimatanthauza Yohane Mbatizi mu chikhalidwe chimenecho, chifukwa Tsiku lowopsya la Ambuye kunalibeko nthawi imeneyo, zaka zikwi ziwiri zitadutsapo. Ndi kulondola uko?

⁷⁶ Tsopano, taonani ndime yotsatirayo. Ndipo ngati inu mungakhale auzimu kwenikweni tsopano; tsopano, iyi ndi kalata ya chikondi, ndipo inu mukuyenera kuwerenga pakati pa mizere ndipo kenako imakhala yolondola. Inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza. Kumbukirani momwe ine ndinanenera, Lemba, “Yesu anamuthokoza Mulungu chifukwa Iye anzibisa Izo kwa anzeru (kwa maso) ndi aluntha, anaziulula Izo kwa makanda.” Tsopano, ine kawirikawiri ndayerekezapo za mkazi wanga pamene iye wandilembera ine kalata; ine ndikhoza kuwona zomwe iye akunena pa kalatayo, koma ine ndimawerenga pakati pa mizere kuti ndidziwe zomwe iye akutanthauza, mwawona, chifukwa ine ndimamukonda iye ndipo ine—ine ndimadziwa chikhalidwe chake. Ndipo inu mukuyenera kudziwa chikhalidwe cha Mulungu ndi

kumukonda Iye, ndiyeno Malemba amawoneka bwino kwa inu. Iye amawawulula Iwo.

77 Tsopano, taonani ndime yotsatira:

Ndipo iye adzatembenzira mitima ya atate kwa ana,
(Tsopano, taonani.) *ndi mitima ya ana kwa atate, . . .*
(Mwawona?)

78 Tsopano, pamene Yohane anabwera ngati Eliya, iye anatembenzira mitima ya Aisraeli, mitima ya ana amene panthawiyi ankaulandira uthenga wake, mitima ya atate kwa ana. Koma pamene iye akubwera nthawi *ino*, iye akudzatembenzira mitima ya Mpingo kubwerera kwa makolo Achipentekoste. Mukuwona, ndi chosemphanitsa pamenepo. Inu mukumvetsa zimenezo? Tsopano, werengani Iwo!

79 Tsopano, mvetserani mwatcheru tsopano:

Ndipo Iye adzatembenzira mitima ya atate kwa ana, . . .

80 Wansembe wakale wa orthodox; iye awauza iwo zimenezo, “Bwanji, Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi apa kuwukitsapo ana kwa Abrahamu. Inu musati muziganiza kuti inu mungathe . . .” Mukuwona? Tsopano, iye adzatenga mitima ya wansembe wakale wokhakhala wa orthodox ndi kutembenezira mitima yawo ku Chikhulupiriro chimene ana anali nacho kuno. Mwawona, “Tsopano, onse awa omwe abatizidwa ndipo akuyembekezera kudza kwa Mesiya. Ndani wakuchenjezani inu, inu kam’badwo ka amamba, kuti muthawe mkwiyo womwe uli nkudza?” Oh, mai! Inu mukuwona, “Iye anali kutembenezira mitima ya atate kwa ana.”

81 “Ndi mitima ya ana kwa atate.” Tsopano, pamene Eliya wamkulu *uyu* adzabwera kumapeto kwa m’badwo uno, iye adzakhala akutenga Uthenga wa Pentekoste kuti atembenezire ana ku Chikhulupiriro cha atate, chifukwa iye adzakhala akuwadzudzula iwo chifukwa chakuti iwo sanasunge Chikhulupiriro chomwecho chimene chinali kumbuyo uko pachiyambi. Ameni! Tsopano, ine ndikukhulupirira ife tikudziwa bwino lomwe adzakhala Eliya. Sichoncho ife? Tsopano ife tikudziwa zimenezo.

82 Ndipo izo ziyenera . . . Tsopano inu mukuwona, Tsiku lowopsya la Ambuye silinafike. Ine nthawi zambiri ndimadabwa, “Kodi munthu uyu adzangokhala mlaliki, ndiye?” Eliya anachita zozizwitsa zonse, osalalikira. Koma pamene Mzimu wake unali pa Yohane, Iwo unachita kulalikira konse ndipo panalibe zozizwitsa. Chifukwa chiyani? Yesu anali woti amutsatira iye, Iye akanadzachita zozizwitsa, “Pakuti Dzuwa la chilungamo lidzatuluka,” iye anatero, “ndi machiritso mmapiko mwake.” Chotero Yohane sanasowekere kuti azichita zozizwitsa, iye anangolengeza za kubwera kwa Khristu. Ndipo iwo . . .

⁸³ Tsopano, kumbukirani, ndipo Yohane uyu . . . kapena Eliya uyu amene adzabwera, sadzamvetsedwa, iye adzakhala munthu wamphamvu chomwecho pamaso pa Ambuye mpaka anthu adzaganiza kuti iye ndiye Mesiya weniweniyo.

⁸⁴ Chifukwa abwenzi ake omwe apamtima anati kwa iye, “Ndinu Mesiya.”

⁸⁵ Iye anati, “Sindine woyenera kumasula nsapato Zake, koma Iye akubwera pambuyo panga!”

⁸⁶ Chifukwa iwo anali pansu pa kuyembekezera, ndiye, kuti awone Mesiya, iwo ankaganiza kuti Mesiya anali akubwera . . . Pamene iwo anawona chochitika chachikulu ichi chikudzuka pakati pawo, iwo anati, “Iye ndiye Mesiya.”

⁸⁷ Yohane anati, “Sindine Iye! Koma Iye akubwera pambuyo panga!”

⁸⁸ Oh, mai! Inu mukumvetsa zimenezo? Chotero abwenzi ake apafupi adzaganiza kuti iye ndiye Mesiya.

⁸⁹ Tsopano, zindikirani chinthu china chomwe chidzachitike, chikhalidwe cha ichi, iye adzabwera basi Tsiku la Ambuye lisanafike. Tsopano, dziko silinawotchedwe konse mmasiku a Yohane, chotero izo zidzakhala mtsogolo. Pamene iye anabwera nthawi yoyamba, iye anangolalikira basi; nthawi yachiwiri, iye—iye adzachita ziwiri zonse kulalikira ndi zizindikiro zolonjezedwa ndi Yesu Khristu. Chabwino, tsopano, tiyeni ife tiyang’ane pa chikhalidwe, chomwe icho chidzakhale, chikhalidwe cha mneneri uyu yemwe akubwera.

⁹⁰ Tsopano, ife ndife okhutira kuti mngelo wa m’badwo wotsiriza wa mpingo uwu, ananenedweratu kuchokera mu Chipangano Chakale kumatsika; tsopano, ena onsewo sanali. Paulo, Ireniasi, iwo sanali onenedweratu. Koma m’badwo wotsiriza uno, pa mapeto a chimaliziro, mapeto a dziko lapansi, iyo idzakhala nthawi yopambana kwambiri yomwe ife titi tikhale nayo basi kutsogolo kwathu, chotero mngelo uyu wa m’badwo uno ananenedweratu njira yonse mmbuyo mu Lemba, Lemba Lakale, kumalizitsa kwa m’badwo uno. Ndi Eliya, wodzozedwa wamkuluyo.

⁹¹ Tsopano, taonani! Kodi ndi chikhalidwe chotani chomwe Eliya adzakhale nacho? Choyamba, iye adzakhala mneneri wamphamvu woona ku Mawu a Mulungu, pakuti Eliya anali woona, ndipo Yohane anali woona. Uko nkulondola. Kuchita zizindikiro ndi zodabwitsa, kudzatembenezira mitima ya ana kubwerera ku Chikhulupiriro cha atate Achipentekoste. Iye adzadana ndi zipembedzo monga Eliya ankachitira. Ndiko kulondola, iye adzatero! Ine ndikuganiza ife tangochiyamba kumene chinthucho cha iye tsopano; za nthawi yomwe iye adzafike. Iye adzadana ndi zipembedzo! Eliya ankadana nazo izo, ndipo momwemonso Yohane ankadana ndi chipembedzo.

92 Yohane anati, “Musati mubwere, ndikuganiza, ‘Tsopano ife tiri naye Abrahamu kwa atate wathu.’ Inu Afarisi ndi Asaduki, inu gulu la amamba! Njoka muudzu,” mwakuyankhula kwina. “Pakuti ine ndikuuzani inu, Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.”

93 Eliya anati, “Iwo onse asochera, aliyense wa iwo! Palibe amene watsala kupatula ine ndekha.” Oh, mai!

94 Iye adzadana nawonso akazi odzikongoletsa! Eliya anatero: Yezebeli. Nkulondola uko? Yohane anatero: Herodia. Onse awiri aneneri, Mzimu, Mzimu womwewo. Iwo ankadana nalo dziko lachipembedzo, dziko la mpingo. Iwo ankadana, nawonso, odzikongoletsa, akazi osakhala abwino. Iwo... Chinachake mkati mwa mzimu wawo chinkafuula motsutsa chinthucho! Yezebeli ankafuna mutu wa Eliya ndipo anali woti awudule iwo; ndipo iye anadulitsanso mutu wa Yohane, Herodia anatero. Onse a iwo!

95 Mneneri uyu adzakhala wokonda chipululu! Monga Eliya, Iye ankakhala mchipululu, yekha. Yohane, mchipululu, yekha. Ndiye ife tikudziwa kuti adzakhala Eliya. Chabwino.

96 Ndipo mneneri uyu adzakhala mmodzi yemwe ati adzakhale ndi Mawu owona a Mulungu. Inde, iye adzakhala nawo Iwo, Mawu onse. Kuti atani? Kuti adzabwezeretse Chikhulupiriro (kwa mpingo wa Efeso) chomwe chatayika nthawi yonseyi, Chikhulupiriro, mu mpingo umene unali ndi “Khomu lotseguka” litaikidwa patsogolo pake ndipo analikana Ilo.

97 Osati munthu wophunzira. Eliya sanali munthu wophunzira, Mtisibe. Yohane sanali munthu wophunzira. Luka 1:67, Baibulo linanena kuti iye anali... “Kuti mwanayo anali mkati... posakhalitsa iye atangobadwa, iye anatengedwera ku chipululu, anali mchipululu kufikira tsiku limene iye anadzawonetsedwa kwa Israeli.” Uko nkulondola. 1:... Luka 1:67 mpaka ndime ya 80, ngati inu mukufuna kulemba izo.

98 Mneneri ameneyu adzakhala munthu wokhala ngati wolunda. Eliya, atatha kukhala ndi msonkhano wopambana, panalibe amene amakhoza kuyanjana naye iye. Eliya amakhala ndi kulosera. Pamene Iye anapita kunja uko ndi kukayitanitsa moto kuchokera kumwamba ndipo anawotcha maguwa a Baala ndi chirichonse, iye anathawira mu chipululu ndipo iye anati, “Ambuye, sindine wabwino kuposa makolo anga, ndiloleni ine ndife.” Nkulondola uko? (Ndipo Yohane...) Iye—iye anakakhala pansu pa mtengo wa mthundu, ndipo chitatha chitsitsimutso chachikulu, tsopano iye ankafuna kuti afe.

99 Ndipo Yohane, pamene iwo anamuponyera iye mu ndende (mkazi woyipa uyu) iye anakakhala kumbuyo uko ndipo anayamba kukhala wokhumudwa. Ine ndikukhulupirira Pember kapena mmodzi wa iwo anati, “Diso lake la mphungu

linaphimbidwapo, mu ndende.” Iye anatumiza ena mwa ophunzira ake.

¹⁰⁰ Ndipo, bwanji, iye anali atalengeza, anati, “Apo pali Mwanawankhosa wa Mulungu amene amachotsa tchimo la dziko lapansi.” Yohane anawona Lawi la Moto litapachikika pa Iye, ngati Nkhunda, ndipo likutsika pansi, kudzakhazikika pa Iye. Anachitira umboni zonsezo, ndipo anati, “Ameneyo ndiye Mwanawankhosa wa Mulungu!” Ndipo anati, “Ine ndiyenera kuti ndibatizidwe ndi Inu, ndipo nchifukwa chiyani Inu mukubwera kwa ine?”

Yesu anati, “Balola kuti izo zikhale chomwecho tsopano.”

¹⁰¹ Koma pamene iwo anadzamuika iye mndende, iye anafika pamalo okhumudwa mofulumira kwenikweni. Mwawona, zinali ngati zovutirapo, sanakhoza konse kumunyamula iye. Ndipo pamene iwo anatero, iye anati, “Pitani mukamufunse Iye ngati Iye alidi Yemweyo, kapena kodi ife tiyembekezere wina kuti abwere?” Ndendende basi monga Eliya anachitira, mwawona, chimodzimidzi basi.

¹⁰² Iye, mtundu wa munthu wolunda, kotero ife timamumvera chisoni iye chifukwa ife tikudziwa chimene icho chiri. Chabwino.

¹⁰³ Tsopano, tsopano pa... Mpi—Mpingo, pa kuwonetseredwa kwake... Ine kulibwino ndizisiye izo zokha. Pa kuwonetseredwa kwake, a—Mpingo... Pamene iye akudzipangitsa yekha kudziwika, Eliya wamphamvu uyu yemwe Mulungu adzamtumize kwa ife, pamene iye adzadzipangitsa yekha kudziwika monga Eliya anachitira, Mpingo unali wokonzeka kuti upulumutsidwe, unapulumutsidwa kuchoka mmanja mwa chikunja. Nkulondola uko? Basi pamene iye anadzabwera apo ndikudzati, “Ife titsimikizira kuti Mulungu ndi ndani,” Eliya anawuwombola Mpingo. Ndipo Yohane, monga Yohane anachitira, iye anati pamene iye anawona Yesu, iye anati, “Ine ndiyenera ndichepe ndipo Iye ayenera kuti akule.” Yohane anayamba kulalikira, anadzipangitsa yekha kudziwika kusanachitike kudza kwa Ambuye. Kumapeto komwe, kuwonetseredwa. Chabwino.

¹⁰⁴ Tsopano, ife tikupeza kuti Eliya akuyenera kutanthauza m’badwo uno kwa Mpingo uwu. Kuti atsimikizire kuti anali Eliya: Eliya atatha kupereka uneneri wake, Eliya samayenera kuti achite kufa, iye anasandulika ndipo anatengedwera kupita Kumwamba; choyimira cha Mpingo (kumapeto kwa Eliya uyu amene adzabwere, kumapeto kwa nthawi *yake*), Mpingo udzapita mu Mkwatulo, popanda kupita kudutsa mmithunzi ya imfa. Iwo udzakhala Mkwatulo! Ine ndikukhulupirira Eliya wamkulu, wamkuluyo amene akubwera, adzakhala Eliya wodzozedwa yemwe waloseredwera kwa masiku otsiriza. Ameni! Ine ndikuganiza iye adzakhala, pamene

iyе adzabwera, mngelo, kapena mthenga ku mpingo mmasiku otsiriza (okanidwa, anthu otsika, monga momwe mpingo uwu udzaloweremo, ndipo watero kale). Ine ndikuganiza Eliya analonjezedwa mu Baibulo. Ine ndikuganiza ife tikhoza kumvetsetsa zimenezo, kuti Eliya ndi amene analonjezedwa mu Baibulo kuti adzabwera mu tsiku lino. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

¹⁰⁵ Tsopano, tiyeni titembenuzire tsopano ku Laodikaya ndipo ife tiwona zomwe Ambuye wathu ati anene kwa ife usikuuno zokhudza Laodikaya, Laodikaya. Chabwino, malonje kwa mpingo:

... *kwa mngelo wa Ambuye* . . .

¹⁰⁶ Ndime ya 14 mpaka mutu wa 3 wa Chivumbulutso:

... *kwa mngelo wa Ambuye* . . . *wa* . . . *Laodikaya lemba; Zinthu izi zimene anena Ameniyo, mboni yokhulupirika ndi yowona, ndi chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu;*

¹⁰⁷ Oh, mai! Ife tiri nazo zonse. . . Ngati ife tikanakhala usiku wonse pa izo apo pomwe, momwe Ambuye akanatiululira izo kwa ife! Tawonani!

¹⁰⁸ “Ameni” ndiye “Wotsiriza.” Iye wawonekera njira yonse monsemo, ndi zinthu zosiyanasiyana, koma apa pali m’badwo wotsiriza wa mpingo pamene akuti, “Ine ndine. . . Uku ndiko kumalizitsa, Ine ndine Wotsiriza.”

¹⁰⁹ Tsopano, kuti asonyeze kuti Iye anali “Woyamba” aponso, monga Iye anali, Iye ali “chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu.” Oh! Kodi inu mukuzimvetsetsa Izo? Mukuwona? Kodi Mulungu angalengedwe bwanji ngati Iye ali Mzimu? Kodi Iye angakhoze bwanji kukhala? Iye—Iye ndi Wamuyaya! Iye sanalengedwe konse, Iye sadzalengedwa konse, chifukwa Iye anali Mulungu pachiyambi. Koma Iye amene ali “chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu” anali Yesu Khristu pamene Iye anawonetseredwa, pamene Mulungu ankakhala mwa Iye. Iye ndi *chilengedwe* cha Mulungu! Oh, mai! Mwawona, “Woyamba ndi Wotsiriza; Ameni, chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu.” Pamene Mulungu anadzilengera Yekha thupi, Iye anatsika ndipo anadzakhala mmenemo, ndicho chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu. Mukuwona? Oh, kodi Iye si wodabwitsa?

¹¹⁰ Tsopano, ife tikupeza poyamba, Iye anawonetsera Umulungu Wake pomwe *pano*, “Ine ndine Wamphamvuzonse! Ine ndine Iye amene Anali, Amene Ali, ndi Amene Adzabwera. Wamphamvuzonse!” Kwa mpingo waku Efeso, ananena izo katatu. Nkulondola uko? Anabwera mpaka ku Laodikaya ndipo anati, “Ndine Ameni. Ine ndinali Woyamba kumbuyo *kuno*, Ndine Wotsiriza cha *kuno*. Ndipo Ine ndine chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu. Kudutsa mmibadwo ya mpingo yomwe titi tikhale nayo, inu mudzaphunzira kuti Ine ndine

Mulungu, Mulungu wolengedwa mmawonekedwe a munthu. Ndine chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu!” Amen.

¹¹¹ Izo zikhoza kumupangitsa wa Presbateria kufuula. Tangoganizani za zimenezo! “Chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu.” Tsopano, ine . . . Oh, momwe ine ndikuzikondera zimenezo, “chilengedwe cha Mulungu,” pamene Mulungu analengedwa, pamene Mulungu anasandulika thupi mwa Yesu Khristu nakhala pakati pathu.

¹¹² Tsopano—tsopano, ndime yotsatira ikanakhala (kwa mipingo ina) kuyiyamikira, koma Iye sanawuyamikire mpingo uwu. Iye anali ndi chidandaulo motsutsana nawo, osati choyamikira. Iye sanawuyamikire uwu pachabe, m’badwo wa Laodikaya uwu. Ndi Kuwala konse komwe iwo anali nako, ndipo nkuchoka kwa Iko, iwo sanasowekere kuyamikiridwa kulikonse. Uh-huh. Iwo ankasowekera chidzudzulo, ndipo iwo anachilandira icho! Iye anali ndi chidandaulo pa mpingo uwu, osati choyamikira.

¹¹³ Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwerenge ndime ya 15 ndi ya 16 apa tsopano:

Ine ndikudziwa ntchito zako, . . . iwe suli wozizira kapena wotentha: Ine ndikanakonda kuti iwe ukanakhala wozizira kapena wotentha. (Mwa kuyankhula kwina, “Usati—usati ungo khala wofunda.”)

Chotero ndiye chifukwa choti iwe ndiwe wofunda, ndipo osati wozizira kapena wotentha, ine ndidzakulavula iwe mkamwa mwanga. (Hmm!)

¹¹⁴ Anaphunzitsidwa . . . Kodi uko ndi kuyamikira? Icho ndi chidzudzulo kwa m’badwo wopanda umulungu wa Laodikaya uwu, woyipitsitsa wa gulu lonse. Ena onse a iwo pansu pa mazunzo ndi zonse zomwe iwo anali nazo; iwo analibe kalikonse, iwo anali okanthidwa ndi umphawi, ankangoyendayenda mu zikopa za nkhoa ndi zikopa za mbuzi, ndipo anali osowa, ndipo anadulidwa ndi kuwotchedwa mpaka ku imfa, ndi kudiyetsedwa ku mikango, ndi china chirichonse, ndipo komabe anagwiritsitsabe Chikhulupiriro. Ndipo gulu ili ndi “lolemera ndi losasowa kanthu,” ndi china chirichonse, ndi hule! Uko nkulondola.

¹¹⁵ Tsopano, ife tiri ndi phunziro lalikulu kwambiri, ine ndikuyembekeza Ambuye atithandiza ife umo. Iye—Iye anati, “Chifukwa iwe suli wotentha kapena wozizira, wofunda.”

¹¹⁶ Monga mkaka, mwawona. Mkaka wabwino wozizira ndi wabwino. Sichoncho iwo? Mkaka wotentha ndi wabwino kwa inu. Koma mkaka wofunda ungapangitseni inu kusanza.

¹¹⁷ Kumbukirani usiku wina ine ndinadwala, kumusi pa mtsinje, pafupifupi zaka twente-faifi zapitazo. Ine ndinali mu bwato lanyumba laling’ono, ndimakhala kumusi uko.

Ine ndinadwala, ndipo iwo anabwera, mlamu wanga anali atanditengera ine kwa Dr. Isler. Anati, “Vuto ndi chiyani?”

Ine ndinati, “Ine ndikudwala kwambiri mmimba mwanga!”

¹¹⁸ Anati, “Imwani kapu yamkaka wofunda.” Oh, m'bale! Mkaka wofunda, iwo unandipangitsa ine kudwala, kotero ine ndinangozitsuka izo zonse zomwe zinali mkatimo.

¹¹⁹ Tsopano, Mulungu anati, “Ine ndikanakonda inu mukanakhala otentha, owotcha kwenikweni, kapena ozizira kwambiri, mukhale chimodzi kapena chinacho. Musakhale ofunda, chifukwa inu mumandipangitsa Ine kudwala.”

¹²⁰ Ndicho chimene m'badwo wa mpingo uwu ukumuchitira Mulungu, ukumupangitsa Iye kudwala! Mukuwona? “Mwina mukhale... Osati... Mwi-... musati mukhale ofiira-... Mwina mukhale otentha kwambiri kapena... Musati mukhale ofunda! Ofunda kapena otentha, chifukwa inu mumandipangitsa Ine kusanza.”

¹²¹ Kuzizira kwa mpingo wa Anglican mmasiku a John Wesley kunamuyendetsa iye kupita kukachita misonkhano kwinakwake, chifukwa unali wozizira, wozizira kwambiri.

¹²² Kuzizira kwa mpingo wa Methodist kunamupangitsa William Booth kukhala wa salvation wotentha. Inu mwawona, Mulungu anati, “Ngati inu simubwera ndi kudzalapa, ine ndichotsa choyikapo nyalicho. Ine ndidzachichotsapo icho, nkuchipereka icho kwa winawake.” Chotero pamene mpingo wa Methodist sunalandire kuyeretsedwa kwa John Wesley, William Booth anabwera ndi a Salvation Army ndipo anautenga iwo nkumapitirira. Uko nkulondola. Chifukwa chiyani? Iwo anawupanga bungwe iwo! Ndizo ndendende. Anapanga bungwe kuchokera mu zimenezo, ndipo Mulungu anati, “Ine ndimadana nacho chinthucho!”

¹²³ Chotero... William Booth anabwera motsatira ndipo anadzawutola iwo, ndi Salvation Army, ndiye kodi iye anachita chiyani? Chinthu chomwecho, anatembenuka mozungulira ndipo anawupanganso bungwe iwo kachiwiri. Pambuyo pa iye kunadzabwera a Campbell, ndipo iwo anakhalapo kwa kanthawi; ndipo kenako John Smith ndi a Baptisti; ndipo kenako pambuyo pa zimenezo kunadzabwera a Nazarene; ndipo kenako pambuyo pa a Nazarene panadzabwera Pentekoste.

¹²⁴ A Nazarene, kodi iwo anachita chiyani? Anawupanga wawo mwanjira yomweyo, anawupanga iwo mpatuko.

¹²⁵ Nchiyani chinabwera mu nthawi imeneyo? Nthambi ziwiri zazing'ono, Mpingo wa Mulungu ndi zina zotero, zinamera kuchokera pamenepo. Kodi iwo anachita chiyani? Anapanga bungwe; anangowasiya iwo azipita.

126 Pomwepo panadzabwera Achipentekoste ndi mdalitso wa mvula yamasika, iwo anachita chiyani? Anapanga bungwe, chotero Iye anangowalola iwo azipita. Ndiko kulondola.

127 Tsopano ife tifika pano kumapeto, inu mupeza chinachake champhamvu kwenikweni mu maminiti pang'ono. Chabwino.

128 Chabwino, Iye akufuna inu mukhale otentha-kwambiri kapena—kapena ozizira kwambiri, chimodzi kapena chimzake. Musati mukhale ofunda! Musati mungonamizira chinachake chimene inu mulibe, mwina mukhale pamoto kwa Mulungu kapena mubwerere mu—mu—mu bungwe. Musati—musati mukhale ofunda!

129 Ndi chinthu chomwecho tsopano! Ndi chinthu chomwecho chinachitika mu. . . mipingo iyi apa. Iye amafuna inu mukhale otentha kapena ozizira. Iye samafuna konse “wofunda.” Ndicho chimene Pentekoste yafikako, chikhaliidwe chofunda. Iwo amafika pa limba kamodzi mu kanthawi, ndi ng'oma pang'ono, ndipo amayimba mozungulira pang'ono pokha; ndi kukhala ndi nyimbo zokwanira, winawake amayimirira nakhala ngati. . . inu mukudziwa, kukhala ngati kunena, “Ambuye alemekezeke! Aleluya!” U-nhu. Ndipo nyimbo zimatsikira pansi, “UH, Uh, u, u,” ndizimenezo. O, mai, zimangomupangitsa Mulungu kudwala mmimba Mwake! Mukuwona? U-nhu. Chabwino.

130 Palibe zochulukuka zomwe zikuchitika pamenepo, monga a—monga chitsitsimutso chotentha kwambiri chikuchitika mwa iwo, koma iwo anali ndi zochitachita mwathupi zambiri mu mpingo uno, inu mwawona, Chifukwa iwo anali olemera ndipo, o, mai, iwo anali akusonkhana palimodzi ndi kumapanga misonkhano yayikulu ndi chirichonse. Iwo anali kukhala ndi nthawi yabwino mu mpingo uwu, zonsezo ndi zoon, koma zonsezo ndi zochitachita mwathupi. Koma palibe kutentha kwa Mzimu Woyera. Mukuwona?

131 Yang'anani apa zomwe Iye ananena mkati umu, mwawona:

Ine ndikudziwa ntchito zako, . . . iwe suli wozizira kapena wotentha: Ine ndikanakonda iwe ukanakhala wozizira kapena wotentha.

Ndipo chifukwa iwe ndiwe wofunda, . . . osati wozizira kapena wotentha, Ine ndidzakulavula iwe mkamwa mwanga. (Mukuwona?)

132 Tsopano, Iye anati, “Ine ndikanakonda iwe ukanakhala wozizira kapena wotentha. Ndipo chifukwa iwe siuli, Ine—Ine ndikungoyenera kuti ndikuchotseni inu, ndizo zonse, kungokusesa iwe kutuluka mkamwa Mwanga.”

133 Tsopano, iwo anali ndi ndalama zambiri, iwo anali ndi nyumba zazikulu, iwo anali ndi zinthu zazikulu zikuchitika, koma iwo analibe kutentha kwa Mzimu Woyera. O, anali ndi machita- . . . a—ulamuliro. O, mai! Iwo ali nawo mpingo

wogwirizana palimodzi, mnyamata, iwo ali ndi nyumba zazikulu kwambiri zomwe iwo anakhalapo nazo, ndi zinthu zikuchitika, koma alibe Mzimu Woyera. Mukuwona? Ndicho chomwe Mulungu anatomiza kwa Mpingo, Mzimu Woyera.

Tsopano, pamene ife tikupitirira mu ndime iyi ya 16.

¹³⁴ Iwo ali ndi makomiti amitundu yonse. “O, ife tiri ndi ulamuliro waukulu wa izo. Bungwe lothandiza azimayi achikulire, ndi ma—masewera a makadi a anyamata achichepere, ndi—ndi masewera a wachiona ndani Lachisanu usiku, ndi—masewera a basketball Lamulungu masana, ndipo, o, masewera a baseball pa *yakuti ndi yakuti*. Ndipo, o, ife tangokhala ndi gu—gulu la phokoso la amuna. Ndipo, o, ife tiri nayo mitundu yonse ya zinthu.”

¹³⁵ Ine ndikukuuzani inu, iye ali wolemedwa, magulu, ndi makalabu, ndi zowukira, ndi zina zambiri, koma popanda kutentha kwa Mzimu Woyera. Mwawona, inu muli ndi ulamuliro waukulu, koma inu mulibe chirichonse mmenemo kuti mutenthe. Inu mukutentha ku dziko lapansi koma osati kwa Mulungu, ndicho chifukwa inu mumakhala wofunda.

¹³⁶ O, inu muli nawo mamembala ochuluka kuposa omwe inu munakhalapo nawo. “Ndithudi, mnyamata! Bwanji, ife tikupezanso miliyoni ochuluka mu '44,” anatero Baptisti. Koma—koma kodi inu muli ndi chiyani? Makina akulu!

¹³⁷ Mu mpingo womwewo kumene ine ndinamva ndemanga imeneyo ikupangidwa, iwo anayenera kupumulira maminiti fifitini, kuti awapatse abusa mwayi kuti apite panja, ndi madikoni onse ndi onse a iwo, kuti akasute, ndi kubwerera mkati kachiwiri. Mukuwona? Ndi inu apo. Baibulo limatsutsa poyera zinthu zimenezo! “Ngati inu muyipitsa thupi ili. . .”

¹³⁸ Madokotala amalitsutsa ilo ndipo amati, “Ndi lodzadza ndi khansa.” Kenako iwo amafika pa waillesi ndi kumati, “Fyuluta yamunthu woganiza.”

¹³⁹ Monga Billy Graham ananenera, “Iye ndi wopusa kuti aziganiza mwa njira imeneyo poyamba.”

¹⁴⁰ “Fyuluta yamunthu woganiza,” munthu *woganiza* sangasute iyo nkomwe, ndiko kulondola, inu mumatenga lingaliro lachiwiri. Koma iye amauza azimayi kuti iyo imawapangitsa iwo kukhala owonda kwenikweni, inu mukudziwa, kotero kuti iwo akhoze kuvala ina mwa mitundu yatsopano iyi ya madiresi omwe iwo ali nawo. Mnyamata, izo zimayenda malonda! Akazi ambiri amasuta ndudu kuposa momwe amachitira amuna tsopano, ndipo mkazi amakhoza kusuta ndudu zitatu kwa imodzi, kuyerekeza ndi mwamuna. Ndiko kulondola ndendende, chifukwa iye akufuna kuti awonde. Iye samazindikira kuti ndiyo TB ndi khansa ndi zinthu zomwe zimamupangitsa iye kukhala wotero, basi mwa mawonekedwe a khanda, kulowa mwa iye, kumudya iye monga choncho, kumupha iye. Palibe

chinthu chomwe chingatuluke mwa icho koma choyipa! Ndiko kulondola. Mukuwona? Koma ndizo, “Iyo—iyo ndi fyuluta yamunthu woganiza.” Ha! O, mai!

¹⁴¹ “Ayi! Ayi! O,” iwo amati, “koma ife tiri nayo... M’bale Branham, ine ndikunyoza izo! Ife tiri nayo misonkhano yabwino! Yang’anani zomwe Billy Graham anali nazo mdziko lonseli.” O, ndithudi, ulamuliro waukulu, alaliki olembedwa ntchito, otsogolera nyimbo olipidwa.

¹⁴² Eya, iwo amalemba ntchito alaliki awo. “Chabwino, kodi inu mudzandipatsa ine ndalama zingati ngati ine ndingabwere kudzachititsa chitsitsimutso chimenecho? Chabwino, ngati inu simungatulutse madola masauzande *mwakuti* ine sindibwera nkongwe. Uko kulondola. Ndipo ndi ndani amene inu mungamulole kuti atsogolere mayimbidwe? Chabwino, inu mupite ndipo mukamulembe ntchito *Wakuti-ndi-wakuti*, iye ndi woyimba yekha wamkulu. Inu mudzamulembe iye ntchito kuti... Iye adzakoka theka la gulu langa, iye adzachita zimenezo yekha.”

¹⁴³ Oyimba olipidwa! Alaliki olipidwa! Bwanji, izo zimafika pamalo akuti kupulumutsa miyoyo ndi malonda. Kupulumutsa miyoyo si malonda a mpingo, ndi mphamvu ya Mzimu Woyera mu mpingo. Kupulumutsa miyoyo si a... inu simugula iko ndi ndalama. Ayi, bwana! Ayi! Zonse za izo ziri, ndi ntchito, ntchito, ntchito, alaliki olipidwa, otsogolera nyimbo olipidwa, makwaya olipidwa, china chirichonse. Mulungu samafuna zimenezo, zonse ndi ntchito! Mulungu samafuna ntchito, Iye amafuna Mzimu Woyera kugwira ntchito mwa inu. Ndiko kulondola.

¹⁴⁴ Ndime ya 17 ikuti:

Chifukwa iwe umati, ine ndine wolemera,... wolemera mu katundu, ndipo sindisowa kanthu; ndipo sukudziwa kuti iwe ndiwe watsoka, (O!)... sudziwa kuti ndiwe watsoka,... womvetsa chisoni,... wosauka,... wakhungu, ndi wamaliseche: (Hmm! Hmm!)

¹⁴⁵ Iwo ankaganiza kuti anali “olemera,” Chipentekoste ichi mu mipingo ya m’badwo wotsiriza uno. Iwo ankaganiza... Ndipo mwakunja iwo anali. Inde, bwana. Iwo ndi olemera. Tangoganizani za mpingo, momwe unkakhalira zaka zingapo zapitazo, utayima kunja ukpo pangodya, amaponyedwera uku ndi uko, anali ndi nthawi yovuta. Koma tsopano iwo ali ndi nyumba zazikulu kwambiri zomwe zilipo.

¹⁴⁶ Inu mukuwona kumene a Assemblies of God kunja kuno, omwe anali nawo malo awo mnyumba yamatabwa ya wamba, chinachake chonga ichi kuno, ndipo tsopano iwo akumanga nyumba ya madola sikisi miliyoni, ndipo iwo akuti, “Yesu akubwera pompano.” Ntchito zanu zimatsimikizira kuti inu simukukhulupirira zimenezo. Ndi chinyengo! Kumanga

zimango za madola mamiliyoni ndi zinthu monga choncho, ndipo kumati, “Yesu akubwera pompano.” Ndipo amishonare osauka kumunda, opanda nsapato kumapazi awo, amishonale enieni owopa Mulungu, opanda nsapato pamapazi awo, ndi kumakhala moyo ndi magawo awiri a mpunga pa sabata; kumadya kawiri pa sabata kuti azinyamula Uthenga kudutsa mnkhalango ndi zinthu monga choncho, kuti awutengere Iwo kwa abale awo. Ndipo ife tikumanga zimango za madola sikisi miliyoni, ndipo mpingo uli ndi akuluakulu, mawindo a magalasi okongoletsedwa, ndi china chirichonse, ndi kumayika izo pa icho. O, inu mumakhala ndi ndalama zochulukwa kwambiri mpaka nthawizina iwo amakhala ndi migwirizano ya ngongole mmipingo yawo momwe. Ndiko kulondola!

¹⁴⁷ Dokotala mmenemo kuti awaunike alaliki awo kapena amishonare awo. Ndipo wina akafuna kupita kumunda, iwo amamupatsa iye kuwunikidwa ndi adokotala kuti awone ngati iye. . . kapena katswiri wazamisala, kuti awone ngati iye ali. . . o, ngati iye ali ndi malingaliro ake abwino, inu mukuwona. Mzimu Woyera umawunika zimenezo, inu simusowa katswiri wazamisala.

¹⁴⁸ “Koma, olemera ndipo osasowa kanthu.” O, ndithudi. Inu muli ndi ndalama zambiri. Kunja, olemera kwambiri; muli ndi zimango zazikulu, mawindo amagalasi okongoletsedwa.

¹⁴⁹ Ndi alaliki odziwa kuyankhula! O, mai. Mai, ine ndikuuzani inu, hmm, iwo ndithudi ndi odziwa kuyankhula. Iwo akhoza kuyima ndi kuyankhula usiku wonse, ndipo nkusanena kalikonse. Mukuwona? Pamene iwo abwerapo. . . Ine ndikutanthauza za zinthu zomwe iwo sakuyenera kunena, inu mukuwona. Kuyimirapo, ndi zina za zinthu izi, ndipo nkuyankhulapo pang'ono za *wakuti ndi wakuti ndi wakuti ndi wakuti* uyu. Ndipo inu mukudziwa momwe izo ziliri. Oyimba olipidwa. Ndiko kulondola. Chabwino. Koma, kubwera paguwa, alaliki odziwa kuyankhula. Ngati iwo sanavale suti ya tuxedo ndi kolala yotembenuzidwa, ndi mtundu wina wa chikhotho cha chipsyepsye kumbuyo, bwanji, osonkhana awo amachita manyazi kwenikweni.

¹⁵⁰ Ndipo oyimba amenewo amabwera kumeneko, akazi amenewo, tsitsi lalifupi lodulidwa ngati Yezebeli, utoto pa nkhope zawo wokwanira kupentera nkhokwe. Mofulumira akangovula mwinjiro umenewo, iwo amavala akabudula ndi zovala za amuna, ndipo Baibulo linati, “Ngati mkazi avala chovala choyenera kwa mwamuna, ndi chonyansa pamaso Pake.” Kumayenda mumsewu ndi mphuno zawo mmwamba, kukanati kugwe mvula, ikanawamiza iwo. Odzimva anzeru, odzikuza, a Yezebeli aukali! Ndicho chifukwa chake ife sitiri mu chitsitsimutso, ndi ntchito yaikulu ya chithupithupi.

¹⁵¹ O, mukhoza kukhala nalo liwu ngati mngelowamkulu,

ndipo Mulungu adzakupangitsani inu kuti mudzayankhire pa zimenezo! A Elvis Presley awa ndi ena otero, ndi a Ernie Fords, kapena ngakhale chirichonse chomwe iwo amawatcha iwo pano ndi maliwu abwino awa ndi kumawagwiritsa iwo ntchito kwa mdierekezi, Mulungu anati, “Ine ndidzazifunsa izo mmanja mwawo.”

¹⁵² Ndicho chifukwa ine ndimamulemekeza Fanny Crosby wakhungu; iye sanagulitsepo mphatso yake ku dziko. Iye anayisunga iyo ndi Mulungu.

¹⁵³ Ambiri mwa anthu awa ndi oyimba aluso, amuna odziwa kuyankhula, amuna aakulu, ndi zina zotero, mmalo moti azigwiritsa ntchito luso lawo kwa Mulungu, mdierekezi wawapotoza iwo ndipo iwo ali kumeneko akumugwirira iye ntchito. Anthu, anthu a pawalesi ndi patelevizioni akudzigulitsa okha, kunja uko kwa dziko mmalo mopereka ilo kwa Mulungu. Ena a iwo amabwera ku tchalitchi, amapita kutchalitchi, amavala mwinjiro wabwino waukulu, amabwera kunja uko ndi kumayimba monga choncho, ndi kubwerera mmbuyo momwe ndi kukayimba gwedemula usiku wotsatira. Monga oyimba omwe ife timawadziwa, ndi a matchalitchi enaake, kumapita kunja uko ndi kukawapangira iwo zithunzi, zithunzi za kanema izo, kumapita kunja uko ndi kumakayimba gwedemula. Mafumu a gwedemula, ndipo nkumadzinenera kukhala achipembedzo! Ndi njomba ya mdierekezi!

¹⁵⁴ Munthu mmodzi anali ndi zokwanira—nzeru zokwanira zabwino pano. Amene ananena kuti iye adzakhala mlaliki, iye azidzabwera Lamulungu mmawa ndikudzalalikirira, ndipo kenako iye nkumapita kumusi uko kumapitirira . . . ndi kupita pawalesi ndi kukayimba nyimbo za gwedemula ndi chirichonse monga choncho, kotero iye potsiriza anatenga mfuti ndi kuphulitsira ubongo wake panja. Ine ndikumulemekeza munthuyo pochita zimenezo. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola. Iye—iye anali nazo zambiri . . . Iye anali ndi nzeru zambiri monga nkhumba zija, mulimonse, pamene izo zinakhala ndi mdierekezi mwa izo izo zinathamangira kumadzi ndi kukatsamwa. Anthu ena alibe ngakhale zochuluka choncho.

¹⁵⁵ ine ndikudziwa inu . . . Ine—Ine ndimadana nazo kuti ndikhale wolimba choncho, koma, m'bale, mlongo, inu mukuyenera—inu mukuyenera kuchikhomerera chinthucho pansu apa kuti muchipangitse icho—muchipangitse icho chilimbe! Ili ndi tsiku lomwe ife tikukhalamo. Ine ndikulingalira ngati Yesu anamutcha Herode “nkhandwe yakale,” ndipo Yohane anawatcha iwo “m’badwo wa amamba,” chabwino.

¹⁵⁶ Iwo ali ndi nyumba zazikulu, mawindo a magalasi okongoletsedwa, alaliki odziwa kuyankhula, oyimba olipidwa. Inde, bwana. Kodi iwo ali ndi chiyani mu izo? Kodi muli chiyani mmenemo? Palibe cha Mzimu Woyera. Kuyimirira pamene ndi

kutuluka kunja ndi kukavala akabudula, ndi kubwera umo ndi kumayimba mu kwayala. Iwe wachinyengo womvetsa chisoni! Inde, bwana. Uko nkulondola.

¹⁵⁷ Ndipo iwe, mlaliki, amene ungapite ku msonkhano chifukwa chakuti iwo akupatsa iwe ndalama zambiri kuposa momwe amachitira ku malo ena! Iwe tambwali, iwe siuli woyenera kukhala paguwa. Uko nkulondola. Ndalama! “Ngati inu simungakwanitse madola masauzande *mwakuti*, chabwino, ife sitingabwere. Athu—athu—oyang’anira athu ndi zinthu adzabwera, ngati inu mungakwanitse kupeza ndalamazo ife tibwera. Ngati ine sindingapeze mgwirizano wathunthu ndi aliyense, ine sindibwera. Ngati aliyense sakugwirizana kwathunthu (mipingo yonse) chotero ine ndikhala ndi ndalama zambiri kuti ndibweze ngongole zanga, ine sindibwera.”

¹⁵⁸ M'bale, munthu weniweni wa Mulungu akhoza kupita ngati Mzimu Woyera unamutsogolera iye, mosasamala zomwe zinali mu chopereka. Ngati iye amayenera kudya zikondamoyo za soda ndi kumwa madzi a mumtsinje. Uko nkulondola, iye ndi wantchito weniweni wa Mulungu.

¹⁵⁹ Koma anthu amadzimangiriza okha ndi zowulutsa ndi wailesi ndi televizioni, ndi mitundu yonse ya zinthu zadziko lapansi, mpaka iwo anakhala ndi ndalama za mtundu umenewo. Uko kulondola ndendende. Mukuwona? Ameneyo si Mulungu.

¹⁶⁰ Iye anati, “O, ndinu olemera, osasowa kalikonse.” Ndithudi, koma chinthu chomwecho chomwe inu munkachisowa, inu munalibe. Uko nkulondola. Koma inu simunadziwe izo. Mwawona, “Olemera, osasowa kanthu.” Kulipidwa kuti achite zinthu zomwe iwo akuchita, kusewera makadi. “O,” inu mukuti, “ife tiri ndi magulu aakulu.” O, ndithudi. Inde, bwana. “Mpingo waukulu kwambiri! Bwanji—bwanji, inu mukudziwa, a meya a mzindawu amabwera ku tchalitchi kwathu.” Um-hum. Uko nkulondola. “Chabwino, inu mukudziwa, *Wakuti ndi wakuti*, iwo akabwera mtawuni, iwo amabwera ku tchalitchi kwathu.” Um-hum. “Ife tiri ndi otchuka onse mu mpingo wathu.”

¹⁶¹ Inde, ndipo lolani osauka, oyera mtima osauka abwere mu mpingo, ndipo iwo ndi chidzudzulo kwa inu. Inu simumawafuna nkomwe iwo mmenemo. Inu mumachita mantha kuti winawake anena “Ameni!” pamene inu mukulalikira.

¹⁶² Monga dona wamng’ono yemwe ine ndinamuwerenga nthawi ina mu kabukhu kakang’ono kuno, iye anabwera mu mpingo. Ana ake, iye anali atawalerera iwo mu mpingo wachikale kumbuyo ku nkhalango kwinkakwake kumene iwo anali aumulungu kwenikweni. Kotero... Mnyamata wachichepere anabwera mkati tsiku lina ndipo anamukwatira mtsikanayo. Anati iye anali wa mpingo *wakunja*, inu mukudziwa, umodzi wa mipingo yayikulu ya chipembedzo chomwecho kunja uko mu mzinda. Kotero iye anawauza amayiwo kuti iye anali

Mkhristu. Kotero iye anamukwatira mwana wamkaziyo ndipo anamutengera iye kunja.

¹⁶³ Chabwino, potsiriza iye anamuchotsa ku tchalitchi chaching'ono chakale kumapiri, kupita kunja kuno, mpingo wawukulu wabwino kwambiri uwu, dzina lomwelo; koma kumbuyo uko iwo anali nawo Mzimu Woyera, kunja kuno iwo analibe kalikonse. Kotero ndiye pamene iwo amabwera umo, mpingo wawukulu wabwino kwambiri uwu.

¹⁶⁴ Kotero Amayi anati, tsiku lina, iye ankabwera kuti—kuti adzamuwone mwana wake wamkazi. Chabwino, iwo anadabwa kuti iwo akanachita naye chiyani mu dziko lapansi. Kotero pamene iye anabwera pansu iye ankawoneka ngati chinachake chochokera mu bukhu la zamakedzana, chimodzi cha zazing'ono izo, madiresi a khosi lalitali, inu mukudziwa, ndi mikono yayitali, ndi tsitsi lake litagwetsedwera kumbuyo uko, nkhope ya anyezi yosalala, monga choncho (logwetsedwera m'mbuyo, inu mukudziwa). Ndipo iye akutsika pansu, ndipo iye anati, “Chabwino, Aleluya, wokondedwa! Inu nonse zikukuyenderani bwanji?” Chabwino, iye anati, “Tsopano, mmawa ndi Lamulungu.” Anati, “Inu nonse mupita ku msonkhano, sichoncho inu?”

¹⁶⁵ (Mwamunayo anati, “Kodi tichita naye chiyani iye?” Anati, “Ife sitingamutenge iye kupita kumeneko monga choncho!”) Ndipo anati, “Chabwino, ine sindikudziwa choti ndichite.”) Chabwino, iye anati, “Amayi, ine ndikukuuzani, ife . . .”

¹⁶⁶ “O,” iye anati, “koma, wokondedwa, ine sindikanakhoza kukhala osapita ku tchalitchi. Ndithudi pali tchalitchi *chakuti-chakuti* moyandikira kuno.” “O,” iye . . . iye anatero . . . Anati, “Ine ndinachiwona china apo pa ngodya pamenepo, ine ndingopitako.”

(Ndipo iye anati, “O, chabwino, ife tikuyenera kungochita izo.”)

¹⁶⁷ Kotero pamene iwo analowa umo, iwo anamulola iye kuti alowe poyamba, (Mukuwona?) akuchita manyazi ndi iye. Apa iye anabwera akuwoloka msewu ndi siketi yaying'ono ija, inu mukudziwa, ndi Baibulo lake kukhwapa kwake. Chabwino, m'bale, iye mwina analibe dzina lake mu *Ndani ndi Ndani*, koma ine ndikuganiza iye anali ndi dzina lake pa Bukhu la Moyo la Mwanawankhosa. Icho chinali chinthu chachikulu.

¹⁶⁸ Pamene iye analowa mu tchalitchimo iye anakhala pansu kumbuyo uko, anamukhazika iye pansu, inu mukudziwa, ndipo anatsegula Baibulo ndipo iye anayamba kuwerenga. Ndipo aliyense anayamba kuyang'anayang'ana mozungulira, ankaganiza mtundu wa chinachake chamakedzana chinali chitagwera penapake. Akuyang'anayang'ana mozungulira monga choncho, “O, mai!” Ndi zovala zawo zonse zabwino atavala, inu mukudziwa, Laodikaya weniweni, ndi madiresi awo

abwino ndi zina zotero. Anayang'ana m'mbuyo ndipo anawona mayi wamng'ono uyu atakhala pamenepo, ndi kumwetulira kwakukulu pa nkhope yake, inu mukudziwa, akuwerenga Baibulo. Eya.

¹⁶⁹ Ndipo m'busa, patapita kanthawi, atamaliza kuchita zinthu zina zonse, iye potsiriza, iye anali ndi pafupifupi maminiti fifitini oti ayankhule. Kotero iye anadzuka ndipo iye anati, "Ambuye ndi wabwino."

¹⁷⁰ Iye anati, "Atamandike Mulungu! Uko nkulondola! Aleluya!" Ndipo aliyense anasolola khosi lake ngati tsekwe, akuyang'ana pozungulira, "Anali ndani ameneyo?"

¹⁷¹ Ndipo patapita kanthawi, iye anati, "Uhm! Uhm! Uhm!" Iye anati, "Akhristu mu m'badwo uliwonse akuyenera kukhala olimba mtima, aakulu, Akhristu abwino," kapena chinachake pa dongosolo limenero.

¹⁷² Iye anati, "Atamandike Mulungu! Uko nkulondola!" Ndipo iwo onse anayang'ana mozungulira.

¹⁷³ Ndipo iye, "Uhm!" anayang'ana kwa gulu lake la madikoni.

¹⁷⁴ Ndipo gulu la madikoni linapeza ganizolo. Linabwerera ndi kukamugwira mkazi wamng'onoyo pa mkono ndi kumutulutsira iye kunja, anati, "Iwe ukuwasokoneza abusa."

¹⁷⁵ Ndinu akufa ndipo simukudziwa izo! Inde. O, kodi mawindo anu a magalasi okongoletsedwawo adzakupindulirani chiyani? Kodi mipando yanu yawofuwofu ndi chiyani? Ndipo kodi mpingo wanu waukulu wonsewo ndi chiyani? Kumangopita molunjika ku gehena, ngati nanzeze ku bokosi lake. Pakuti ngati inu mulibe Mzimu wa Mulungu, inu mwataika! Pokhapokha inu mutabadwanso mwatsopano inu simungakhoze kuwona Ufumu wa Mulungu.

¹⁷⁶ Izo ndizowawa. Ziri ngati ine ndinkakonda kumwa mafuta a msatsi, ine ndinati, "Amayi, ine sindingathe ngakhale kuzipirira izo."

¹⁷⁷ Iye anati, "Ngati izo sizikupangitsa iwe kudwala, izo sizikuchitira iwe ubwino." Kotero ine ndikuganiza ndizo pafupifupi momwe Izi, nazonso.

¹⁷⁸ O, ngati inu mukanati muyankhule kwa iwo! O, zazikulu, zimango zabwino, ndi zina zotero. O, iwo—iwo—iwo... Inu mukapita ku tchalitchi kwawo, inu mukanakhoza kunena... Kupita ku tchalitchi kwawo ndi kuti, "Chabwino, ine ndikukuuzani inu, ndinu a Chipentekoste?"

"O, inde. U-nhu. Ndithudi, ndife a Chipentekoste."

"Inu mumakhulupirira mu kubadwanso mwatsopano?"

"Inde."

"Chabwino, ine ndikufuna ndikuwonetseni inu chinachake..."

179 “O, tayang’anani pa chimangochi ichi! Inu mukudziwa kuchuluka kwa chimango... mtengo wa chimango ichi? Izo zinatengera makotala atatu a madola miliyoni kuti izi zitheke. Inu mukudziwa, ife sitinakhalepo nazo izo mwanjira imeneneyo. Ife—ife tinkakonda kukhala kumusi uko mu msewu.” Um-hum, ndipo muyang’ane pozungulira, inu mumapeza zinthu zazikulu zonse izi zomwe iwo ali nazo. Inde, bwana. Ndipo kenako iwo amati, “O, ife—ife tiri ndi zinthu zazikulu zonse izi!” Koma iwo alibe kulemedwa kwa miyoyo yotayika! Nthawi zonse iwo amafuna kukuwonetsani inu kuchuluka kwa zimango zomwe iwo ali nazo. “Tayang’anani pa kawundula wathu wa Sande sukulu, momwe iyo iliri yayikulu!” Kodi izo zimachita ubwino wanji ngati iwo alibe Mzimu Woyera? “Olemera, ochuluka mu akatundu, osasowa kanthu.”

180 Ndizo zomwe Iye ananena, “Inu mukuganiza choncho, koma simukudziwa kuti ndinu osauka, atsoka, omvetsa chisoni, akhungu, amaliseche. Ndipo osadziwa izo!” Mwawona? Ndizimenezo.

181 O, ndithudi, iwo amati, “Inu mukudziwa chiyani? Ife tinali kale... Tchalitchi chaching’ono chomwe ife tinkakonda kugwiritsa ntchito chiri kumbuyo, ichi ndi chachikulu tsopano!” Ndipo ine ndikukuuzani inu, palibe cholemera kwa miyoyo, koma iwo amayenera kuwonetsa kuti zinthu zonse izi zikusamaliridwa. Thandizo la amayi, ndi zinthu zina zonse izi, zonsezi zikuyenera kuti zizisamaliridwa, koma palibe cholemera kwa miyoyo yotayika. O, amuna, chomwe—chomwe mpingo uwu walowamo!

182 Iwo sanali olemedwa chifukwa cha miyoyo, koma iwo anali olemedwa ndi chuma. Uko nkulondola. Iwo anali ndi cholemera cholakwika. Iwo anali ndi cholemera cha chuma chawo koma osati cholemera kwa miyoyo yotayika. Lemba linati, “Iwo sanadziwe kuti anali atsoka,” (O!) “omvetsa chisoni, akhungu.”

183 Iwo amaganiza kuti akhoza kutenga ndalama ndi kutembenuza nazo dziko lapansi. “O, ngati ife tikanangokhoza kuyambitsa dongosolo, kuti ife tikanakhoza kupeza ndalama zambiri kuno, ine ndikukhulupirira ife tikanakhoza kulitembenuza dziko lapansi. Ngati ena a anthu olemera mu mpingo wathu, M’bale Branham, ngati ife tikanakhoza kokha kuwapangitsa iwo kuti akumbe, ndipo ine ndikukhulupirira kuti ife tikhoza kuyambitsa gulu lomwe lingathe—lomwe lingathe kupita kuzungulira ndi—ndi kulitembenuza dziko lapansi. Ife Tikhoza kutenga ndege ndi kumakasiya zowerenga ku Africa konse, ndi zinthu monga zimenezo. Ngati ife tikanangokhala ndi ndalama!”

184 M’bale, dziko silidzatembenuzidwa ndi ndalama. Dziko lidzatembenuzidwa ndi Mzimu Woyera; kulalikira kwamphamvu kwa Mzimu Woyera ndi Mtanda ndi chinthu

chokhacho chomwe chidzatembenuze dziko lapansi. Dongosolo la Mulungu si ndalama. Ndi Mzimu Woyera, ndilo limene liri dongosolo la Mulungu kwa M'badwo wa Mpingo wa Laodikaya kapena m'badwo wina uliwonse wa mpingo. Inde, bwana.

¹⁸⁵ Iwo amafuna Mzimu Woyera. O, iwo amati, “Ife ndife. . . tiri ndi golide.” Iye anali golide, chabwino, koma osati mtundu woyenera. Iwo anali ndi golide wambiri koma osati wa mtundu woyenera. Tsopano, kotero iwo analamulidwa ndi Yesu, “Ine ndikudziwa ndinu olemera, ndipo muli ndi golide, ndipo simukusowa kalikonse,” koma:

*Ine ndikukulangiza iwe kuti ubwere udzagule kwa ine
golidi woyengeka mmoto, . . .*

¹⁸⁶ Mtundu wosiyana wa golide, eya, golide yemwe amayesedwa mng'anjo yamoto, amene anadutsa mu moto wa imfa, amene anadutsa pa Kalvare, anatuluka.

¹⁸⁷ Golide wambiri amene inu mwamupeza tsopano ndi wothimbirira, iye adzadyeka, adzachita dzimbiri. Ngati inu mungathe kulemba izi, Yakobo. . . Yakobo Woyera 5:1 mpaka 4, ndipo inu mupeza zomwe izo ziri, anati, “Pitani inu, inu anthu olemera, tsopano pakudza kwa Ambuye, lirani ndi kufuula pakuti masautso anu afika pa inu, golide wanu wadyeka mwa inu.” Mwawona, ndiwo mtundu wa golide womwe umadyeka.

¹⁸⁸ Koma golide amene Yesu amapereka ndiye Mzimu Woyera, Mafuta agolide a Mzimu, amatsanulira muntima mwanu. Ndipo—ndipo, o, mai, “Uphungu wa iwe, bwera udzagule kwa ine golide, ngati iwe ukufuna kuti ulemere.” O, inde.

¹⁸⁹ Komanso, iwo anali “akhungu.” Tsopano, imeneyo ndi njira yoyipa kuti ukhalemo. Ine sindikuganiza kuti Akhristu awa anali akhungu monga iwo anali “kuwonapafupi.” Ine ndikukhulupirira iwo anali owonapafupi. Chinthu chokha chimene iwo akanatha kuyang'anapo chinali zimango zawo zazikulu. Chinthu chokha chimene iwo akanakhoza kuyang'anapo chinali mpingo wawo waukulu. Chinthu chokhacho chomwe iwo ankachiyang'ana chinali kwaya yopukutidwa bwino yokhala ndi miinjira yake yonse yayikulu ndi zinthu. Ine ndikuganiza kuti iwo amangowonapafupi, iwo samakhoza kuwona pamwamba pa mphuno pawo, nkomwe. Ine sindikuganiza kuti iwo anali akhungu, iwo amangowona pafupi chabe. Zonse zomwe iwo amakhoza kuwona zinali zawo. . . “Chabwino, inu mukudziwa chiyani? Ife ndife a *Wakuti ndi wakuti!*” Zipembedzo zawo zazikulu, magulu awo aakulu, mamembala ambiri, Sande sukulu yawo, nyumba zawo zabwino.

¹⁹⁰ “Koma iwo anali nako kusowa kwa Mzimu Woyera,” Yesu anatero. Iwo ankasowekera Mzimu Woyera! Kotero Yehova anati kwa iwo, “Diso. . . Ngati inu muli. . . maso ndi oyipa kwambiri, ndipo inu ndinu woonapafupi kwambiri mpaka inu simungathe kuwona kalikonse koma chimango chanu chachikulu pano ndi

mpingo wanu wabwino kwambiri, ndipo wanu...meya wa mzindawo ndi onse amabwera ku tchalitchi chanu, ndipo inu muli ndi munthu wotchuka. Ndipo inu munandiiwala Ine. Koma ngati inu muli wakhungu choncho, ndipo maso anu ali owonongeka choncho, ine ndidzakugulitsani inu mankhwala opaka mmaso.” Eya.

¹⁹¹ Mukuwona, ndi zachilendo kuti madokotala a zaumulungu analibe chirichonse cha izo, sichoncho? Iwo anali ndi mafuta onunkhiritsa ambiri, anali ndi fiyoloje yambiri. Koma iwo amasowejera mankhwala opaka mmaso, Mzimu Woyera wa Mulungu, kuti asisite maso awo ndikuwalola iwo kuti ayang’anire kudza kwa Ambuye, aloleni iwo ayang’ane pa Baibulo, aloleni iwo ayang’ane pa Mawu. Iwo akudziwa kunena “ah-munthu” ndendende basi molondola. Iwo anali ndi mafuta onunkhira, iwo anali ndi mafuta onse. Koma, “Iwo ankasowejera mankhwala opaka mmaso,” Ambuye anatero. Anati, “Inu mukusowejera mankhwala pang’ono kuti apite mmaso mwanu, ndipo adzawatsegula iwo.”

¹⁹² Zinali kuti, pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono... Ine ndazinenapo izi, ine ndikukhulupirira, ine mwina ndinazinena izo kutchalitchi. Izi zikubwera mmalingaliro mwanga tsopano. Ine ndinakulira mmapiri aku Kentucky, pang’ono, ndipo ife tinkakhala mnyumba yakale yazipapati. Amayi, apa... Ndipo ife tinali ndi—tinali ndi malo aang’ono akale kumtunda, ndipo tinali ndi matiresi a—a udzu. Ndipo kenako pamwamba pa matiresi a udzuwo panali nthenga. Ine sindikudziwa ngati inu mukudziwa chomwe chofunda chanthenga chiri kapena ayi, kapena bedi laudzu; bedi lakale, ife tinali osauka kwambiri. Abambo ndi amayi anali ndi bedi pansu. Ndipo kotero ife tinkakwera ka khwerero kakang’ono ndi kukwera pamwamba, ndipo amayi amayika, zina—zina—nthawizina, chidutswa cha chinsalu chophimba pa zofunda ndi zinthu, kuti pakhale... Inu mukudziwa, inu mukuyima... kugona pamenepo ndi kuwerengera nyenyezi pakati pa zipapati zakale zitayikidwapo ndi kuwala kwa mwezi, inu mukudziwa, ndipo panali mabowo akuluakulu kudenga monga choncho.

¹⁹³ Ndipo kotero pamene kukhala chisanu kapena chinachake, kapena mvula inkagwa, ife ana aang’ono timalowa pansu pa ichi—chidutswa ichi chansalu, inu mukudziwa, kusunga icho...kuti tisanayowe. Ndipo nthawi zina chifunga chodutsa mmabowo amenewo, ife—ifetinkadwala chimfine ndipo maso athu amakhoza kumatana. Inu mukudziwa, kuyimitsidwa onse ndi kuzizira, kuzizira mmaso mwathu. Ndipo kotero amayi amatiyitana ife mmawa, “Tsikani.” Ndinganene kuti, “Ine sindingathe kubwera, amayi, chifukwa maso anga onse amatirira.” Ine ndiri—ine ndiri ndi zinthu mu iwo, inu mukudziwa, kuzizidwa mmaso. Sindinkatha kuwatsegula iwo, inu mukudziwa. Wamng’ono wachichepereyo atagona

pamenepo, ndipo ine ndi Humpy ndi iwo tikuyesera kutsegula maso athu ndipo ife sitinkatha kuchita izo, titachititsidwa khungu.

¹⁹⁴ Agogo anga aamuna anali mlenje, iwo ankatchera nkhandwe, nkhandwe. Ndipo ilo linali yankho ku mavuto onse pakhomo pathu, anali mafuta a nkhandwe. Ife tinkadzodza nsapatozo ndi mafuta a nkhandwe. Ndipo ngati iwe unali ndi nsungu, iwo amayika nsatsi pang'ono pa iwo ndipo basi, eya, iwe umayenera kuzimeza izo, choncho, chifukwa cha nsungu.

¹⁹⁵ Ndiyeno maso athu akakhala onse omatirira, amayi amatenga zinthu izi. . . “Chabwino, miniti yokha, wokonedwa.” Iwo amathamangira kunja ku khitchini ndi kukatenga chikho chachikulu ichi cha mafuta a nkhandwe ndipo anachiyika icho pamenepo, ndi kuchitentheta icho kwenikweni. Ndipo iwo anabwera ndi kudzatikita maso athu, mwawona, mpaka kuti iwo anachita ntchitoyo. Ndipo patapita kanthawi ine ndinayamba kuti ndikhoze kuwona, kutsegula maso anga. Nkupeza. . . Mafuta a nkhandwe anawatsegula iwo.

¹⁹⁶ Ndipo ine ndikukuuzani inu, ife takhala ndi chifunga chowopsya! Mukuwona? Pakhala pali kuzizira kowopsya kukusesa mdzikoli. Abaptisti anati, “Masiku a zozizwitsa anapita. Palibe chinthu chotero monga Mzimu Woyera, ndipo palibe zoyankhula mmalirime. Palibe ubatizo mu Dzina la Ambuye Yesu.” Ndipo, o, mitundu yonse ya zifunga, ndipo izo zatsaka maso ambiri ndi mtundu wina wa kuzizira kwauzimu. Izo zidzatengera zoposa mafuta a nkhandwe ochuluka kuti atsegule maso amenewo, m'bale. Izo zidzatengera ubatizo watsopano wa Mzimu Woyera. . . ? . . . kuti utikitire maso anu ndipo inu mukhoze kuwona, uchose kuwonapafupi kwanu kuti inu mukhoze kuwona kuti Mawu a Mulungu ndi owona. Uko nkulondola. O, “Ine ndikukulangizani inu kuti mubwere mudzapeze mankhwala opaka mmaso kwa Ine, mtundu umene umadzodza maso anu.” Kotero inu. . . Kotero. . .

¹⁹⁷ Madokotala afiyoloje ali nawo. . . fiyoloje yonse, ndi zonunkhiritsa zawo ndi zinthu, koma izo zinatengera zochuluka za izo. Izo zimatengera Mzimu Woyera kuti upereke masomphenya auzimu kuti muwone mphamvu Zakumwamba zikugwira ntchito. Mzimu Woyera, mankhwala a Mzimu Woyera! Mankhwala a mmaso ndi mafuta otentha, ife tikudziwa izo, ndiyeno Mzimu Woyera ndi Mafuta a Mulungu.

¹⁹⁸ Ndi mafiyoloje onse ndi zonunkhiritsa, “O, m'bale, wokonedwa, inu muli bwino. Palibe cholakwika ndi. . . Chirichonse chiri bwino. Chabwino, ife tiri ndi tchalitchi chachikulu kwambiri chomwe chilipo mumzinda.” Zonunkhiritsa zimenezo sizigwira ntchito! Ayi, bwana! Izo zikupangitsani inu kuti muwone pomwe *apa* (wowonapafupi) ndi kuti, “Inde, ife tiri ndi tchalitchi chachikulu kwambiri.”

Nanga bwanji za Chiweruzo chomwe chikubwera pamene Mulungu adzakupangani inu kuti muyankhe, inu mamembala ampingo wa Laodikaya?

¹⁹⁹ Ine sindikuyankhula zambiri pano, koma ine ndiri pa tepi ndipo zikupita ku dziko lonse lapansi, inu mukuwona, kotero ndikuyankhula kwa anthu pafupifupi mamiliyoni angapo pa nthawi ino, inu mukuwona.

²⁰⁰ Kotero ndiye ndizimenezotu. Mlaodikaya! Wofunda! Wobwerera mmbuyo! Wowonapafupi! Ine sindikudziwa zina zonse. Mphongolo! Mphongolo ndi wosakanizidwa, iye alibe luntha kuyamba nkuyamba. Ndipo inu mukayankhula kwa iye, iye amayimitsa makutu aakulu awo mmwamba, nkupita, “Hoo! Hoo! Hoo! Hoo!” Palibepo za chifundo kwa iye. Iye ndiwosakanizidwa, iye ali pakati pa kavalo ndi bulu. Ndilo lomwe liri vuto tsopano, inu mukayika Achinikolai ndi Alaodikaya pamodzi, ndipo inu muli ndi bulu kachiwiri. Chomwe ife tikusowa. . . Ndiko kulondola. Iwo samadziwa. Inu mukawauza iwo za machiritso Auzimu, ubatizo mu Dzina la Yesu. Amati, “Hoo! Hoo! Abusa anga samatero. . . Hoo! Hoo! Ife sitimakhulupirira zimenezo ngati Achipresbateria.” Mbuli! Ndizo pafupifupi zomwe inu mungazitche izo. . . ? . . .

²⁰¹ Ine ndimadana ndi mphongolo. Koma ine ndikukuuzani inu, ine ndimakonda kavalo wabwino, wofatsa wambewu, mnyamata, inu mukhoza kumuphunzitsa iye chinachake. Inu mukhoza kumuphunzitsa iye kuwerama, ndikulowa mu masewero, ndipo pafupifupi kuchita ngati munthu, chifukwa iye ndi. . . iye amadziwa chinachake. iye ali ndi mbewu. Mphongolo siimadziwa yemwe bambo wake anali kapena mayi ake anali, ndipo iye sangathe kudzychulukitsa yekha. Ndi momwe ziliri ndi zina mwa zipembedzo zakale, zozizira, zamwambo, izo sizingakhoze kudzukanso kachiwiri. Mwamsanga pamene mpingo upita mu chipembedzo, iwo wafa! Iwo sumadzukanso kachiwiri. Ndi chiyani icho? Ndi chosakanizidwa!

²⁰² Martin Luther anali bwino, koma pamene iye anapanga bungwe kodi iye anachita chiyani? Methodisti anali bwino, pamene iye anapanga bungwe kodi iye anachita chiyani? Pentekoste anali bwino, koma pamene inu munapanga bungwe inu munachita chiyani? Inu munachisakaniza icho, inu munachibweretsa icho mu mpingo wa Katolika wa Chinikolai. Ndendende zomwe inu munachita! Munatenga mawonekedwe ake a ubatizo, munatenga njira zake ndi machitidwe, ndipo Baibulo linati, “Inu ndinu mwana wamkazi wa hule, hule. Mwana wamkazi wa timahule!” Kulondola ndendende!

²⁰³ Kavalo wambewu wabwino, eya, iye ndi wofatsa. O, iye ndi wabwino, ine ndimamukonda iye. Kuika mutu wake pamapewa ako, wachikondi, wachifundo. Bwanji? Iye amadziwa yemwe abambo ake ali, iye amadziwa yemwe agogo ake aamuna ali, iye

amadziwa yemwe abambo a agogo ake aamuna anali. Iye akhoza kubwerera kumbuyo, iye ndi mbadwa.

²⁰⁴ Ndipo ine ndimakonda kuwona mbadwa yeniyeni ya Chikristu! Osati kunyamula kalata yake: iye ndi wa Methodisti sabata yatha, ndi wa Baptisti sabata ino, ndi wa Chipentekoste sabata ino, ndi wa Pilgrim Holiness sabata yamawa. Iye samadziwa yemwe abambo ake ali kapena yemwe amayi ake ali. Koma ndiloleni ine ndikuuzeni inu, munthu yemwe wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu akhoza kukutengerani inu kubwerera komwe ku Tsiku la Pentekoste; akhoza kukuwuzani inu iye ndi mbadwa, wapentekoste! Ameni! Ine ndikufuna kuti ndikhale pentekoste kuyambira pamwamba pa mutu wanga kufikira ku zidendene za mapazi anga. Ine sindikutanthauza Chipentekoste chachipembedzo. Ine ndikutanthauza mphamvu yeniyeni ya Khristu woukitsidwayo, Mdalitso weniweni wa Pentekoste.

²⁰⁵ Mankhwala ammaso, kutsegula maso anu kuti ife tikhoze kuyang'ana kumbuyo ndi kuwona komwe iwo unachokera. Inu mukungoyang'ana chomwe mpingo uli lero; yang'anani mmbuyo ndi kuwona komwe iwo unachokera, ndiye pitirizani kusunthira kwa Mulungu, inu mudzapita kutali ndi izo. Inde, bwana.

²⁰⁶ Chabwino, ine ndinazindikira chinthu china, anati, “Iwo ali amaliseche; amaliseche ndipo sakudziwa izo.” Ndithudi.

²⁰⁷ O, wamaliseche ndipo osadziwa izo. Tsopano, munthu ameneyo ali mu chikhaliidwe chomvetsa chisoni, ngati munthu ali watsoka, wakhungu, womvetsa chisoni, wamaliseche. Tsopano, ngati iye—ngati iye akudziwa izo, iye adzithandiza yekha; koma ngati iye sakudziwa izo, munthu wosaukayo wasokonekera malingaliro. Ndi kulondola uko? Fyuu! Icho chinali ngati cholimba. Wosokonekera malingaliro, iye sakudziwa mokwanira kuti adzithandizire yekha.

²⁰⁸ Inu munawona winawake akubwera chotsika njira, wosauka, womvetsa chisoni, wakhungu, watsoka, ndi wamaliseche, ndipo inu nkuti, “M'bale, inu muli wamaliseche.” “O, ndiri choncho? O, O, m'bale, ndithandizeni ine kwinakwake, ndithandizeni ine kuti ndivale.”

²⁰⁹ Koma inu mukapita kwa iwo ndi kunena, “Kunena, kodi munalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni?”

²¹⁰ “Ndiwe chiyani, woyera-wodzigudubuza? Chabwino, mukuti, kodi inu mukutanthauza chiyani? Musati inu muzindiyanhula ine monga choncho, ndine wa Presbateria, ndine wa Baptisti, ndine wochokera kwakuti ndi kwakuti ndi kwakuti ndi kwakuti.”

²¹¹ Wamaliseche ndipo sakudziwa izo! Tsopano, ine sindinanene zimenezo, Baibulo linanena izo za m'badwo uno, “Wamaliseche ndipo osadziwa izo. Bwerani mudzagule zovala zina kwa Ine,” Iye anatero.

. . .zovala zoyera. . .

Zovala zoyera ndi za Oyeramtima; ndi chilungamo cha Oyeramtima. Mukuwona?

²¹² Wamaliseche? O, ndithudi! Inde, bwana! O, inu mukuti, “M’bale Branham, osati mpingo wathu, ndi mpingo wovala bwino kwambiri mumzinda!” Ine sindingakayikire zimenezo; ena mwa mafashoni atsopano, zovala zazifupi zapamwamba, zovala zatsopano za otchuka aku Hollywood, za dama mochuluka mwakuti mungakope tcheru cha mwamuna aliyense pamsewu. U-hum. Ndithudi.

²¹³ Dona wina ananena kwa ine, anati, “M’bale Branham, kodi inu mukutanthauza kundiuza ine? Tsopano, ife timagula madiresi awa mu sitolo ndipo ndizo zonse zomwe inu mungakhoze kugula.”

²¹⁴ Ine ndinati, “Iwo akugulitsabe nsalu ndipo akupanga makina osokera. Icho sichowiringula kwenikweni pa izo.”

²¹⁵ Baibulo linati, “Aliyense amene ayang’ana pa mkazi ndikumusilira iye wachita naye chigololo iye.” Ndi kulondola uko? Chabwino, ndiye, ngati mkazi adziveka yekha mwadama nadziyika yekha pamaso pa mwamuna, kodi ndi ndani amene walakwitsa pa izo? Mkaziyo ndi iye, iye anazipanga izo. Ndiko kulondola ndendende.

²¹⁶ Tsopano, iwe ukhoza kukhala woyera ngati kakombo kwa mwamuna wako. Iwe ukhoza kukhala msungwana wachichepere yemwe sunachitepo cholakwika chirichonse mmoyo mwako, kukhala namwali pamene iwe ukukwatirana ndi mwamuna wako. Koma ngati iwe umavala motero ndi kuwapangitsa amuna kuti azikuyang’ana iwe monga choncho, iye wachita chigololo ndi *iwe* kale mu mtima mwake. Wochimwa ameneyo anayang’ana pa iwe. Monga Mkristu iwe ukhoza kukhala ndi zovala zazifupi zapamwamba kwambiri mumzinda, zopambana zaubweya, koma izo ndizosayenera kwa Woyeramtima wa Mulungu kuti azivala motero.

²¹⁷ [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] O, inde, sizimabwera kwa mwana wa Mulungu.

²¹⁸ “O, ayi,” iwo amati. Chabwino, iwo amati, “Mpingo wathu. . .” Inu mwavala bwino? Iwo anati iwo anali. Iwo anali “achuma, osasowa kanthu.” Ndithudi. Bwanji, iwo anati, “Ngakhale abusa athu amatuluka atavala mwinjiro waukulu kwambiri. Kwaya yonse imatuluka itavala mwinjiro waukulu kwambiri.” Mdierekezi anadzigudubuzira pansi pake. U-hum. U-hum, ndiko kulondola. O! Hmm, hmm! Chabwino, ine kulibwino ndisaneneno zimenezo konse. Koteru, ine ndikhoza kusiya chimenecho chipite. Chabwino.

²¹⁹ O, zinthu zazikulu zonsezi! Makwaya amiinjira, makwaya olipidwa, amayenera kuwalipira iwo kuti ayimbe. Hmm.

Muyenera kumupatsa mlaliki zochuluka kwambiri kapena iye angalandire ndalama ina ya komwe angamulipire iye bwinoko pang'ono. Iye angayitanitse gulu la matrastii pamodzi ndi kuti, "Tsopano, abale, ine—ine . . . inu mwakhala achifundo kwambiri kwa ine kuno, inu mumandipatsa ine ma handirede *ambiri* pa sabata," kapena chinachake monga choncho. "Koma Mpingo wina wa Presbateria wa . . ." (Tiwutche iwo "Pentekoste" kapena uliwonse womwe uli.) "kudutsa kuno, iwo ali—iwo andilonjeza ine kuti andipatsa ine zochuluka *mwakuti*." O, mai!

²²⁰ Ndiye woyera wosawuka ali ndi chiyani? Kodi ali ndi mwayi wotani? Kodi mpingo wawung'ono wosauka wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera, kodi iwo ali ndi mwayi wamtundu wanji? Iwo sangakwanitse chirichonse chonga icho. Kotero Ambuye amangokudzutsirani chinachake pamenepo, ameni, chimene chasankhidwa ndi dzanja la Iyemwini, amachidzaza icho ndi Mzimu Woyera ndipo amamuika iye kukhala woyang'anira wamkulu pa iwo. Amamutumiza pansi . . . Iye anati, "Ine ndikukulangizani inu kuti mubwere ndi kudzagula zovala zoyera kwa iye." Baibulo linati, "Miinjiro yoyera ndi chilungamo- . . . cha oyeramtima."

²²¹ Tsopano, ine ndikukhulupirira ife . . . Tiyeni tipeze za—pafupifupi ndime ya 19 tsopano. Ine ndikukhulupirira ndi pafupifupi ndime ya 20 pomwe ife tiri, chopambana chomwe ine ndingakhoze kuwona. Eya, eya, ndipo ndikutseka pa izi. Tsopano khalani chete kwenikweni tsopano ndipo mumvetsere tsopano pamene ife tikuchita izi. Mvetserani:

Tawonani, Ine ndayima pakhomo, ndi kugogoda: ngati wina amva liwu langa, ndi kutsegula chitseko, Ine ndidzalowa mkati . . . ndipo ndidzadya ndi iye, ndipo iye ndi ine.

Kwa iye amene agonjetsa Ine ndidzampatsa kuti adzakhale ndi ine pa mpando wanga wachifumu, ngakhale monga Inenso ndagonjetsa, ndipo ndakhala pansi ndi Atate wanga pampando wake wachifumu.

Iye amene ali nalo khutu, mloleni iye amve chomwe Mzimu akunena kwa mipingo.

²²² Awa ndi amodzi mwa maneno apamwamba kwambiri amene ine ndinayamba ndawawonapo mu Chipangano Chatsopano. Ine ndikufuna kuti inu muzindikire, "Ine ndayima pakhomo ndipo ndikugogoda." Izi nthawi zambiri zimagwiritsidwa ntchito, chowerenga chowachonderera ochimwa. Ndi kulondola uko? Ife timawauza ochimwa, "Yesu ali pakhomo, akugogoda." Koma apa Iye akugogoda pa chitseko cha *mpingo* chifukwa Iye nthawi ina anayendapo ndi iwo, koma iwo (ndi bungwe lawo ndi chidziko ndi kuzizira) anali atamutulutsa Iye. Iye ali kunja kwa mpingo.

²²³ Tsopano, kumbukirani, mu woyamba wa mibadwo ya mpingo, pamene ife tikutseka, Iye anali akuyenda pakati pa

zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide (Ndi kulondola uko?), mibadwo isanu ndi iwiri ya mpingo. Ndipo pa mapeto apa, ife tikumupeza Iye kunjja kwa mpingo uti? Wa Laodikaya, mpingo wa Laodikaya. Kunja, iwo anali atamutulu- . . . atamutulutsa Iye. Bwanji, Iye anali atayima kunjja akuyesera kuti alowenso mkati. Ndi chithunzi chomvetsa chisoni bwanji! Mpulumutsi wadziko lapansi, atayima kunjja kwa mpingo womwe Iye anawugula ndi Magazi Ake Omwe. Manyazi pa iwo!

²²⁴ “Ine ndayima pakhomo ndipo ndikugogoda.” Atakankhidwira kunjja kapena atatulutsidwa, ndiyeno akuyesera kuti abwererenso mkati, akukwawa kubwerera ndipo akugogoda pakhomo. Iyi ndi mbiri yokhudza kwambiri mu Chipangano Chatsopano. Ine ndikuganiza palibe chomwe chingakhale chomvetsa chisoni kwambiri kuposa ichi, kuwona Mpulumutsi wa dziko lapansi akuchotsedwa mu mpingo Wake Womwe, m’badwo wa Laodikaya. Iye atatha kuwauza iwo zomwe iwo anali atachita, kulemera kwawo ndi chirichonse, ndi chimene iwo anali, ndi momwe iwo analiri ofunda ndi zina zotero, ndipo iwo—iwo anayenera. . . iwo. . . Iye sankayenera kuti awalavulire iwo kunjja, iwo anali atamulavulira *Iye* kunjja. Ndipo apa panali zonse za izo, akugogoda pakhomo, akuyesera kuti abwererenso mkati. Za chiyani? Kutu awapatse iwo Moyo Wamuyaya. Iwo omwewo omwe anamupha Iye pa Kalvare, Iye amayesera kuti apulumutse moyo wawo. Ndi chithunzi chomvetsa chisoni kwambiri chomwe ine ndinachiwonapo mmoyo mwanga, chomwe ndinachiganizapo konse.

²²⁵ Kuchotsedwa! Kodi Iye anachotsedwa kuchoka ku chiyani? Tsopano, mveterani, abwenzi. Ngati izi sizokhudza! Pezani chithunzi cha icho, chiloleni icho chilowerere pansu mumtima mwanu. Mpulumutsi wathu, pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye anachotsedwa mu fuko Lake Lomwe. Iye anakanidwa, Iye anachotsedwa. Dziko linamuchotsa Iye ndi kumupachika Iye. Ndipo tsopano, kuchokera ku mpingo Wake Womwe, Iye wachotsedwa. Iye sakufunidwa kulikonse, sakumusowa Iye. Iwo anali nacho chipembedzo, iwo sankamusowa Iye. Iwo anali naye papa, kodi iwo angamufunire chiyanso china Iye? Iwo ali naye bishopu wamkulu, woyang’anira wamkulu, iwo analibe ntchito ndi Mzimu Woyera nkomwe. Iwo sankawusowanso Umenewo konse. Khristu, Mzimu Woyera, iwo sankamufuna Iye. Kotero iwo ali. . .

²²⁶ Ine sindikukhulupirira iwo anangodzuka ndi kumuponyera Iye kunjja, chifukwa iwo anali asanamusowe Iye. Iwo sanamusowe Iye, chifukwa iwo anali kuyimbabe nyimbo kwa Iye. Mlaliki ankayankhulabe za Iye, kotero iwo sanamusowe Iye. Koma chidzikodziko chawo chomwe ndi bungwe lawo, kupanga bungwe, kunena, “Masiku a zozizwitsa anapita ndipo kulibe chinthu chonga *ichi* ndi *icho*.”

²²⁷ Ine ndikukufunsani inu. Chitsitsimutso chirichonse chomwe

chinayamba chabwerapo (aliyense, inu a zambiriyakale), tsopano, kutsika kudutsa kuno, mipingo iyi, chitsitsimutso chirichonse chimene chinayamba chabwerapo, a...icho nthawizonse chimabweretsedwa kunja kwa bungwe. Munthu aliyense amene anayamba konse chitsitsimutso, anali kunja kwa mabungwe. Ndipo nthawi iliyonse chi—chitsitsimutso chikayamba, iwo anali nazo zizindikiro ndi zozizwitsa za kuyankhula mmalirime ndi machiritso, ndi zina zotero monga choncho, zikuchitika. Mwamsanga pamene woyambitsa ameneyo anamwalira, ndiye iwo anawupanga iwo bungwe ndipo anapanga bungwe kuchokera mwa iwo, ndipo anapita molunjika “akufa” ndipo Mulungu sanasewere konse ndi iwo kenanso. Ndiko kulondola ndendende.

²²⁸ Ndipo apa Iye ali pa m'badwo wa mpingo wotsiriza, atayima kunja kwa chitseko, Mulungu Wamphamvuzonse. Zimenezo—Zimenezo zimaswa mtima wanga kuti ndiganizire za zimenezo. Ambuye wanga atayima kunja kwa chitseko cha mpingo Wake Womwe, atatha kukankhidwira kunja ndi chidziko ndi kuzizira ndi chipembedzo ndi kusayanjanitsika, atayima kunja kwa chitseko, akugogoda, akuyesera kuti alowenso mkati. Pamene ine ndimaganiza choncho, kanthawi kapitako, ine ndinangotsamira pa tebulo langa ndi kuyamba kulira. Ine ndimaganiza...

²²⁹ Ine nthawi zambiri ndimaganiza, pamene Yesu anali atakhala mnyumba ya Mfarisi wakale uja kumeneko, palibe amene anapereka tcheru chirichonse kwa Iye, pamene Iye anali ndi mapazi akuda. Iwo sanakumane naye Iye pakhomo ndi kumusambitsa mapazi Ake ndi kumudzaza Iye, kuchotsa ndowe ndi zinthu kumene Iye anali akuyenda; Chovala chake chikusesa mozungulira, anabweretsa kununkha kwakale kwa msewu kumene akavalo ndi zinthu zinayendapo, ndipo—ndipo anakhala ndi kununkha kumeneko pa Iye.

²³⁰ Iwo nthawi zonse ankasambitsana mapazi, iwo unali mwambo wake. Ndipo wosambitsa mapazi ankakhala pakhomo. Ndipo munthu akabwera, iwo ankamusambitsa mapazi ake, ndi kufikira pamwamba apo ndi kutenga nsapato zazing'ono zomwe zinkamukwana iye, nkuzivala izo. Ndipo iwo amadzodza mutu wake ndi ake... ndi kumupangitsa iye kununkhira bwino, ndi kutentha mkhosi mwake kuchokera ku kuwala kwa dzuwa, kupesera tsitsi lake mmbuyo. Iye amalowa mkati.

²³¹ Ndipo kulandiridwa kwa mlendo, tsopano nayi njira yomwe iwo... Imani apa miniti, Pat, ine ndikufuna kuti ndikuwonetseni inu chinachake. Umu ndi momwe iwo ankachitira, iwo ankalandira izo monga chonchi. Tsopano, ine ndikukhulupirira... Ayi, monga kuno, ine ndikukhulupirira izo ziri monga chinachake mu dongosoo ili kuno, kumulandira monga *chonchi*, mwawona, ndi kukumbatirana wina ndi mzake. Ndipo iye ankalandiridwa.

232 Koma pamene Yesu anabwera ku phwando ili, monga momwe Iye anabwera ku phwando la Chipentekoste kuno, winawake anamuphonya Iye. Iwo anali ndi chidwi kwambiri mu zochitika zawo, mabishopu ndi ena otero anali kumeneko. Yesu anayitanidwa koma palibe amene anasambitsa mapazi Ake. Ndipo apo Iye anali atakhala apo mu ngodya, iwo sanadziwe nkomwe kuti Iye anali pamenepo, ndi mapazi Ake akununkha, dothi paliponse pa Iye, wafumbi.

233 Ndipo kenako pali hule losauka lakale mu msewu limene linabwera kumeneko, iye anali ndi ndalama pang'ono chabe mthumba. Ndipo iye anayang'ana uko ndipo iye anamuwona Yesu atakhala pamenepo ndi mapazi akuda. Izo zinamuwona mtima wake. Iye anati, "Ameneyo ndi mwamuna amene anamukhululukira mkazi ameneyo machimo ake. Ameneyo ndi mwamuna amene ine ndamva kuti anachita machiritso. Chifukwa chiyani iwo sakupereka tcheru kwa Iye?"

234 Chifukwa mabishopu ndi onse a iwo anali pafupi, iwo anamutulutsira Iye kunjira. Apo Iye . . . Iwo anamuyitana Iye kuti abwere.

235 Ndipo umu ndi momwe ife timachitira. Ife timamuyitana Iye kuti abwere ku misonkhano yathu, koma ndiye pamene ife tibwera timachita Naye manyazi. "O, ine sindikanakhala ndi kumanena 'Ambuye alemekezeke.' O, ayi, apo pakhala a Jones, iwo angaganize kuti ine ndinali woyera-wodzigudubuza." Wachinyengo iwe! Uko nkulondola. "Ine ndikuwopa kuti ndingayankhule mmalirime ndipo iwo akananditcha ine 'munthu wamalirime.'" Ndiwe watsoka womvetsa chisoni!

236 Tsopano, inu kumbukirani, izi zikulowa mkati, inu mukuwona. Ndiwe womvetsa chisoni, watsoka, wosauka, wamaliseche, ndi wakhungu, ndipo sukudziwa izo.

237 Yesu atakhala pamenepo ndi mapazi osasambitsidwa. Ndipo hule la mumsewu, ine ndikutha kumuwona iye akupita, tiyeni—tiyeni tikambirane. . . mutengeni iye kwa miniti. Ine ndikukhoza kumuwona iye akupita kumusi ku sitolo, ndipo iye akuti, "Ine. . ." Ndipo misonzi inayamba kutsika pankhope yake, ndipo iye anati, "Ine—Ine sindingathe kuchita izo. Ngati—ngati—ngati ine ndingatengere zinthu izi kumtunda uko, Iye adzadziwa kumene ine ndazipeza ndalama izi. Iye akudziwa momwe ine ndazipezera izo, koma ndi chinthu chokha chomwe ine ndiri nacho."

238 Ndizo zonse zomwe Iye akufuna. Ndizo zonse zomwe Iye akufuna. Mukuwona? Iye sasamala. Inu mungobwera, "Palibe chirichonse mmanja mwanga chomwe ine ndabweretsa."

239 Koteri iye anatenga mafuta ena ndipo iye anawabweretsa iwo. Ndipo iye anafika pamwamba apo ndipo iye anaganiza, "O, ngati ine ndikanakhoza kungomuwona Iye!" Ndipo kenako iye analowa mkati ndipo anakhala kuseri kwa chitseko penapake.

240 Ndipo, ayi, iwo anali asanamulandire Iye. Koteru iye anatenga bokosi la alabastero ndi kulitsegula ilo ndi kumupaka iye. . . pa mapazi Ake, ndi kuyamba kusambitsa mapazi Ake. Ndipo iye anayamba kulira, "O, akuyenera kukhala Iye. Ndi Ameneyo amene ndakhala ndikumuwerenga nthawi zonse mu Baibulo. Ine ndikudziwa Iye akhoza kuchizindikira icho." Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa. . . Ndi madzi okongola bwanji a mapazi Ake, misozi ya kulapa ikugwera pa mapazi Ake. Iye analibe nsanza kuti apukutire mapazi Ake ndi iyo, koteru iye anafikira pamwamba ndipo anatenga tsitsi lake. Zingongo zokongola zonse zinamasuka, misozi ikutsika pankhope yake monga choncho. Iye anasambitsa mapazi Ake, ndipo kamodzi mu kanthawi iye amakhoza, "*kupsopsona*," kupsopsona mapazi Ake, kusambitsa mapazi Ake monga choncho.

241 Yesu ali ndi mapazi akuda, ndipo popanda aliyense wopereka tcheru ku izo. Ndipo lero Iye akunyamula dzina loyipa ngati woyera wodzigudubuza, *chinachake chimzake* monga icho, ndipo anthu alibe ndulu kuti amuyimire Iye!

Mtanda wopatulika uwu ine ndiunyamula,
Mpaka imfa idzandimasule ine,

Nditenga njira ndi onyozeka ochepa a Ambuye,
Ine ndayamba nawo ndi Yesu, O Ambuye,
mundidutsitse ine.

242 Mundidutsitse ine, Ambuye, ziribe kanthu zomwe izo zingatengere, Ine ndiri nawo, monga Yakobo, mtsamiro, mwala. Kodi izo zimapanga kusiyana kotani? Zomwe Iye anandichitira ine!

243 Ndipo hule wosauka uyu pamenepo, akufuula, akulira. Ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, apa panayima Simoni, munthu wamkulu yemwe anamupangitsa Iye kuti abwere pansu, anati, "Uhm, uhm, uhm, uhm! Izo zikusonyeza ngati Iye ali mneneri kapena ayi, Iye akanadziwa mtundu wa mkazi yemwe iye anali." Wachinyengo ameneyo!

244 Koteru iye atamaliza. . . Ndipo Yesu sanasunthe mapazi Ake, Iye anangokhala ndi kumamuyang'ana iye ndi kumuwona iye. O, ine ndikuzikonda izo. Izo sizinthu zazikulu zimene ife timachita, ndi zinthu zazing'ono zimene ife timazisiya osazichita nthawizina. Iye anamuyang'ana iye, amangomuyang'ana iye atakhala pamenepo. Panalibe amene anali kupereka tcheru kwa Iye; potsiriza, iye mmenemo akulira ndi kusambitsa mapazi Ake, kukhala ngati akupereka tcheru kwa izo, anakopa tcheru cha anthu. Ndipo Iye anangomuyang'ana iye, osanena konse mawu.

245 Simoni wakaleyo atayimirira kumbuyo uko, anati, "Uhm! Inu mukuwona ngati Iye ali mneneri kapena ayi, sichoncho inu? Ndinakuuzani inu! Ndinakuuzani inu! Ngati Iye anali mneneri, Iye akanadziwa yemwe mkazi ameneyo anali. Inu mukuwona,

ife tinali mpingo wawukulu kuno, inu mukuwona, ife tikudziwa, koteru. Ife tikudziwa Iye si mneneri, Iye akanadziwa izo.”

²⁴⁶ Atatha iye...Iye atamaliza, misozi iyo ya kulapa ikuyenderera pankhope yake, anasambitsa mapazi a Yesu. Iye...Ine ndikukhulupirira Iye anamverera kutsitsimuka pang’ono.

²⁴⁷ O Mulungu, ine ndikanakonda ndikanakhala kumeneko! Ine ndikanawatsuka iwo kenanso. Inde, bwana.

²⁴⁸ Mnyamata, kodi mkazi sangakhale ndi nthawi yovuta kupukuta mapazi ndi tsitsi lake lero? Iye angayenere kuti ayime ndi mutu wake kuti achite izo, kuti apeze tsitsi lokwanira kuti apukute iwo. Inde, bwana, analidula ilo lonse.

²⁴⁹ Koma pamenepo, mapazi a Yesu, panalibe amene amapereka... (zovuta), atakhala wamanyazi, fungo limenero pa mapazi Ake. Iye anamusambitsa Iye. Iye atatha—Iye atamaliza, Iye anayang’ana kwa iye ngati kuti akunena, “Chabwino.”

²⁵⁰ Anayang’ana uko, anati, “Simoni, Ine ndiri ndi china choti ndinene kwa iwe. Iwe unandiyitanira Ine kuno, ndipo iwe sunakumane ndi Ine pakhomo. Iwe sunandipatse Ine madzi kuti ndisambitse nawo mapazi Anga. Iwe sunadzoze mutu Wanga pamene Ine ndinalowa mkati, kudzachotsa ziwawu za dzuwa pa Ine. Iwe sunandipatse Ine konse kupsopsona kondilandira pamene Ine ndimalowa. Koma mkazi wosauka uyu,” (O, mai.) “wakunja uyu, hule pa msewu, iye analibe madzi kuti asambitsire mapazi Anga ndipo iye wawasambitsa iwo ndi misozi yake. Iye analibe chirichonse choti apukutire nacho iwo, koteru iye anatenga tsitsi lake, iye wawapukuta iwo. Iye wapsopsona mapazi Anga mosalekeza. Tsopano Ine ndikufuna kuti ndinene kwa iwe: machimo ake, amene anali ochuluka, akhululukidwa kwa iye.” Ndiko kulondola, sananene chirichonse chokhudza ake. “Machimo ako, amene ali ochuluka, akhululukidwa.”

²⁵¹ Ndipo lero pamene Yesu, atayima kunja kwa chitseko cha mabungwe Achipentekoste, mabungwe a Baptisti, Mabungwe a Methodist, akuyesera kuti abwerere umo ndi pentekoste kachiwiri, ndipo anthu akumulambalala Iye. Inu mutatha... chidzikodziko chanu ndi zinthu zamukankhira Iye kunja kwa mpingo, Iye akuyimirira, akuyesera, akulirira kuti abwererenso mkati kachiwiri. Ndipo, o, ndi chinthu chomvetsa chisoni kwambiri chomwe ine ndinayamba ndachiwonapo mmoyo mwanga. Sankamusowa Iye! Iye, kunja, akugogoda, akuyesera kuti alowe mkati. Ndicho chinthu chomwecho chimene Iye akuyesera kuti achite. Chifukwa chiyani? Chifukwa chiyani? Iye anali kunja.

²⁵² Iwo sanamuponyere Iye kunja. Iwo ankayimbabe za Iye, ankalalikira za Iye, koma sanamusowe Iye pamaso pawo. Ndiko kulondola. Iwo ankapitirirabe. Chifukwa chiyani?

Iwo anali owonapafupi. Iwo ankayang'ana pa chimango chawo chachikulu. Iwo anali olemera. Iwo ankayang'ana pa bungwe lalikulu lomwe iwo anali nalo, kuyesera kuti alimange ilo, akupeza mamembala ambiri kuti abwere, ndipo iwo sanamusowe Iye. Ayi, ayi. Iwo sanasowe kuyankhula mmalirime. Iwo sanawasowe aakulu, mauthenga amphamvu a Mulungu Yemwe amadula mpaka kumtima ndi kudula mtima, kung'amba zinthu za mdziko lapansi ndi kukusendani inu ngati kachidutswa ka chimanga. O, iwo. . .

²⁵³ Ngati inu mukanalalikira monga choncho kutchalitchi kwawo, iwo akanakutulutsani inu kunja. Ndipo umo ndi momwe Mzimu Woyera unkalalikirira. Yesu anati, "Inu m'badwo wa amamba! Inu—inu njoka muudzu!" Ndipo Yohane anatero, nayenso, ndipo amuna aakulu odzozedwa, nthawizonse ankawasenda khungu lawo iwo. Uko nkulondola.

²⁵⁴ Koma iwo sankamusowa Iye, chifukwa iwo analibe Chimenecho. Mukuwona? Kotero iwo anali ndi kanthu kenakake kakang'ono ka maluwapaluwa kakuwasisita iwo pamsana, ndipo anati, "Inu mungojowina, lembani dzina lanu pomwe apa, ndipo—ndipo ife tidzakutengani mu umembala wanu. Ndipo inu mupite mukatenge pepala lanu ku mpingo winawo ndipo ife tidzakulandirani inu, ndi—ndi zina zotero. Tsopano, cholonjeza chanu chizikhala chochuluka bwanji chaka chirichonse?" Inu mukuwona, ndizimenezotu, "Olemera, osasowa kanthu." O! Koma inu mukusowa chinthu chachikulu kwambiri ndipo simunachipeze Icho, Yesu atayima panja akuyesera kuti alowemo ndi pentekoste.

²⁵⁵ Kodi inu mukuganiza kuti chingachitike ndi chiyani usikuuno mu mpingo wa Methodisti ngati Mzimu Woyera ukanagwera pa mpingowo ndipo iwo nkuyamba kufuula, kudumpha, kuyankhula mmalirime ndi kumachita ngati oledzera. . . gulu la anthu oledzera? Bwanji, Mso—Msonkhanowo ungaponyere mpingo wa Methodisti umenewo kunja kwa Msonkhanowo. Inu mukudziwa zimenezo. Chingachitike ndi chiyani mu mpingo wa Baptist ngati izo zingachitike? Chinthu chomwecho. Achipentekoste? Bwanji, alipo ambiri a iwo, izo zinachitikanso chimodzimidzi. Ndithudi. Inde, bwana, iwo sangapirire ndi zamkutu zimenezo. Iwo angati, "Bwanji, iwo anawononga ngakhale makalapeti athu atsopano." U-hum, ndithudi. Mai! Mai! Ndi gulu lomvetsa chisoni bwanji lomwe iwo ali. Ndiko kulondola.

²⁵⁶ Chabwino, chabwino, Iye anali nawo iwo poyamba, Iye anayenda nawo iwo pakati pa zoyikapo nyali zisanu ndi ziwiri zagolide. Ndipo apa pali yankho: zipembedzo ndi zinthu zawo za chidziko, mabishopu awo, makadinolo, ndipo chidzikodziko chawo chonse, chinali chitamutulutsira Iye kunja ndipo iwo sanamusowe nkomwe Iye. Ndipo mpingo. . .

²⁵⁷ Tsopano, kodi ife tichite chiyani kuti timubwezeretse Iye mkati? Ngati Iye ali kunjwa kwa mpingo wa Pentekoste tsopano, ife tichite chiyani kuti timubwezeretse Iye mkati? Kodi izo zidzatengera voti yogwirizana pamodzi ya anthu kuti amubwezeretsenso Iye mkati? Kodi izo zidzatengera kusankha papa watsopano, kadinolo watsopano? Kapena mwina izo zidzatengera—zidza—zidzatengera kudzukapo kwa chipembedzo chatsopano. Izo sizidzatengera izo konse! Izo sizidzachita konse izo. Chipembedzo chatsopano sichingachite izo, watsopano—a—a—a—a—kadinolo watsopano sangachite izo, m’busa watsopano sangachite izo, mlaliki wolipidwa bwino sangachite izo. Palibe chirichonse mdziko lapansi chomwe chingachitike koma inu nokha. Kodi ife timamutengera chotani Iye mkati? Osati mwa voti. Ayi, bwana. Sitimamuvotera Yesu kuti abwerere, chifukwa Iye sadzalowa.

²⁵⁸ Apa izo—Apa izo ziri, “Ngati munthu aliyense ati amve Liwu Langa ndi kutsegula chitseko.” Tsopano, ife tikudziwa chimene khomo liri ndiye. “Ngati munthu aliyense ati atsegule chitseko, amva Liwu Langa.”

²⁵⁹ Osati—osati “Ngati mpingo uliwonse...Ngati bungwe lirilonse...” Ayi, bwana. Iye samachita ndi iwo, iwo ndiakufa ndipo anapita kuyamba nkuyamba. Iye amadana nazo izo, Iye nthawizonse ankadana nazo. Iye anati Iye amadana nazo izo! Ndipo Iye amadana nazo izo panobe usikuuno!

²⁶⁰ “Koma ngati munthu aliyense,” munthu aliyense wa Methodist, munthu aliyense wa Baptist, munthu aliyense wa Presbateria, kapena munthu aliyense wa Katolika, munthu aliyense wa Church of God, munthu wa Nazarene, munthu wa Pentekoste. “Munthu aliyense yemwe ati adzamve Mawu Anga ndi kutsegula chitseko, Ine ndidzalowa mkati ndi kudzadya naye iye ndipo iye ndi Ine.” Umenewo ndiye uthenga wopita kwa mpingo wa Pentekoste. Osati kuyesera kutsitsimutsa bungwe la Chipentekoste, koma kutsitsimutsa Mdalitso wa Chipentekoste muntima wa munthu aliyense. Ndiyo njira yokhayo. “Ndipo ine ndidzadya naye iye, ndipo iye, Ine.”

²⁶¹ Kodi mthenga amatani ku mpingo... uthenga kwa mpingo umatiphunzitsa ife chiyani ndiye, kuphunzitsa—kutiphunzitsa ife? Osati kukula mu Mzimu. Ayi, bwana. Kugwa kwa Mzimu, ife timakhala ndi kugwa nthawi zonse. Amethodi... A—amithenga ku mpingo ndi uthenga ku m’badwo uliwonse wa mpingo unatsutsa zachipembedzo. Uthenga uliwonse ku mpingo, mpingowo umakhala ukugwa mosalekeza ndipo sukanamvera ku Icho. U—uthenga kwa mpingowo sunkalabadira zipembedzo. Ndipo izo zinapanga Akhristu osakanizidwa, otchedwa choncho, ndiko kulondola, omwe sankadziwa kanthu za Mulungu kapena Mzimu Woyera. Ndizo zowona monga ine ndayimira pa nsanja pano usikuuno. Mamembala abwino ofunda, ongoti alavulidwe kutuluka mkamwa Mwake.

²⁶² Paulo anachenjeza, Amitundu anali nthambi. Tsopano, ine ndikufuna ena a inu, ngati inu mungatero, kuti mutembenezire ku Aroma, mutu wa 11, ndime ya 15 mpaka ya 27, basi kuti inu mukhoze kulemba izo, inu nonse. Ndiyeno, pokhala kuti tachedwa, Ine ndinena chobwereza ichi kwa inu tsopano ndisanachoke, chifukwa ndicho. . . Tsopano, Aroma, ngati inu mukufuna kuzilemba izo, 11:15 mpaka twente- . . . mpaka 27. Paulo anawauza iwo, anawauza, akuyankhula kwa Amitundu kumeneko, Aroma, iye anati, “Ngati Mulungu. . .” Tsopano, mvetserani pamene ife tikutseka mibadwo ya mpingo! Paulo anati, “Ngati. . . Mulungu sanasunge mtengo wa azitona wapachiyambi, koma anaudula iwo chifukwa cha kusakhulupirira.”

²⁶³ Ndi kulondola uko? Nchiyani chinawapangitsa iwo kuti adulidwe? Chifukwa iwo anakana Pentekoste. Ndi kulondola uko? Pa Tsiku la Pentekoste iwo anawuseka ndi kuwuchitira mwano Mzimu Woyera.

²⁶⁴ Pamene Yesu anali pano pa dziko lapansi, Iye anati. . . Iwo ana—anamutcha Iye, “Belezebule,” anati “Iye anali mdierekezi,” ndipo “Iye ndi wam’bwebwe,” china chirichonsecho.

²⁶⁵ Iye anati, “Ine ndakukhululukirani inu chifukwa cha izo, koma pamene Mzimu Woyera udzabwera inu musati mudzayankhule mowutsutsa Iwo; chifukwa inu mukayankhula mowutsutsa Iwo, izo sizidzakhululukidwa konse kwa inu.”

²⁶⁶ Ndipo kumbukirani pamene Yesu anatuma ophunzira Ake, “Kuti asapite kwa Amitundu.” Ndi kulondola uko? “Koma pitani mmalomwake kwa nkhosa zotayika za Israeli.”

²⁶⁷ Kodi iwo anadzitsutsa bwanji okha? Pa kuchitira mwano Mzimu Woyera, kuwutcha Mzimu wa Mulungu “chinthu chosayera.” Anamupanga Iye choseketsa pamene iwo ankavina mu Mzimu, ndi zina zotero, pa Tsiku la Pentekoste. Mzinda womwewo, iwo anawunyozza Iwo, Tito anawapha iwo mmenemo ndipo magazi awo anathamangira ku njira ya kuchipata. Iwo amadya ana awo omwe, ndi chirichonse, mzaka zana zomwezo. Ndipo ndiko kulondola. Limodzi mwa mafuko aakulu kwambiri padziko lapansi linakhala lotsikitsitsa, ndipo anamwazikana ku iliyo- . . . mphepo zinayi za dziko. Chifukwa chiyani? Kusakhulupirira! Ndipo icho chinali chitsa choyambirira, mtengo wapachiyambi, Israeli.

²⁶⁸ Ndipo Paulo sakunena pamenepo? Ndani ali ndi Lemba pomwe apo? Mwalipeza ilo, Pat? Imirira ndipo uwerenge kuyambira pa ndime ya 15 mpaka ya 27. [M'bale Pat awerenga Aroma 11:15-27—Mkonzi.]

[Pakuti ngati kutayika kwa iwo ndiko kuyanjanitsa kwa dziko lapansi, kodi kulandiridwa kwa iwo—kwa iwo kudzakhala kotani, koma moyo kuchokera kwa akufa?]

[Pakuti ngati chipatso choyamba chiri chopatulika, mtanda wonsewo ndi wopatulikanso: ndipo ngati muzu uli wopatulika, momwemonso ziri nthambizo.]

[Ndipo ngati zina mwa nthambi zake zathyoledwa, ndipo iwe, pokhala mtengo wa azitona wakuthengo, unamezanitsidwa mwa izo, ndipo ndi izo ugawana nawo za muzu ndi mafuta a mtengo wa azitona;]

[Usadzitama motsutsa nthambizo. Koma ngati iwe udzitama, iwe sunyamula muzu, koma muzu ukunyamula iwe.]

[Iwe udzati ndiye, Nthambizo zinathyoledwapo, kuti ine ndikhoze kumezanitsidwamo.]

[Chabwino; chifukwa cha kusakhulupirira iwo anathyoledwapo, . . .]

Mvetserani, “kusakhulupirira.” Chabwino, pitirirani.

[. . .ndipo iwe uyima mwa chikhulupiriro. Usati ukhale wodzikuzwa, koma kuopa:]

[Pakuti ngati Mulungu sanalekerere nthambi zachirengedwe, dziwa kuti iye sadzakulekereranso iwe.]

[Tawonani kotero ubwino ndi kuopsya kwa Mulungu: pa iwo amene anagwa, kuopsya; koma kwa iwe, ubwino, ngati iwe uti upitirirebe mu ubwino wake: ngati siutero iwenso udzadulidwa.]

[Ndipo iwonso, ngati iwo sakhalabe mu kusakhulupirira, adzamezanitsidwamo: pakuti Mulungu ndi wothejera kuwamezanitsanso iwo kachiwiri.]

[Pakuti ngati iwe unadulidwa kuchokera ku mtengo wa azitona umene uli wakuthengo mwa chilengedwe, ndipo unamezanitsidwa motsutsana ndi chilengedwe ku mtengo wabwino wa azitona: mochuluka motani nanga izi, zomwe ndi nthambi zachilengedwe, zingamezanitsidwe mu mtengo wawo womwe wa azitona?]

Hmm!

[Pakuti ine sindikufuna, abale, kuti inu mukhale osadziwa za chinsinsi ichi, kuti inu mungadziyese anzeru mu kudzikweza kwanu komwe; kuti khungu pang’ono linachitikira Israeli, kufikira chidzalo cha Amitafu chitafika.]

[Ndipo kotero Israeli yense adzapulumutsidwa: monga izo zalembedwera, Padzatuluka ku Ziyoni Mpulumutsi, ndipo adzachotsa kupanda umulungu mwa Yakobo:]

[*Pakuti ili ndi pangano langa kwa iwo, pamene ine ndidzachotsa machimo awo.*]

269 Kodi inu mukumvetsa Izo? Paulo anati, “Ngati Israeli akanabwera kuno ndi kuwona zizindikiro apa za Mzimu Woyera, ndipo anadulidwapo. . .” Kumbukirani, chifukwa iwo anakana uthenga wa Paulo (ubatizo mu Dzina la Yesu, kulapa ndi ubatizo mu Dzina la Yesu, zizindikiro ndi zodabwitsa zikutsatira wokhulupirira), ndipo iwo anaukana Iwo. Ndipo iwo anati, “Tawonani, ife tikutembenukira kwa Amitundu.” Ndi kulondola uko?

270 Tiyeni tiwone, ine ndikukhulupirira panali pa . . . kumene iwo anawatcha koyamba Akhristu, kunali ku Efeso, kapena, Antiokeya.

271 Tsopano—tsopano, ngati—ngati mtengo woyamba unali woyera, nthambi zake zinali zoyera, mtengo wapachiyambi, ndipo chifukwa iwo sanakhulupirire Uthenga wa Chipentekoste womwe Paulo anali kulalikira (Kodi ndi choncho?), Mulungu anawadula iwo ndi kutenga mtengo wa azitona wakutchire (omwe anali Amitundu, ife) ndipo anatimezanitsa ife kuti ife tikhale moyo kuchokera mwa ntha- . . . thunthu la mtengo umenewo.

272 Tsopano, ndi mochuluka bwanji mu tsiku lino pamene ife tikukana Uthenga wa Chipentekoste umene watsika kudutsa mmibadwo ya mpingo, ndi mochuluka bwanji momwe Mulungu ali wothejera kuti awuchotse mtengo wakale wakutchire uja kwa iwo, mulimonse, ndi kulola winawo kulowamo? Chifukwa iye adzawakana Iwo, chifukwa cha kusakhulupirira. Tsopano lumikizani izo ndi phunziro la mmawa uja. Inu mukudziwa pamene ife tikuyima tsopano, sichoncho inu? Ife tiri pa nthawi yotsiriza pa kuchotsedwa kwa Mpingo wa Amitundu, Mkwatulo wa Iwo; ndi kuperekedwa kwa Mzimu Woyera kuti ubwere pa Ayuda, ndipo Yesu kuti adzipangitse Yekha kudziwika, kuti asindikize handiredi ndi forte foro sauzande aja. Ndi inu apo. Akuwubwezeretsa mtengo wapachiyambi (kubwerera mu Dalitso) kulowa mu Israeli kachiwiri.

273 Yesu sadzayima kunja kwa chitseko chako ndi kumagogoda nthawi zonse. Pali nthawi yomwe Iye adzatopa nazo ndipo adzatembenukira kutali, ndiyeno inu mudzapanga kugogodako koma inu simudzamupeza Iye. Bwerani pamene nthawi ikadalipo. Bwerani pamene pali kugogoda. Inu musati mulekerere ndi china chirichonse kupatula ubatizo wa Mzimu Woyera monga iwo anawupeza pa Pentekoste, ndi mtundu womwewa wa ubatizo wa madzi, zinthu zomwezo zimene iwo ankachita kumeneko. Musati mulole chirichonse chiyike chirichonse mumtima mwanu kupatula chimenecho.

274 Tsopano, kwa inu abwenzi anga Achikatolika, ndiloleni ine ndikuuzeni inu chinachake, inu mumakhulupirira mwa

namwali Maria. Namwali Maria, pokhala mayi wa Yesu Khristu, anayenera kuti apite ku Pentekoste ndi kukadzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndipo iye anachita ngati munthu woledzera. Iye anali pakati pa iwo handiredi ndi twente, anali nawo ubatizo wa Mzimu Woyera, akuyankhula mmalirime ndi kumachita ngati mkazi woledzera kunjā uko, pansi pa Mzimu wa Mulungu. Ndipo ngati namwali Maria anayenera kuti achite zimenezo kuti alowe mu Ulemerero, kodi inu mulowa chotani mwa Iwo, chirichonse pambali pa izo? Taganizani za izo. Uko nkulondola.

²⁷⁵ Abaptisti . . . Mlaliki wa Baptist uyo kumbuyo kuno akufuna atsimikize kuti zanenedwa kwa Abaptisti nawonso. Izo ndi za aliyense, sindikusasamala kuti ndi ndani.

²⁷⁶ Kotero kungojowina mpingo ndi kunena kachikhulupiriro, ndi kumapita kutchalitchi Lamulungu lirilonse mmawa, sizingakuchitireni inu kachidutswa kamodzi ka ubwino. Inu mukungomupangira chabe chipongwe Mulungu. Kulibwino mukhale Mkristu weniweni kapena musakhale chirichonse nkomwe. Mukhale mwina wotentha kapena wozizira. Mukhale kunjā . . . Chifukwa inu simungathe kukhala . . . Inu simunayiwonepo mbalame yakuda yoyera, inu simunayambe mwamuwonapo munthu woledzera wosaledzera, inu simunayambe mwamuwonapo woyera-wochimwa. Ayi, inu simutero, iwo samazipanga izo. Inu ndinu mwinamwake wodzadzidwa ndi Mzimu Woyera ndipo Mulungu akukhala mwa inu, kapena inu simuli konse. Inu—inu muli kapena inu simuli.

²⁷⁷ Kotero chifukwa chake inu mukuyenera—inu mukuyenera kukumbukira kuti Yesu wayima pa khomo lanu, ndipo kumbukirani lonjezo la Mulungu pano kuti Iye adzatero mmasiku ano, chifukwa cha chiyani? Kukana. Nchiyani chinapangitsa Israeli kuti adulidwe, mtengo wapachiyambi? Chifukwa iwo anakana Uthenga wa Chipentekoste wa Paulo. Ndipo kodi inu mukukhulupirira kuti uwu ndi m'badwo wa mpingo wotsiriza? Baibulo linanena chomwecho! Ndipo nchiyani chikuti chichitike ndi iwo? Iwo adulidwa chifukwa chokana Uthenga wa Chipentekoste, ndipo kenako Mulungu adzabwereranso kachiwiri kwa Ayuda.

²⁷⁸ Ndipo Israeli yense ndiye adzapulumutsidwa, chifukwa Iye adzawatenga iwo ngati fuko, osati ngati mmodzi payekha. Koma kwa inu ndi ine ndi mmodzi payekha, chifukwa Iye anabwera kwa Ayuda . . . Machitidwe, mu Bukhu la Machitidwe, Iye anabwera kwa Amitundu kuti adzatenge “anthu kuchokera mwa Amitundu kwa Dzina Lake,” Mkwatibwi Wake. “Anthu,” mmodzi apa, mmodzi apo, wina cha apa, ndipo Iye amachita nafe monga aliyense payekha, ndipo mosasamala za mtundu, chikhulupiriro, kapena mtundu. Iye amachita nafe monga munthu payekha, ndi maluwā Ake omwe Iye adzawayike pa guwa Lake. Koma monga Ayuda, Iye nthawi zonse ankachita ndi Israeli ngati fuko, iwo ndi fuko la anthu, fuko Lake.

279 Ndine wokondwa usikuuno kuti ife tiri ndi Uthenga uwu. Ndipo ndine wokondwa kuti inu munapezekapo, ndipo kupezeka kwanu kwakhala kuli koyamikiridwa kwambiri ndi ine. Ine ndiri woyamika kwa Mulungu Wamphamvuzonse chifukwa cha Iye pondilola ine ndiwone zomwe ine ndaziwona, ndi kukhala wothekera kuti ndipereke ku mpingo uno, ndipo tsopano Icho chachoka pamtima panga. Kwa nthawi yaitali Mzimu Woyera umachita pa mtima wanga, ine sindinathe kuwukutumulira Iwo kutali, ine ndinangoyenera kuti ndizipita nawo Iwo.

Pali zinthu ziwiri zomwe ine ndinamverera kutsogoleredwa kuti ndichite.

280 Kupita ku Shreveport, Louisiana, kukakumana ndi M'bale Moore. Ndipo mkazi wanga wakhala pamenepo akhoza kukuuzani inu. Kwa masabata angapo ine ndinatsala pang'ono kulira, "Ine ndikufuna kupita ku Shreveport. *Chifukwa chiyani?*" Ndipo aliyense anali uko ku Shreveport akudziwa *chifukwa* chake tsopano. Iwo anali asanawonapo kapena kumva chirichonse chonga icho. Alaliki akubwera kuchokera kulikonse, Achibaptisti ndi mitundu yosiyana. Munthu mmodzi anati iye anayamba, anayika dzanja lake pa bokosi la ayezi, ndipo Mzimu Woyera unabwera pa iye ndi kuti, "Pita ku Shreveport, Louisiana, akakuuza iwe kumeneko choti uchite." Unamuuzwa iye dzina langa ndi komwe angapeze. . . Anati, "Iye akakuuza iwe zoyenera kuchita."

281 Ine ndinati, "Dziwe ndilotseguka pansu pa masitepe. Inu mukusowa ubatizo wa Mzimu Woyera." Ndipo pamenepo. . .

282 Kotero zinthu monga zimenezo, anthu akuyankhula, ndi—ndi maulosi ndi zinthu za kuneneratu zinthu zomwe zinachitika pakati pathu pomwe.

283 Ndiye ine ndinati, "Ine ndiyenera kupita ku Jeffersonville ndi kukalemba buku ili, chifukwa ine sindikudziwa ndi nthawi yayitali bwanji ine ndiyenera kuti ndikhale kuno. Koma ngati ine ndingazifotokoze Izi ndi kuzilemba Izo, ndikadzapita ine Mawuwu adzakhalabe ndi moyo." Ine ndiri ndi mbiriyakale yolembedwa yomwe idzalowe mu bukhuli. Ndipo ine ndabwera kuno kuti ndichibweretse icho pamaso pa mpingo kuti ndipeze kudzodza kwa Mzimu Woyera, chifukwa ine sindimadziwa zinthu izi inemwini. Ndizo zowona. Ndizo mu Dzina la Ambuye, ndizoona, "Ine sindimazidziwa iwo."

284 Tsopano ine ndikumverera womasulidwa, ine ndikumverera kuti Mulungu watibweretsera ife Uthengawu. Ine ndikukhulupirira kuti ife tiri kumapeto kwa ulendo, Ine ndikukhulupirira kuti ora liri pano kuti kuwonetseredwa kwa Mulungu kupangidwe kudziwika pakati pathu. Ndipo ine sindikudziwa izo zidzakhalala nthawi yayitali bwanji, koma oralo layandikira kwambiri.

²⁸⁵ Iye tidzakhala tikufunafuna wamkuluyo kuti adzauke. Iye akhoza kubwera mu tsiku langa, iye akhoza kubwera mu tsiku laling'ono, ine sindikudziwa. Iye akhoza kukhala pakati pathu tsopano, ife sitinganene. Mzimu Woyera uli pano kuti utitsogolere ife mpaka nthawi imeneyo, ndiye pamene mtsogoleri uyu adzatitengera ife kumeneko iye adzakhala apobe wodzodzedwa ndi Mzimu Woyera; E—Eliya adzatero, ndithudi, izo zidzafika. Koma iye adzakhala mtsogoleri yemwe adzatembenusa mitima ya ana, kapena, mitima ya ana kubwerera ku Uthenga wa Atate, kubwerera ku Uthenga wa Atate wathu Wakumwamba pa Tsiku la Pentekoste pamene Iye anatsanulira Mzimu Wake.

²⁸⁶ Chimene chingwe chaching'ono chija, ine ndinabweretsa icho pafupi basi momwe ine ndikanathera mwa mbiriyakale ndi Baibulo, ndi kusonyeza kuti chinthu chimenecho chabwera kudutsa mmibadwo ya mpingo, ndipo ndi zomwezo lero, kusonyeza kuti zipembedzo ndi themberero pamaso pa Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti izo zakhazikika mmalingaliro mwanu, mwa Baibulo, mwa machitidwe a atumwi, mwa mbiri yakale ndi zonse. Izo . . .

²⁸⁷ Ndipo palibe nthawi imodzi yomwe Mulungu anaupangapo bungwe Mpingo Wake. Mayi wa mipingo yopangidwa bungwe ndi mndandanda wamaudindo wa Roma Katolika. Mpingo wa Roma Katolika, ndi mayi wa mabungwe. Ndipo mwamsanga pamene chitsitsimutso chiyambika mu gulu lirilonse la Chiprotestanti, iwo amabwerera mmbuyo momwe ndi kukachita chinthu chomwecho. Ndipo Baibulo linati, “Iye anali hule. Ndipo iye, iye anali nawo ana aakazi omwe anali mipingo yochokera kwa iye.” Iwo amayenera kukhala akazi, kuti akhale timahule. Ndi uyo apo. Kotero ife tikukhazikitsa . . .

²⁸⁸ Koma Iye ananenanso izi, “Musawope, kagulu kankhosa, ndi chifuniro chabwino cha Atate wanu kuti akupatseni inu Ufumu.” Kotero mulole ife tonse, pa tsiku limenero, inu a Methodist, a Baptisti, chirichonse chomwe inu muli, “Aliyense amene adzatsegule chitseko, Ine ndidzalowa ndi kudzadya naye limodzi.”

²⁸⁹ Mulole ife tiwerengedwe, abale anga, alongo anga, mulole ife tiwerengedwe mu gulu lankhosa laling'ono limenero pa tsiku limenero. Mulole ife tikhale gawo la kagulu kankhosa kamene kakhala kakuyembekezera pamene Iye akubwera, pamene Iye akubwera kuti adzakatenge iko padziko lonse. Pakuti mkwa—Mkwatulo udzakhala wa dziko lonse. “Padzakhala awiri pa kama, Ine ndidzatenga mmodzi; awiri mmunda, ndipo Ine ndidzatenga mmodzi.” Zikuwonetsa kuti kudzakhala usiku mbali imodzi ya dziko lapansi ndi masana mbali inayo, mwawona. Kotero, ndi, “Awiri adzakhala pa kama, awiri adzakhala mmunda,” mwawona, “Ine ndidzatenga m'modzi wa alionsewo.”

²⁹⁰ Ndipo monga ine ndinanena mmawa uja, inu mudzakhala mukukwera mu msewu ena mwa masiku awa, mukuyankhula kwa amayi, ndipo inu mudzayang'a pozungulira, iwo adzakhala atapita. Inu mudzakhala pa tebulo, ndi kumamwa wanu—khofi wanu kapena kudya kadzutsa wanu, kapena—kapena chinachake, ndipo chinthu choyamba inu mukudziwa, inu mudzayang'ana pozungulira ndipo adadi palibepo. Ndiko kulondola ndendende. Ukubwera, ndipo ife sitikudziwa nthawi yanji. Koma nkhani yake ndi yakuti, pamene iyo yatha ndiye iyo yatha, ndiyeno palibe china chirichonse chomwe inu mungachite za izo. Inu mukuti, "Ine ndamva zimneezo kwa nthawi yaitali." Koma inu mudzamva izo nthawi yanu yotsiriza. Uko nkulondola. Izo zidzachitika chifukwa Ndi Mawu a Ambuye. Ndipo, kumbukirani, Kodi izo zalepherapo nthawi iliyonse kudutsa mausiku eyiti omwe ine ndakhala ndikulalikirawa? Koma zomwe—zomwe Yesu ananena apa, zafika pochitika, ndipo anazichita m'badwo wa mpingo uliwonse ndendende basi.

²⁹¹ Ndipo ife tikuwuwona m'badwo wa mpingo uwu uli mu izo, ndipo pa ora lomwelo. Ngakhale mmawa uja, pofanizira anamwali, nthawi yomweyo imene namwali wogonayo... Tsopano, inu kumbukirani, Baibulo linanena kuti namwali wogona...pamene mfuwu unamveka, "Tawonani, Mkwati akubwera," kudza kwa Ambuye, kulalikirira kwa Mawu. Ndipo kenako chinachitika ndi chiyani? "Nthawiyo yayandikirira, mabomba a atomiki ndi zonse zakonzeka," alaliki akuthamanga mmisewu ndi kuyamba kufuula Uthenga.

²⁹² Ndipo mwamsanga pamene iwo atero, mpingo waukulu ndiye, namwali wogona, anati, "Ah, chabwino, ife takhala tiri Achipresbateria nthawi yayitali, mwina ife tingaphunzire ndi kupeza. Inde, inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira ife tikusowa Mzimu Woyera." Ndipo iwo akulemba mabuku ndi chirichonse za Iwo tsopano, kuyamba. Ndipo iwo anati, "Kodi inu mungatipatseko ife wina wa Iwo?"

Ndipo iwo anati, "Ayi, ife tiri nawo wongotikwanira tokha."

²⁹³ Koteri pamene iwo anapita kuti akapeze Mzimu Woyera, anapita kukapemphera, monga mipingo, mipingo yayikulu yabwino ikuchitira lero, mabungwe. Pamene iwo anapita kukapeza Mafuta, Mkwati anabwera. Koteri iwo akuyesera kuti awupeze Iwo pakali pano, mipingo yayikulu, mabungwe, misonkhano yayikulu yapadziko lonse yokhudza Iwo mu—mmipingo yopangidwa bungwe, kumati, "Ife tikuyenera kubwerera ku Dalitso la Chipentekoste. Ife tikuyenera kukhala ndi ochiritsa auzimu mu mpingo. Ife tikuyenera kukhala ndi oyankhula ndi malirime. Ife tikuyenera kukhala ndi omasulira malirime. Ife tikuyenera kukhala ndi mphatso zonse zauzimu izi mu mpingo wathu, ndipo ife basi tikuyenera kuyambitsa misonkhano ndi kuyamba kuzichita izo." Iwo akukhala ndi makhonsolo, ayamba kuchita izi. Pamene iwo akupita kukachita

zimenezo, ndi nthawi yomweyo imene Mkwati akubwera ndipo anatenga iwo amene anali nawo Mafuta mu nyali zawo, ndipo anachokapo.

²⁹⁴ Ndiye iwo anabwera, ndipo chinachitika ndi chiyani? Iwo anaponyedwa mumdima wakunja (nthawi ya Chisautso Chachikulu) kumene kudzakhala kulira ndi kubuma ndi kukukuta kwa mano, pamene Mkwatibwi ali Kumwamba. O, mai!

²⁹⁵ Ndiye kumapeto kwa zaka zitatu ndi theka zimenezo, Iye adzabwera monga Yosefe anachitira ndi kudzazizindikiritsa Yekha kwa abale Ake. Izo zidzapangitsa kulira ponseponse, ndipo iwo adzati. . . Iwo adzalekanitsa mabanja awo, ndipo adzalira ndi—ndi kuti, “Kodi Inu munazipeza kuti zipsera zimenezo?” Ndipo—ndipo anamubaya. . . iwo amene anamubaya Iye adzamuwona Iye, ndipo Iye adzazizindikiritsa Yekha kwa abale Ake.

²⁹⁶ Tsopano Iye akuyesera kudzipangitsa Yekha kudziwika ku Mpingo Wake, ndipo iwo amukankhira Iye kunja. Ndipo Iye akuyimabe, akugogoda, akuti, “Kodi pali winanso mmenemo? Yemwe angati atsegule ndi kundilola Ine kuti ndilowe ndi kuyankhula ndi inu?”

²⁹⁷ O, ndine wokondwa, wothokoza kwambiri kuti pafupifupi. . . zaka zambiri zapitazo, pafupifupi zaka twente-eyiti zapitazo, ine ndinamverera kugogoda kumeneko pa mtima wanga. Ndipo ine. . . Iye analowa mkati, ndakhala ndikudya naye Iye ndipo Iye ndi ine kuyambira nthawi imeneyo. Ndipo ine ndinalandira Mdalitso wa Chipentekoste, ndinalandira Mzimu Woyera.

²⁹⁸ Ndinabatizidwa mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha machimo anga, nthawi yokhayo yomwe ine ndinayamba ndabatizidwapo mmoyo mwanga, kamodzi. Pamene ine ndinali mnyamata wamng’ono, panalibe amene akanakhoza kundiiza ine kuti kuli Milungu itatu. Ayi, inu simukanatha kuzikanikizira izo kukhosi kwanga. Inu simungazipereke izo kwa aliyense amene amadziwa chirichonse. . . amadziwa chimene Mulungu ali. Uko nkulondola. Kotero pamene ine ndinabatizidwa. . . mlaliki wa Baptisti anandibatiza ine. Ine ndinati, “Ine ndikufuna kubatizidwa mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.” Dr. Roy E. Davis anandibatiza ine mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu pamene ine ndinali mnyamata. Mukuwona? Uko nkulondola. Kotero ine—ine ndinazikhulupirira izo, ine ndakhalabe nazo, ndipo ine ndikudziwa icho ndi Choonadi. Ndi Mawu Amuyaya a Mulungu. Uko nkulondola. Uko nkulondola.

Ndine wokondwa kuti ine ndikhoza kunena
ndine mmodzi wa iwo.

Ndine mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,

Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wa iwo;
 Ndine mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wa iwo.

Ngakhale anthu awa angakhale osaphunzira,
 Kapena kudzitamandira za kutchuka kwa
 chidziko,

Onse alandira Pentekoste wawo,
 Kubatizidwa mu Dzina la Yesu;
 Ndipo akunena tsopano, konsekonse,
 Mphamvu Yake ikadali yomweyo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wa . . .

²⁹⁹ Kodi ndinu okondwa? Ngati inu muli, kwezani mmwamba
 dzanja lanu.

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wa iwo;

Inu mukadzakhala Ake inu mudzakhala pamwamba pa
 tchimo lonse, mu Dzina la Yesu Khristu.

Bwera, m'bale wanga, ufune mdalitso uwu
 Lomwe litsuka mtima wako ku tchimo,
 Lomwe liyambitsa mabelu achimwemwe
 kulira

Ndipo lidzauyikabe moyo wanu pamoto;
 O, likutentha tsopano pansu mumtima
 mwanga,

Oh, ulemelero ku Dzina Lake,
 Ndipo ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena
 ndine mmodzi wa iwo.

Oh, mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wa iwo; (Aleluya!)

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
 mmodzi wa iwo.

Anasonkhana m'chipinda cham'mwamba,
 Onse akupemphera mu Dzina Lake,
 Iwo anabatizidwa ndi Mzimu Woyera,
 Ndipo mphamvu ya utumiki inabwera;
 Tsopano chimene Iye anachita kwa iwo tsiku
 limenero

Iye achita kwa inu chimodzimidzi,
 Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena . . .

³⁰⁰ Tsopano tiyeni tigwirane chanza, kutsogolo, kumbuyo, ndi
 pozungulira.

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo;

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo.

Oh, mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo;

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo.

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo;

Mmodzi wa iwo, mmodzi wa iwo,
Ndine wokondwa kuti ndikhoza kunena ndine
mmodzi wa iwo.

Kodi simukusangalala kuti ndinu mmodzi wa iwo?
[Osonkhana akuti, “Inde! Ameni! Aleluya!”—Mkonzi.] Ine
ndimazikonda izo. Gulu laphokoso!

Shh! Shh! [M’bale ayankhula mmalirime, m’bale wina
atanthauzira—Mkonzi.]

³⁰¹ Momwe ife tikukuthokozerani Inu, Atate, chifukwa cha
ubwino Wanu ndi zifundo kwa ife, osayenerafe. Kuti tiganize
kuti Inu mukhoza kutsimikizira Uthenga Wanu tsopano,
Ambuye, munawalonjeza anthu. Ine ndikupemphera, Mulungu,
kuti zifundo Zanu zikhale pa iwo.

³⁰² Ngati pali ena pano amene sakumudziwa Iye ngati
Mpulumutsi, mukufuna kuti mumupeze Iye pakali pano
mmitima yanu ngati Mpulumutsi, kodi inu mungayime
pamapazi anu pamene ife tikukupemphererani inu? Iye ananena
kuti Iye adzatero . . . anapanga Uthenga uwu pamenepo ndipo
Iye amafuna kuti atsimikizire Mawu Ake kwa inu. Ngati pali
ena pano omwe sakumudziwa Iye ndipo sanalandire Mzimu
Wake, Iye akuyankhula kwa inu.

³⁰³ Chabwino, uyo kumbuyo uko. Kodi inu mungangoyimirira
pamapazi anu, m’bale? [M’bale ayankhula—Mkonzi.] Iye
akufuna kuti abatizidwe mu Mzimu Woyera, ndi choncho,
m’bale? Mulungu akudalitseni inu. Imani pomwe inu muli. Kodi
alipo wina angafune kuti ayimirire ndi kunena, “Ine ndikufuna
kuti ndikhale wobatizidwa mwa Mzimu Woyera”? Mulungu
akudalitseni inu, m’bale. Mulungu akudalitseni inu. Ndizo
zabwino. Ingoyimirirani pamapazi anu. Basi mungoyimirirabe
pamapazi anu. Kodi pangakhale wina amene angafune
kulandira Mzimu Woyera ndi kubatizidwa, mungakonde
kukumbukiridwa mmapemphero athu pompano, kubatizidwa

ndi Mzimu Woyera? Kodi pali wina, ine ndisanati ndinene zomwe ine ndikukonzekera kutero, angafune kuti ayimirire ndi kuphatikizidwa?

O, kodi inu mungati muwerengedwe ngati mmodzi wa khola Lake? (Kodi inu mungachite izo?)

Khalani opanda banga mkati, khalani mukuyang'anira ndi kuyembekezera kuwoneka kumeneko kuti mudzakuwone; Iye akudza kachiwiri.

³⁰⁴ Iye akudza kachiwiri. Kodi inu mungafune kukhala mdani Wake kapena inu mukufuna kuti mukhale mwana Wake? Mulungu wokwiya mmawa umenewo, palibe china koma Magazi a Yesu ndi omwe Iye ati adzawazindikire. Iye sadzatero... Umembala wa mpingo wanu sudzakhala kanthu kwa Iye. Palibe china koma Magazi!

O, kofunika ndi kuyendererako
Kumene kumandiyeretsa ine monga chipale;

Pang'onopang'ono.

Palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa,
Si china koma Magazi a Yesu.

Chingatsuke tchimo langa ndi chiyani?
Si china koma Magazi a Yesu;
Nchiyani chingandipange ine wamphumphu
kachiwiri?

Si china koma Magazi a Yesu.

O, kofunika ndi kuyendererako
Komwe kumandiyeretsa ine monga chipale;
Palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa,
Si china koma Magazi a Yesu.

[M'bale Branham akung'ung'udza *Sichina
Koma Magazi—Mkonzi.*]

Si china koma Magazi a Yesu;
Ichi ndi chilungamo changa chonse,
Si china koma Magazi a Yesu.

Pali wina?

O, ndi wofunika . . .

Palibe chomwe chingayime, m'bale, mlongo. Dziko lapansi likumira, ilo lapita!

. . . ngati chipale;
Palibe kasupe wina yemwe ine ndikumudziwa,
Si china koma Magazi a Yesu.

³⁰⁵ Pang'onopang'ono, Teddy, ngati iwe ungatero, "Pali Kasupe Wodzaza Ndi Magazi, wotengedwa kuchokera mmitsempha ya Emmanueli."

³⁰⁶ Tsopano, abwenzi, inu omwe mwayimirira pamapazi anu mu—mukuyesera kulandira kukoma kwa Ambuye Yesu. Baibulo lomwelo lomwe limatiuza ife kuti zinthu izi zikanadzachitika, linazifikitsa izo pochitika ndendende basi momwe Iye analonjezera izo. “Tsopano, lonjezo,” anatero Petro, “liri kwa inu ndi kwa ana anu ndi kwa iwo omwe ali kutali, ngakhale kwa ambiri amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.”

³⁰⁷ Inu munayimirira chifukwa mukufuna madalitso a Mulungu pa inu. Ndipo monga wantchito Wake, ine ndikupemphererani inu, ine ndipemphera kuti Mulungu akupatseni inu ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndipo ine ndikudabwa ngati inu mungachite izi mumtima mwanu, ngati muli owonamtima, ngati inu mungapange lonjezo ili kwa Mulungu: “Mulungu, ine, kuyambira pano, ndayimirira pamapazi anga, kufunafuna ubatizo uwu wa Mzimu Woyera, Ine ndidzapemphera mosalekeza ndi kudikirira mpaka Inu mutandidzaza ine ndi Mzimu Woyera.” Kodi inu mupanga lonjezo limenero kwa Mulungu pokweza manja anu? “Ine ndipemphera mosalekeza, mosalekeza, mpaka Inu mutandidzaza ine ndi kukoma ndi ubwino wa Mzimu.”

Ine ndikupereka pemphero langa kwa inu tsopano pamene ife tikuweramitsa mitu yathu:

³⁰⁸ Atate Athu Akumwamba, iwo ndi zikho za Kukhalapo Kwanu. Iwo akudziwa kuti Mawu awa ndi owona chifukwa iwo ndi Anu. Iwo akudziwa kuti iwo aperekedwa ndi Mzimu Woyera, chifukwa iwo ndi Mawu a Mulungu. Ndipo iwo atsamikizika kuti iwo akukusowani Inu, kuti iwo akusowaa kukoma kwa Mzimu Woyera mmiyoyo yawo kuti uwapatse iwo mphamvu yogonjetsa. “Ndipo iwo adzalandira mphamvu yochokera Kumwamba,” alandire mphamvu kuti akhale moyo wa Chikhristu, kuti alandire mphamvu yoti azigonjetsera mayesero. Monga nyimbo yomwe ife timangoyiyimbayi, “Iwo anasonkhana mchipinda chapamwamba ndipo amapemphera mu Dzina Lake, iwo anabatizidwa ndi Mzimu Woyera ndipo mphamvu ya utumiki inadza.” Ndizo zomwe iwo akufuna, mphamvu ya utumiki kuti ibwere pa iwo.

³⁰⁹ Ine ndikukupemphani Inu, Atate, monga wantchito Wanu, monga Inu munawawona iwo akukweza manja awo, iwo apanga lonjezo kwa Inu ndi lonjezo kuti iwo sadzaleka konse, iwo sadzalisiya ilo pambali, koma iwo apemphera mpaka Inu mutawadzaza iwo, Ambuye, ku gawo lokhutitsa la Kukhalapo Kwanu Koyera mmoyo wawo. Ine ndikupereka pemphero langa mmalo mwawo, Ambuye, monga wantchito Wanu, kuti iwo adzazidwe ndi Mzimu Woyera. Ambuye, ine ndikupemphera kuti iwo asatuluke mu tchalitchichi mpaka izo zitachitika, kuti adzakhala pomwe pano mpaka moyo uliwonse utadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Perekani izi, Ambuye.

³¹⁰ Inu ndinu Mulungu, Wamphamvuzonse, Inu munawonetseredwa mthupi kuti mudzachotse machimo a dziko lapansi. Inu munawuka tsiku lachitatu, munakwera Kumwamba. Ndipo Inu muli pano usikuuno, pakati pathu, ndipo mu dzina la Mzimu Woyera. Ndipo ife tikupemphera, Atate, kuti Inu, Ambuye wathu wofunika, mudzadze aliyense wa iwo ndi Inu Mwini Nokha. Ndipo mulole iwo akhale mda—mdalitso ku Ufumu Wanu ndi mu dziko lomwe likudzalo. Ndipo tsiku lina pamene Inu potsiriza mudzafika kumapeto kwa ulendo, mwina iwo akhoza kukhala lero, ife sitikudziwa nthawi imene izo zidzakhale. Koma mulole ine ndikhoze, Ambuye; ndikhale wowerengedwa limodzi ndi omwe adzapita mu Mkwatulo. Mulole awa akhale omwe ati apite mu Mkwatulo. Mulole munthu aliyense, Kukhalapo Kwaumulungu ndi onse amene adzazidwa ndi Mzimu, omwe ali a Mulungu, adzapite mu Mkwatulo.

³¹¹ Atengereni awa mkati usikuuno, Atate. Iwo ndi Anu tsopano, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³¹² Tsopano ine ndikufuna nonse a inu amene mwayimirira pafupi ndi anthu awa, amene muli nawo Mzimu Woyera, mudzuke, ikani manja anu pa iwo.

... Kasupe wodzaza ndi Magazi,
 Ochokera mmitsempha ya Emanueli,
 Momwe ochimwa amadziponyera pansu pa
 kusefukirako,
 Ataya mawanga a zolakwa zawo zonse.
 Ataya mawanga a zolakwa zawo zonse,
 Ataya mabanga a zolakwa zawo zonse;
 Ndipo ochimwa amadziponyera pansu pa
 kusefukirako,
 Ataya mawanga a zolakwa zawo zonse.
 Mbala pa kufa anakondwa pakuwona
 Kasupe uja mu tsiku lake;
 Ndipo apo mulole ine, ngakhale woyipa monga
 iye,
 Nditsuke machimo anga onse.
 Nditsuke machimo anga onse,
 Nditsuke machimo anga onse;
 Momwe ochimwa amadziponyera pansu pa
 kusefukirako,
 Nditaye machimo anga onse.

³¹³ Tsopano kwezani manja anu kwa Mulungu ndipo mungomupatsa Iye matamando. Nenani, “Zikomo Inu, Ambuye. Ine ndikudzuka pamapazi anga, ine ndikupatsani Inu matamando. Ine ndikuthokozani Inu chifukwa cha madalitso Anu, chifukwa cha ubwino Wanu, ndipo chifukwa chondipatsa

ine ubatizo wa Mzimu Woyera.” Zikomo Inu, Ambuye! Zikomo Inu, Ambuye! Tikukuthokozani Inu, wokondedwa Mulungu, potipatsa ife. . . Inu mumasunga lonjezo Lanu, Inu munanena chomwecho. Ife tikukukhulupirirani Inu.

³¹⁴ Kodi inu simuli osangalala? Nenani, “Ambuye alemekezeke!” Teddy, ndiloleni ine. . . imodzi yokha, “Ife timapeza anthu ambiri omwe sangathe kumvetsetsa. . .” *Izi Ziri Ngati Kumwamba Kwa Ine.*

Ife timapeza anthu ambiri omwe sangathe
kumvetsetsa

Chifukwa ife tiri okondwa ndi omasuka;
Tawoloka Yordano kupita ku Dziko lokongola
la Kenani,

Ndipo izi ziri ngati Kumwamba kwa ine.

O, izi ziri ngati Kumwamba kwa ine,

O, izi ziri ngati Kumwamba kwa ine;

O, tawoloka Yordano kupita ku Dziko
lokongola la Kenani,

Ndipo izi ziri ngati Kumwamba kwa ine.

O, pamene ine ndikhala wokondwera, ine
ndimayimba ndi kufuula,

Mdirekezi samakhulupirira Izo, ine
ndikuwona;

Koma ndadzazidwa ndi Mzimu, palibe
kukayika,

Ndilo lomwe liri vuto ndi ine.

O, ndicho chomwe chiri. . . Kumwamba kwa
ine, (Tamandani Mulungu!)

O, izi ziri ngati Kumwamba kwa ine;

Ndawoloka Yordano kupita ku dziko
lokongola la Kenani,

Ndipo izi ziri ngati Kumwamba kwa ine.

³¹⁵ Kodi izo sizikukupangitsani inu kusangalala? Zabwino. Gwiranani chanza ndi winawake, ndikuti, “Ambuye alemekezeke!” Izi ziri ngati Kumwamba, Ambuye.

Tenga Dzina la Yesu nawe,
Mwana wachisoni ndi watsoka;
Ilo lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,
Litenge Ilo kulikonse upita.

Dzina lofunika, O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba;


Dzina lofunika, O kukoma kwake!

Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
cha Kumwamba.

Pa Dzina la Yesu kugwada,

Kugwa modzilambatitsa pa mapazi Ake,
 Mfumu ya mafumu Kumwamba tidzamuveka
 Iye korona,
 Pamene ulendo wathu udzatha.
 Dzina lofunika, O kukoma kwake!
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba;
 Dzina lofunika, O kukoma kwake! (Ndi
 lokoma bwanji!)
 Chiyembekezo cha padziko ndi chimwemwe
 cha Kumwamba.

Tsopano, mwakachetechete, ndi mitu yathu
 yoweramitsidwa:

. . . Dzina la Yesu nthawi zonse,
 Monga chishango ku msampha uliwonse;
 Pamene mayesero akuzungulirani inu,
 Ingopumani Dzina Loyera ilo mu pemphero.
 Dzina lofunika, O kukoma kwake! 

60-1211E M'badwo Wa Mpingo Wa Laodikaya
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org